


# NCHIFUKWA CHIYANI

## IFE SITIRI CHIPEMBEDZO?

 Chamwayi kuti ndabwereranso pa guwa kachiwiri patatha pafupi, ine ndikuganiza, pafupifupi miyezi itatu nditasowapo. Agologolo anali ndi nthawi yovuta, chomwechonso ine ndinali. O, ndi kutakasuka, ngakhale, tsopano, ndipo ine ndikumverera ngati ndilowe mu utumiki kachiwiri. Ndipo tikuyembekezera tsopano kuti ndiyambe sabata likudza ili, Lachitatu likudza ili usiku, kwa—chitsitsimutso momwe muno mu Kachisi. Ndipo ngati Mulungu alola, ine ndakhala ngati, Ambuye andilonjeza ine mtundu wosiyana ndi watsopano wa utumiki. Ndipo ngati Iye akondweretsedwa kuti achite motero, ine ndikuyembeza kuti ndiyambe iwo—mtundu wa utumiki umenewo sabata likubwerali, pano pa Kachisi, mwa malo oyamba.

<sup>2</sup> Ndiyeno ine ndiribe misonkhano yokonzedweratu, koma basi ku Australia ndi New Zealand ya Januwane akubwera uyu. Ndiyeno M'bale Osborn akuyitanira msonkhano wupalimodzi umene ine ndinakhala ngati ndinamulonjeza iye kuno nthawiyina kale, mu Tulsa, koma mtsogolopo pang'ono, koma ife sitiri otsimikiza za izo panobe.

<sup>3</sup> Izo zinali zabwino ndithudi, M'bale Jeffreys, kufika pogwirana nanu chanza kumbuyo kuno, ndiponso kuti ndimumve mnyamata wanu akuyimba nyimbo ija, ndi inu mukuyimba chida. Ine ndimakhala ngati ndimazikonda zimenezo, bambo ndi mwana. Kodi inu simumakonda zimenezo? “Kumulerera mwana mu njira imene iye ayenera kuyendamo.” Ndiko kulondola, Bambo Guenther, inu—inu mukudziwa kuti ndiko kulondola, nonse a inu. “Kumulerera mwana mu njira imene iye ayenera kuyendamo, ndipo pamene iye afika pokula icho sichidzachoka.” Ndipo ndizo zooni. Zikhoza kukhalapo nthawi zimene iye akhoza kuchoka kwa icho, koma icho sichidzachoka kwa iye, mwaona. Icho chidza—icho nthawizonse chidzakhala ndi iye. Kuphunzitsa koyambirira uko ndi chirichonse chimene iye waleredwera kuti azichita, icho chidza—icho ndithudi chidzakhala ndi iye. Tsopano izi ziri. . .

<sup>4</sup> Ine ndinakomana naye M'bale Jeffreys kunjira uko, ndipo ine ndinati, “M'bale Jeffreys. . .” Ine ndinaganiza, inu mukudziwa, ine nthawizonse ndine wokondwa kuwona aliyense wa abale anga odzacheza muno, koma usiku woterowu kuti m'bale wodzacheza abwere! Uno ndi usiku wa anthu basi amene

amabwera ku Kachisiyu, pemphero basi, chitsitsimutso ichi, usiku wake ndi uno. Ife tikufuna kutenga usikuuno, ndi mawa mmawa, ndi mawa usiku, basi pa zimene ife timakhulupirira pano pa Kachisi, kuti—kuti tizibwereze izo kachiwiri. Ife tiri nazo zikhulupiriro zina zosamvetseka ndithu, zachirendo kwambiri, koma mwinamwake kapena mwina ife timazipeza izo mu Baibulo ili. Izo zimawoneka kuti ziri mmenemo bwinobwino.

<sup>5</sup> Ndipo tsopano ngati pakanati pakhale m'bale wachirendo kapena mlongo mkati, yemwe ali wa—chipembedzo chinachake, kapena—kapena wosagwirizana nazo, yemwe wangokhala mkati mu pa izi usikuuno, ife tikufuna kuti inu mudziwe kuti inu muli olandiridwa mwangwiwo. Onani, inu muli olandiridwa basi monga inu mungakhoze kukhalira. Koma tsopano ine ndikuyembekeza. . . Ndipo ife timazipanga izi mwaukali ndithu. Kotero ngati—ngati izo ziwoneka kuti inu simukugwirizana nazo izo, chabwino, tsopano, ndipo inu muchite zimenezo monga ine ndimachitira pamene ine ndikudya mkate wanga wa zipatso. Ndipo pamene ine ndikudya mkate wa zipatso, umene uli womwe ine ndimawukonda, ine nthawizonse, pamene ine—pamene ine ndikudya mkatewo, ngati ine ndigunda mu njere, ine sindimautaya mkatewo, ine—ine ndimangoitaya njereyo ndi—ndi kumangopitirira kumadya mkatewo. Kotero, kapena monga kudya nkhuku. Tsopano, nonse a inu mumayikonda nkhuku, onani. Ndipo pamene inu mugunda fupa, inu simumasiya, inu mumangopita molambalala fupalalo ndipo mumangopitirira kumadya nkhuku. Chabwino, ndimo momwe inu mutachitire usikuuno, zimene ine ndikunena pano, inu basi. . . pamene inu mugunda chinachake, inu muti, “Tsopano, ine—ine basi sindi. . . Ine ndikungokhala mu izi ngati Chiphunzitsa cha mpingo waung'onowu kwa misonkhano itatu yotsatira iyi, iwo akungokhala ngati akubwereza zimene iwo—zimene iwo amakhulupirira, ndi kupitanso pa izo.”

<sup>6</sup> Ndipo njira yokha imene inu mungakhozere pafupifupi kumupanga munthu kuti akhulupirire Izo, ndiyo kuwongololera Izo pachimake molimba chotero mpaka kuti iwo ayenera kuti adziwe kuti Ndicho chinthu chimene chiri cholondola. Ndiyo njira yokhayo imene inu mungapangire izo kumatirira. Ndipo monga ngati mzanga wa ine, Bambo Woods yemwe ine ndakhala ndiri naye, ngati—ngati iwe ungokhomera mkati msomali nulowa mwaheka, ndipo bolodi liri lonse losalimba, mphepo ligwetsera ilo pansu posakhalitsa ndithu, koma iwe uyenera kuwukhomerera iwo mkati ndi kuwupanga iwo kugwira molimba. Kotero tsopano ngati ine nditi ndipange izi mwa mwano kwenikweni pa malo ena awa, ndipo kwa inu alendo usikuuno amene muti mukhalepobe, ine sindiri—ine sindiri kuyesera kukukankhirani inu kumbali, ine ndiri kungoyesera kuti ndiwongolere pachimake kwa mpingo uwu zimene ife timakhulupirira. Nonse mukumvetisa izo tsopano

mwabwino kwenikweni, nenani “ameni.” [Osonkhana anena “Ameni!”—Mkonzi.] Chabwino, ndizo—ndizo zabwino. Ndipo ine ndazichotsa izi mmanja anga. Ndiyeno—ndiye. . . Iwo akujambula izi, ndi zina zotero, kuti kanthawi kena ngati iwo atafuna kuti apeze ndiye chimene ife tiri kuyima nacho kwenikweni, ndi amene ali maziko amene ife tiri kuyimapo, zojambulidwa izi zidzanena izo. Ndiyeno ife timachita izi mwakuwirikiza kulikonse, chifukwa pali anthu atsopano amene amabwera muno ndipo—ndipo ife timapita patsogolo. Ndipo tsopano ife sitikhala okhoza kuti tipitemo kachiwiri mu Ziphunzitso za mpingo zonse, koma basi zina za izo zimene ife tikufuna kuti—kuti tiyankhulepo. Ndipo tsopano Lachitatu usiku, ngakhale, kuyamba. . .

<sup>7</sup> Tsopano, Lolemba ndi Lachiwiri, ine ndikupita kutali kuti ndikapemphere, kukonzekera msonkhano wa machiritso. Ndipo inu mukhoza kufika pa mafoni, kapena chirichonse chimene inu mukufuna kutero, ndipo bwerani nawo aliyense yemwe inu mukumufuna kutero, chifukwa cha chitsitsimutso chikubwera ichi. Ndipo, muwawuze iwo kuti asabwere mwa changu, tsopano. Osati abwere, kuti, “Chabwino, tsopano ine ndithamangira mkati ndi kukapempheredwa usikuuno, ndipo mawa usiku ndizo zonse. . .” Inu musati muchite zimenezo. Inu mubwere mkati ndi kumvetsera kwa kanthawi, chifukwa ife tikufuna kuti titenge nthawi yathu ndi kuyala Mawu amenewo mwapafupi kwambiri mwakuti Mdierekezi sadzakhoza ngakhale ndi kachidutswa kakang’ono kamodzi ka chipinda koti azisunthamo konse. Ndiyeno pamene inu mulola chikhulupiriro chanu kuyenderera mpaka ku mapeto ake, mpaka inu mutayamba kukhulupirira, ndiye mulole chikumbumtima chanu chiyambe kuchita, ndiye chikhulupiriro cha Mulungu chidzayikira izo kumbuyo, ndiye inu muzipitirira patsogolobe. Mwaona? Chifukwa chikhulupiriro chanu sichichita mochuluka kwambiri; chikumbumtima chanu chiyenera kusunthira mu dera limene chikhulupiriro chanu chikusunthirako, ndiyeno chikhulupiriro cha Mulungu chimasunthira mmbuyo ndi kutsimikizira izo zonse. Mwaona? Koma ngati chiri chikhulupiriro chanu, “O, inde, ine ndachita izo pakali pano”; ndipo ngakhale chikumbumtima chanu chikugudubuzikira mmbuyo kuno, chikunena, “Ine ndikudabwa ngati izo ziti zigwire ntchito pa ine.” Izo—izo sizichita icho bwino pomwepo. Mwaona? Kotero ife tikufuna uwu kuti ukhale msonkhano weniweni wa machiritso. Ndipo ine ndisanatengere aliyense kupita mu zipinda ndi zina zotero, kwa machiritso, kapena mautumiki atsopano awa, ine ndikufuna kuti iwo amvetse kwenikweni chimene iwo akudzera mmenemo. Kotero ingokumbukirani, ndipo mubwere mudzatichezeze ife, ndipo ife tidzakhala okondwa kukhala nanu inu.

<sup>8</sup> Tsopano, kumbukirani tsopano, mmawa, ife tikhala

tikupitirizabe ndi Chiphunzitso cha mpingo, ndipo mawa usiku mwa njira yomweyo. Tsopano, ndinu olandiridwa kuti mubwere, ndipo aliyense akhoza kubwera. Ndife nthawizonse okondwera kumuwona aliyense. Koma tsopano izi usikuuno zangolunjikidwa kwa anthu amene ali a pa Kachisi pano, amene—omwe aleredwa mu Chiphunzitso ichi. Pakuti, kunja mminda, minda ya ulaliki, ife timangotenga Ziphunzitso zaulaliki wachikhazikitso zenizeni za Mmalemba. Koma pano pa Kachisi, ife tiri nawo malingaliro athu omwe ndi zikhulupiriro zathu zomwe, monga—monga—monga mpingo, ndipo ndizo zomwe tati tipitemonso usikuuno.

<sup>9</sup> Ndipo ife tisanati titsegule Mawu Ake odalitsidwa, kodi ife sitingati tingoweramitsa mitu yathu kwa mphindi ya pemphero.

<sup>10</sup> Mulungu Wamphamvuzonse ndi wamphamvu kwambiri, Amene, dziko lisanayambe konse kuzungulira pa atomu yoyamba, Inu munalali Mulungu. Inu simunasinthe kachidutswa. Ndipo pamene palibe maatomu enanso oti ayigwire iyo, ndipo palibenso dziko loti ligwirizidwe, Inu mudzakhala mukanali Mulungu. Ndinu wa nthawizonse, ndipo kuchokera ku nthawizonse, Ndinu Mulungu. Inu munalibe konse chiyambi cha masiku kapena mathero a moyo, Inu mudzakhala nthawizonse. Ndipo, Atate, Inu pokhala wopandamalire, ndipo ife amalire, ndiye ife tikupempha chifundo Chanu Chaumulungu, Mulungu, pozindikira kuti mzimu wathu uwu ndi woti ulumikizane mu Umuyaya kuchokera mu chinthu cha nthawi ichi kupita mu Umuyaya. Chotero, Ambuye, ife tiri pano kuti tifufuze pa chipulumutso chathu, kuti tiwone momwe ife tikuyimira pamaso pa Mawu Anu, ndi kuti tiwone komwe ife tiri mu zotichitikira zathu. Kodi ife tikukhala icho chimene chiri chokondweretsa kwa Inu? Kodi mzimu wathu ukuchitirana umboni ndi Mzimu Wanu? Ndipo kodi kuphunzitsa kwathu kukuchitirana umboni ndi Baibulo ili? Ndipo, Atate, mulole ife tifufuze zonsezo, mwapafupi, mu misonkhano itatu yotsatira iyi imene ikubwera. Perekani izo, Ambuye.

<sup>11</sup> Dalitsani abusa pano, madikoni, matrastii, ndi osonkhana onse, anthu amene amabwera ku mpingo uno. Chiyambireni masiku anga pano, Ambuye, alipo ambiri, ambiri amene ine sindiwadziwa ngakhale maina awo kapena kumene iwo amachokerako, koma ine ndikutsimikiza kuti Inu mukudziwa zonse zokhudza iwo. Ndipo ife tiri pano chifukwa cha cholinga chimodzi chimenecho usikuuno, Ambuye, kuti tiyanjane pozungulira Mawu olembedwa. Ndipo tipatseni ife Mzimu Woyera mu miyoyo yathu, kuti ife tikhoze kukhala mwamtendere ndi mwabwinobwino ndi mwa kuwopa Mulungu, ndipo kuifufuza miyoyo yathu ndi Mawu Anu. Perekani izo, Ambuye.

<sup>12</sup> Ndipo mu nyumba ino usikuuno, Ambuye, alipo abale anga a zigawo zosiyana za—za mpingo. Ndipo, Ambuye, ine ndiri woyamikira kwambiri kuti iwo ali pano kudzachita chiyanjano.

Mwinamwake ife tikhoza kusagwirizana pa mfundo zazing'ono za ziphunzitso. Koma mu mfundo imodzi yayikulu yofunika iyo, ife tikuyima ngati abale olumikizana patsogolo pamene, O Mulungu, mulole izo zilimbikitse chathu—chijanyano chathu, ndi chathu... ndipo zilumikizo za chisomo cha Mulungu ndi chikondi zikhale pa ife molemerera. Tsopano, pozindikira, Ambuye, kuti iyi ndi ntchito yochuluka kwambiri kuti munthu ayichite, chifukwa ife tiri nawo pano pansu pa kusinkhasinkha, usikuuno, kopita kwa miyoyo imene ili yomka ku Muyaya. Kotero ife tikupemphera kuti Mzimu Woyera ulowe kumene mu Mawu, ndipo ziyale Izo ndi kuzifotokoza Izo mwa njira Yake Yomwe, kwa ife, zinthu zimene Iye akanakhala nazo kuti ife tizidziwe. Perekani izo, Ambuye. Ndipo pamene zitatu... nthawi za msonkhano zatha, mulole ife tipite monga mpingo wolimbikitsidwa, monga olumikizana palimodzi, kuti tikayike mitima yathu ndi zolinga zathu zonse palimodzi, ndi mbadwa zimzathu za Ufumu wa Mulungu, ndi kusunthira patsogolo monga sizinachitikirepo kale.

<sup>13</sup> Ine ndikufuna ndikuthokozeni Inu, Ambuye, pano mu Kukhalapo kwa mpingo ndi—ndi kwa anthu amene ali pano, kuti Inu munandipatsa ine tsopano masabata angapo a kupuma kwabwino. Ine ndikumverera modabwitsa usikuuno chifukwa cha Kukhalapo Kwanu ndi dalitso Lanu. Ndipo, O Mulungu, ife tikupemphera chifukwa cha m'bale pano, m'bale wathu yemwe akupita kutsidya kwa nyanja, kutali uko mu maiko awo a mdima, akhatikhathi, kumene moyo wake umene ukhala ngati chandamale. Ndipo, O Ambuye, mdalitseni M'bale wathu Jeffreys pamene iye akupita, ndi mwana wake wamwamuna, ndi mkazi wake, ndipo mpatseni iye kuwonjezekera kwakukulu. Mumulole iye akacheke mabowo kupyola mu mdima mpaka Kuwala kwa Uthenga kukawalire kutali ndi motambalala. Timvereni ife, Atate, pakuti ife tikupempha pempho ili mu Dzina la Ambuye Yesu, Mwana Wanu. Amen.

<sup>14</sup> Tsopano, usikuuno, powerenga mu Baibulo langa laling'ono la Scofield. Ine ndangodutsa kumene usinkhu wa zaka makumi awiri ndi zisanu, posakhalitsapa. Ndipo ine ndikhoza kuliwerengabe ilo, koma izo zimathima ndithu, kotero ine ndadzipezera magalasi owerengera pamene ine ndiri kuwerenga. Ndipo ine ndiwona momwe izo ziti zigwirire ntchito usikuuno, kwa nthawi yanga yoyamba. Tsopano ine ndiri nawo maphunziro monga awa, oti, *Uyenera Mpingo...* O, zinthu zambiri, ngati ife tingakhoze kufika kwa izo. Chimodzi cha izo, *Nchifukwa chiyani ife timatchedwa Mpingo? Nchifukwa chiyani ife sitiri chipembedzo? Chifukwa chiyani—chifukwa chiyani ife timakhulupirira mu chitetezero Chamuyaya cha moyo wa wokhulupirira? Nchifukwa chiyani ife timawatsutsa alaliki aakazi? Nchifukwa chiyani ife timabatiza mwa kumiza? Ndipo kodi Mpingo udzapita kupyola mu Chisautso?* Ndi ambiri

a maphunziro amenewo pano, ine ndikuganiza ine ndiri nawo khumi ndi asanu kapena khumi asanu ndi atatu a iwo, kwa mausiku otsatira pang'onowa.

<sup>15</sup> Kotero ine ndikuganiza usikuuno, kuti ndiyambe nazo, kuti ndiyambitse nazo, izo zikuwoneka kuti Ambuye akuyika pa mtima wanga kwa phunziro ili lokha, n. . . *Nchifukwa Chiyani Ife Sitiri Chipembedzo?* Chifukwa chimene. . . Tsopano, ife tiribe kanthu kotsutsa anthu ena amene ali chipembedzo. Ife tiribe kanthu kowatsutsa iwo, koma ine ndikufuna kufotokoza chifukwa chimene ife sitinapite konse mu chipembedzo chirichonse. Ine ndinadzozedwa mu mpingo wawung'ono wa Baptisti, monga inu mukudziwa. Ndipo Baptisti si chipembedzo ayi, sanali mpaka posachedwapa, ndipo tsopano iwo ukukhala mochuluka basi chipembedzo monga ina yonseyo. Koma, chifukwa chimene ife sitinakhale konse chipembedzo.

<sup>16</sup> Tsopano, ife ndife bungwe. Ife ndife bungwe, lolembedwa pano mu—mu mabwalo amilandu ngati bungwe, gulu la anthu limene lagwirizana palimodzi kuti lizipembedza Khristu, koma ife sitiri mu chipembedzo. Palibe yemwe ati achite ulamuliro pa ife, inu mukuona. Sindicho chipembedzo. Ilo—ndi bungwe chabe la chiyanjano pakati pa Akhristu okhulupirira. Anthu amabwera kuno ku tchalitchi, ndipo chino chimakhala tchalitchi cha kwawo, ngati iwo afuna kuti azibwera pamene iwo ali moyo.

<sup>17</sup> Ndipo iwo akhoza kumabwera pano ndi kutsutsana nacho chirichonse chimene ife timalalikira. Ndizo zabwino mwangwiro. Inu mukanali, malingana ngati inu muli Mkristu, inu muli nacho chiyanjano ndi dzanja lotambasuka basi mofanana ndi ena onsewo. Mwaona? Ngati ine nditanena kuti ine ndimakhulupirira mu kubatizidwa mwa kumizidwa ndi madzi, ndipo inu mumakhulupirira mu kukonkha, ndi kukhala kumene pa icho, ife tidzakhalabe mofanana basi monga ife tinali ngati ife tonse titagwirizana. Ife mwina sitingakhoze kukwanitsa kupenya diso kwa diso, mofanana, koma malingana ngati inu muli m'bale Wachikhristu kapena mlongo, ndinu wolandiridwa mwangwiro, onani, aliyense.

<sup>18</sup> Kotero ife tiribe zipembedzo zirizonse, chifukwa ine ndikuganiza kuti chipembedzo chimalekanitsa ubale. Ena a iwo, amati, “Chabwino, ife tiribe kanthu koti tichite mu chitsitsimutso chimenecho, icho ndi chitsitsimutso cha Chimethodisti. Chabwino, icho ndi cha Chibaptisti, ife tiribe. . . Ndife Amethodisti, ife tiribe kanthu kochita ndi izo.” M'bale, ngati Khristu ali mu zimenezo, ife tiyenera—ife tiyenera tonse kuti tichite ndi icho. Ife tiyenera kuyika zathu. . . Ilo—ndi thupi la Khristu limene liri—liri kuvutika. Ndipo ine ndikuwona izo mochuluka kwambiri mu dziko lero, kuti momwe ife tiri. . . Tsopano, Khristu sanachite konse, pa nthawi iliyonse, kuyamba wapangapo bungwe mpingo wa

chipembedzo uliwonse. Tsopano, ingololani izo kuti zikhale zotsimikizidwa bwino.

<sup>19</sup> Tsopano, tsopano, ine ndikufunsani inu mawa usiku, ngati zirizonse za zinthu izi inu mukufuna kuti mudziwe, monga mbiriyakale ina imene ine ndikuyikamba, kapena chinachake chimzake. Ine ndiribe nthawi basi yoti ndikhuthuliremo zimenezo, ine sindifika ku phunziro lina, chifukwa iwe ukhoza kukhala masabata pa phunziro lomwelomwelo. Koma ngati inu mukufuna kuti mudziwe malo ake, chirichonse, ingondifunsani ine ndi kuliyika ilo apa pa—pa desiki, ndipo ine ndilitenga ilo, kuyankhira ilo kwa inu.

<sup>20</sup> Tsopano, chipembedzo chakale kwambiri, ndi mpingo woyamba wa chipembedzo umene ife tinayamba takhalapo nawo, ndi mpingo wa Katolika. Ndipo iwo unapangidwa bungwe zaka mazana atatu ndi zina pambuyo pa imfa ya mtumwi wotsiriza. Ndiko kulondola. Inu mumapeza izo mu Nicene Fathers yoyambirira, ndipo inu mumapeza izo mu zolemba izi za Josephus, ndipo, o, zambiri za—za azambiriyakale opambana. Mukuona? Ndipo monga mu—i... iliyonse ya mibadwo ya mpingo, mmusi kupyola mpaka imfa ya mtumwi wotsiriza, ndi zaka mazana atatu kumbali yina ya atumwi, uko kunalibe mipingo ya chipembedzo. Ndipo Katolika unali mpingo woyamba wa chipembedzo.

<sup>21</sup> Ndipo mipingo ya Chiprotestanti ili zipembedzo zimene zinatuluka kuchokera ku chipembedzo. Kukonzanso koyamba kumene kunabwera, kunali Lutera; atachoka Lutera anabwera Swingli, atachoka Zwingli anabwera Kalvini, ndipo basi kupitirira mmusi monga choncho. Ndipo mmusi mpaka ku Chitsitsimutso cha Chiwesile, ndipo kupitirira mmusi kwa Alexander Campbell, John Smith, ndi enaonse, onani, kupitirira mmusi. Ndipo kusuntha kotsiriza kumene ife tiri nako, mpaka tsopano, kuli nthawi zosiyana za m'badwo wa Chipentekoste.

<sup>22</sup> Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Mulungu wachita mu m'badwo uliwonse. Koma kodi inu munayamba mwazindikira kuti nthawi iliyonse pamene mpingo ulephera konse, ndipo mwamsanga pamene iwo achita chipembedzo iwo amayamba kulephera pomwepo? Ndipo pamene iwo alephera, Mulungu samawuwukitsanso mpingo umenewo kachiwiri. Iwo umapita molunjika kumene ku mbewu. Tsopano inu basi... Ngati inu mukufuna kudziwa mbiriyakale pa zimenezo, ife—ife tikhoza kuyitulutsa iyo, kuti—kuti palibe mpingo, palibe konse mu mbiriyakale ya mipingo, pamene chipembedzo chirichonse chinayamba chagwa chimene chinawuka konse kachiwiri. Baptisti, Methodist, Presbateria, Lutera, ndi chirichonse chimene icho chingakhale, pamene iwo anagwa, iwo apita. Tsopano, ndiko kulondola. Tsopano, izi, ine—ine ndinakuwuzani inu tsopano, valani zikhoto, chifukwa ife tipanga Izi kuti zimatirire. Mwaona? Sipanakhale konse, pa nthawi imodzi,

pamene munthu anatuluka monga wapayekha ndipo nawupanga bungwe mpingo, umene unayamba.

<sup>23</sup> Mulungu amachita ndi aliyense payekha, osati ndi chipembedzo. Mulungu palibe mu m'badwo uliwonse umene anayamba wachitapo ndi chipembedzo. Iye nthawizonse wachita ndi munthu payekha. Mu Chipangano Chakale, Iye ankachita ndi munthu payekha. Mu Chipangano Chatsopano, Iye ankachita ndi munthu payekha. Mu m'badwo uliwonse, Iye nthawizonse wachita ndi munthu payekha, ndipo osati zipembedzo. Kotero, chotero, ngati Mulungu sali mu chipembedzo, nchantchito yanji kuti ine ndikhale nacho chirichonse chochita ndi icho monga chipembedzo? Tsopano, ine sindikuyankhula zokhudza anthu mu chipembedzo chimenecho, ine ndikuyankhula zokhudza chipembedzo pachokha, chifukwa anthu a Mulungu ali mu zipembedzo zonse izo.

<sup>24</sup> Tsopano, Mulungu samalola konse chirichonse kuti chichitike kupatula ngati Iye apereka chenjezo kwa icho. Ine sindikukhulupirira kuti chiripo chirichonse chimene . . .

<sup>25</sup> Tsopano, monga ife tiri nazo nkhani zimene zimabwera kuchokera mu mipingo, monga ngati ife takhala nayo imodzi posakhalitsapa yokhudza magari ndi mafuta, ndi zina zotero, ndipo inu mukuyidziwa kalata ya "Wokonedwa M'bale Branham," ndi zina zotero. Koma chifukwa chimene ine ndinayima motsutsa izo, chifukwa izo siziri mu Mawu. Ndipo ndicho chifukwa chimene ine ndikutsutsa chipembedzo, chifukwa icho sichiri mu Mawu. Ndipo icho chiyenera kukhala ndi chinachake chimene ife tiyenera kuyikapo chikhulupiriro chathu. Ndipo ngati ife sitingakhoze kuchiyika icho pa chipembedzo china, ife tiyenera kuchiyika icho pa Mawu a Mulungu. Chifukwa, Awo ndiwo maziko okhawo, ali, Mawu a Mulungu.

<sup>26</sup> Ndiyeno ngati Mawu a Mulungu sayankhula za chipembedzo, koma amayankhula motsutsa chipembedzo, ndiye ife tiyenera kuyankhula limodzi ndi Mawu. Mosasamala chimene abishopu, chimene wina aliyense anena, chimene aliyense aganiza, chimene munthu wabwino anena, chimene chirichonse chinena, ngati icho sichiri mogwirizana ndi Mawu a Mulungu, ndiye ndi cholakwika. Onani, icho chiyenera kukhala, Mawu ayenera kukhala chinthu chotsirizira. Mawu a Mulungu ayenera kukhala Ameni wotsiriza.

<sup>27</sup> Tsopano kumbukirani, ine sindikumupanga aliyense kusakhala mkhristu (inu mukumvetisa zimenezo) mu zipembedzo. Ziripo zikwi makumi za miyoyo yofunika mu zipembedzo zonse zimenezo, omwe ali ana a Mulungu. Koma kuti ndiwalekanitse iwo ndi kuwasankha iwo, ine ndikutsutsana nazo izo. Ndipo Mawu a Mulungu amatsutsa izo.



28 Ndipo ine ndikukhulupirira kuti palibe lingaliro limene liripo mu dziko lero, palibe lingaliro limene linayamba lakhalapo mu dziko, koma limene ilo linaloseredwa kuti likubwera, mwa Mawu a Mulungu. Ine ndikukhulupirira kuti Mawu a Mulungu amapereka chirichonse chimene ife tiri nako kusowa kwake, pano pomwe mu Mawu. Kuchokera ku... chiyambi chathu mpaka ku mapeto, izo zimapezeka kumene mu Mawu a Mulungu. Ndiyeno ine—ine ndikukhulupirira kuti ngati izo ziri mu Mawu a Mulungu, ndiye ife tiyenera... Izo zimaneneratu. Ndipo Mawu a Mulungu ali chenjezo.

29 Tsopano, iwe sumawerenga Mawu a Mulungu monga ngati iwe ukuwerenga nyuzipepala. Iwe umawerenga Mawu a Mulungu mwa Mzimu Woyera, mwaona, chifukwa Mzimu Woyera Iwomwini ukuyankhula kupyolera mwa Khristu. Khristu kumuthokoza Mulungu kuti Iye anali atazibisa zinthu izi kwa maso a anzeru ndi aluntha, ndipo akanadzaziulula izo kwa makanda onga amene akanati adzaphunzire. Kotero, inu mukuona, palibe njira yokhalira wophunzira konse, palibe njira yopangira chipembedzo konse. Pali njira imodzi yokha kuti ukhale bwino, ndiyo, kukhala otsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, ndipo chokuchitikira icho chimene iwe unali nacho chiyenera kumagwirizana ndi Mawu awa. Mwaona, ndiye iwe wachipeza icho. Mwaona?

30 Monga pamene ife tifika mmusi umu maminiti pang'ono tsopano, ife tikuchita ndi anthu amene ali—ali... ena a iwo ali Achikalvini mopitiriza muyezo, ndi—ndi njira zosiyana. Tsopano, pali nthawizonse, ziribe kanthu kaya inu muyengula mopyapyala bwanji icho, icho chiri nazo mbali ziwiri kwa icho. Ndiko kulondola chimodzimidzi. Ndipo iwo onse ali nazo nsonga zotsutsirana. Koma, chinthu cha icho chiri, pamene pakugona Choonadi cha izo? Ndi kumene ife tikubwerako, kumene ife tikuganiza, mwa chisomo cha Mulungu, ife tikhocha kukuwonetsani inu Choonadi cha izo. Tsopano tiyeni tingotenga... ndipo apa pali basi pamene ine ndalembapo zina za Ziphunzitso za mpingo izi.

31 Tiyeni titembenuze mu Mabaibulo anu maminiti pang'ono chabe, nonse a inu tsopano, ndipo tiyeni tifikе ku Chivumbulutso, mutu woyamba, kapena Chivumbulutso, mutu wa 17, kuti tiyambirepo. Ndipo tiyeni tingoyamba kuwerenga ndi kupeza tsopano kumene mipingo iyi inayambirapo, ndi chimene—chimene chinayambitsa iyo. Tsopano, Baibulo limachenjezeratu chirichonse. Ilo limachenjeza masiku amene ife tirimo—amene ife tikukhalamo. Ndipo tsopano, Chivumbulutso, mutu wa 17, ngati inu mungathe. Ine ndinati mutu wa 13, ine sindinatanthauze zimenezo, ndizo pa... Ife titenga umenewo pakapita kanthawi, aponso, ndizo mu ulosi

wa United States. Koma mvetserani mwatcheru kwenikweni tsopano.

*Ndipo pamenepo anadza kwa ine mmodzi wa angelo asanu ndi awiri amene anali nazo mbale zisanu ndi ziwiri, ndipo anayankhula ndi ine, kunena . . . Bwera kuno; ndipo ine ndikuwonetsa . . . iwe chiweruzo cha hule lalikulu limene likukhala pa madzi ambiri:*

<sup>32</sup> Tsopano kumbukirani, izi zikumveka mwachinsinsi. Tsopano mkazi wa mbiri-yoyipa uyu, tsopano, ngati ife titi tiphunzitse izi, inu muyenera kupeza poyamba chimene ziphiphiritso izi zikutanthauza. Tsopano, *mkazi*, mu Baibulo, amayimira “mpingo.” Ndi angati amadziwa zimenezo? Ife ndife Mkwatibwi, Mpingo uli Mkwatibwi.

<sup>33</sup> “Bwera kuno ndipo ine ndidzakuwonetsa iwe chiweruzo.” Tsopano, apo pakhala chiweruzo chimene chiyankhulidwira pa hule lalikulu, mkazi wosayera amene akukhala pa madzi ambiri. Tsopano, *mkazi* kufanizira “mpingo,” ndipo *madzi* kufanizira “anthu.” Tsopano, ngati inu muti muzindikire izo, ndiponso, penyani pa ndime ya 15 inu mukanali pamenepo, ndime ya 15, mutu womwewo.

*Ndipo iye ananena kwa ine, Madzi amene iwe ukuwawona, kumene hule akhalako, ali anthu, ndi khamu, . . . mafuko, ndi malirime. Mwaona?*

<sup>34</sup> Tsopano, mpingo wawukulu uwu, mkazi wamkulu, tsopano kumbukirani iye ali mkazi wa mbiri-yoyipa. Ndipo ngati mkazi amayimira mpingo, (ndipo Mpingo wa Khristu uli Mkwatibwi, Mkwatibwi woyera), ndiye apa pali mkazi wosayera. Ameneyo akanayenera kuti akhale wosayera, wonamizira kukhala, mkwatibwi. Mwaona? Tsopano, ndipo kodi iye akuchita chiyani? “Iye akukhala pa,” kapena, “kukhala pamwamba” zikutanthauza “kukhala nako kulamulira pa madzi ambiri.” Mwa kuyankhula kwina, iye ali nayo mphamvu kupyola mu mafuko onse ndi malirime ndi anthu. Iye ndi munthu wamkulu, mkazi uyu ali.

*Tsopano, yemwe mafumu a dziko lapansi achita naye chiwerewere, . . .*

<sup>35</sup> “Pakuti mafumu a dziko lapansi achita ziwerewere,” anthu olemera, anthu otchuka achita. Iwe ungakhoze bwanji kuchita, mfumu ingachite bwanji ziwerewere ndi mpingo? Ndizo ziwerewere zauzimu, zauzimu! Chiwerewere ndi chiyani? Ndicho, chabwino, ndizo monga mkazi kumakhala mosawona kwa mwamuna wake, iye akugona ndi mwamuna wina pamene iye ali naye mwamuna. Ndipo mpingo uwu, ndiye, uli—ukunyengezera kukhala Mkwatibwi wa Khristu, pamene iwo ukuchita chiwerewere ndi mafumu a dziko, ndi makhalidwe ake osayera, kudzinenera kosayera. O, Ndi zakuya ndipo Ndi zolemerera, ine ndimangowakonda Mawu! Tsopano zindikirani.

*...yemwe mafumu a dziko lapansi achita naye  
ziwerewere, ndipo okhala mu dziko lapansi apangidwa  
kuledzera ndi vinyo wa chiwerewere chake.*

<sup>36</sup> “Vinyo” wake ndi yemwe iye anali kumupereka, kukondoweza kwache, “Ife ndife mpingo! Ife ndife amene tiri nacho icho.” Mwaona? Tsopano, ingojambulani zimenezo mu malingaliro anu tsopano. Chabwino. Kotero iye ananditenga. . .

<sup>37</sup> Monga mngelo anamuwuza Yohane, “Ine ndikuwonetsa iwe chiweruzo ichi chimene chikubwera kwa mpingo wawukulu uwu.” Tsopano penyani.

*Kotero iye ananditengera iye kutali mu mzimu kupita  
ku chipululu: ndipo ine ndinamuwona mkazi akukhala  
pa chirombo cha mtundu wofiira, . . .*

<sup>38</sup> *Kufiira*, mu Baibulo, kumayimira, “ufumu.” *Mtundu wa scarlet* umatanthawuza “kufiira.” Ndipo *chirombo* chimayimira “mphamvu.” Kodi inu munazindikira kuti chirombo chinatuluka kuchokera mu nyanja, umo munali mu Chivumbulutso, wa 13. Ndipo pamene inu muwona chirombo chikubwera kuchokera mu nyanja, izo zikutanthauza kuti mphamvu iyi inali kuwuka pakati pa anthu. Koma mu Chivumbulutso 13, pamene mwanawankhosa uyu anabwera, iye anabwera kuchokera pa dziko lapansi, popanda anthu, United States. Komano pambuyo pa kukhala kwake ndi nyanga ziwiri zazing’ono, mphamvu zaboma ndi zampingo, ndiyeno iye analandira mphamvu ndipo anayankhula monga chinjoka chinachita asanakhalepo iye. Kotero inu mungoyenera kuti muchilembe icho, ife tikubwera mu kuzunza kwa chipembedzo ndi zinthu zomwezo zimene iwo anachita mu Roma wachikunja zaka zambiri zapitazo, pakuti, ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE! Tsopano ndi chiyani icho, “akukhala pa chirombo, mphamvu.”

<sup>39</sup> Kodi inu munazindikira Rabeka pamene Elieza anamupeza iye, umo munali mu nthawi ya madzulo, ndipo iye anamwetsera ngamira. Chifukwa, Elieza anati, “Ngati namwali amene ati abwere ndi kumwetsera ngamira iyi, ameneyo adzakhala. . . ndi kundipatsa ine ndimwe, ameneyo adzakhala mmodzi yemwe Inu mwamusankha, Ambuye, kuti akhale mkwatibwi wa wantchito Wanu, Isaki.” Ndipo pamene iye anali akadali mu pemphero, Rabeka anabwera ndipo anatunga madzi ndi kumupatsa iye kuti amwe, ndi kumwetsera ngamira. Zindikirani, ngamira inali nyama. Ndipo nyama yomweyo imene iye anali kuyimwetsera, inali yomwe inamunyamula iye kupita kwa mkwatibwi wake, Isaki.

<sup>40</sup> Ndipo lero, mphamvu ya Mzimu Woyera, imene mpingo ukuyimwetsera ndi kuyipembedza, ili chinthu chimene chiti chidzawunyamule iwo kuchokera pa dziko lapansi ili, kuti akakomane naye Mkwatibwi. Zedi, Isaki anali kunjira mmunda

madzulo. Ife sitikukomana naye Ambuye mmwamba mu Ulemerero. Aefeso, mutu wa 5, ananena kuti “ife tidzakomana naye Iye mu mlengalenga.” O, izo zimapangitsa Amethodisti kukonzekera kufuula. Taganizani za izo! Mwaona? Ambuye. . . Isaki anali atabwera kuchokera ku nyumba ya atate ake, ndipo anali kunja mmunda pamene iye anamuwona Rabeka akubwera pa ngamila, ndipo iye anamukonda iye pakuwonana koyamba, ndipo analumpha kuchoka pa ngamila ndi kuthamanga kuti akakomane naye iye. Ndiko kulondola. Ndiko kumene ife tikukomana naye Ambuye. Ndipo ngamila yomweyo imene iye anayimwetsera, inamunyamulira iye kupita kwa mwamuna wake. Ndipo mphamvu yomweyo imene mpingo ukuyipembedza, imene dziko likuyitcha zotentheka, imene mpingo ukuyipembedza, idzakhala mphamvu yomweyo imene idzatengere mpingo mmwamba mu mlengalenga, kukakomana naye Ambuye mu mlengalenga. Mzimu Woyera, mukuona. Apo izo. . . Ndipo, penyani, Rabeka anali namwali.

<sup>41</sup> Ndipo mkazi uyu ndi wachiwerewere, za yemwe ife tikukamba apa. Tsopano, inu mwamvetsa chimene mphamvuyo ili tsopano? M—mphamvu, chimene. . . zikutanthauza kuti chirombo, iye anali pa chofiira. Tsopano, kodi icho chingakhale chirombo cha mtundu wanji? *Chofiira*, iyo ikanakhala “mphamvu yolemera.” Ndi mpingo wamtundu wanji uwu umene iye ati akhalepo tsopano? Iwo ndi mpingo wolemera, ndipo iwo ndi mpingo wawukulu, ndipo iwo ndi mpingo wamphamvu, ndipo iwo. . . chikopa chikusesa khamu ndi anthu. Ndipo mafumu a dziko lapansi achita ziwerewere zauzimu ndi iye, ndiwo, amuna otchuka a dziko lapansi. Tsopano ife tipeza yemwe iye ali mu miniti chabe, ndi kupeza zokhudza zipembedzo izi.

*Ndipo mkaziyo anali atavekedwa chibakuwa (mwachifumu), anavekedwa mu mitundu ya chibakuwa ndi yofiira, . . . zokongoletsedwa ndi golide ndi miyala yodula . . . ngale, ali nacho chikho chagolide mu dzanja lake chodzaza ndi themberero ndi uwe wa chiwerewere chake:*

<sup>42</sup> Kodi iye anali ndi chiyani mu dzanja lake? Chiphunzitso chake, chimene iye anali kunyamula kuchipereka kwa anthu, “Ife ndife mpingo! Ife ndife *ichi!*” Ndipo iye wapangitsa mafumu a dziko lapansi kuti akhale oledzera ndi iye monga choncho. “Ife ndife *ichi!* Ife ndife mphamvu zazikulu! Ife tikusesa fuko lirilonse! Ndife mpingo wawukulu umene ulipo. Bwerani kuno, zamweni za wathu. . . Pano, tsanulani pang’ono pokha za iwo, inu imwani iwo, inu imwani iwo.” Ndi zimenezo, mwaona, “ndipo iye anali nacho mu dzanja lake chikho.” Penyani.

*Ndipo mkaziyo anali atavekedwa mu mitundu ya chibakuwa ndi yofiira, . . . zokongoletsedwa ndi golide ndi miyala yodula ndi ngale, ali nacho chikho chagolide*

*mu dzanja lake chodzaza ndi themberero ndi uwe wa chiwerewere chake:*

43 Tsopano abwenzi, ife sitikuwerenga nyuzipepala ya tsiku ndi tsiku, ife tikuwerenga Mawu a Mulungu Amuyaya ndi odalitsika. Miyamba yonse ndi dziko lapansi zidzapita, koma Mawu amenewo adzakhalapobe! Ndiko kulondola.

*Ndipo pa mutu pake panali patalembedwa dzina, panali dzina litalembedwa, kani, CHINSINSI, BABELONI WAMKULU, MAYI WA TIMAHULE, THEMBERERO LA DZIKO LAPANSI.*

44 Tsopano, kuno nthawiyina kale, ine sindikuganiza kuti ndi mu mpingo muno, koma ine ndinalalikira pa phunziro, *Cholembedwa Pa Khoma*, ndi kupereka mayimidwe a mbiriyakale ya Babeloni. Tsopano, lingaliro lirilonse limene linayamba labwerapo, chipembedzo chirichonse ndi lingaliro lirilonse limene liripo mu dziko lero, linayambira mu Genesis. Tsopano, ngati inu mutatenga *Two Babylons* la Hislop, ngati inu mukufuna kutsatira izo mu mbiriyakale, kapena ena a mabuku abwino awo, inu mukhoza ngakhale kulipeza lingaliro lirilonse limene inu mukufuna kuti mulipeze. Ine ndikutengerani inu kumbuyo uko mu maminiti pang'ono pa alaliki aakazi, mwaona, ndi kukuwonetsani inu basi kumene izo zinayambikira poyamba, mwaona, mmbuyo mu Genesis. Ndi pa zinthu izi zosiyana, basi momwe izo zinatulukira kuchokera ku Genesis. *Genesis* amatanthauza “chiyambi.” Ndi angati akudziwa kuti ndiko kulondola? Genesis ali chiyambi. Kotero, chirichonse chimene chiripo, chinayenera kukhala nacho chiyambi.

45 Pamene ine ndiyang'ana pa mtengo. Ine ndakhala ndiri mthengo kwa ingapo, itatu, pafupi miyezi iwiri. Ine ndimawona mtengo, momwe iwo uliri wokongola. Ine ndimawuwona iwo, iwo ukupita pansu; wina umatulukira mu malo ake, moyo wosadukiza. Ndipo ine ndimaganiza za zimenezo. Koma penapake mtengo umenewo unali nacho chiyambi. Iwo unayenera kukhala nacho chiyambi. Ndipo njira yokhayo yomwe iwo ukanakhoza kukonzedwa kuti ukhale mtengo, kapena kuti ukhale nthundu, kapena chiwale, kapena popula, kapena mgwalangwa, kapena chirichonse chimene iwo unali, apo panayenera kukhala Mwini wa Luntha kumbuyo kwa iwo. Kapena ngati kukanakhala umodzi wokha, kukanakhala mtengo umodzi wa nthundu, chirichonse mu dziko chikanadzakhala zonse mtengo wa nthundu. Koma Chinachake chachikulu, Mwini wa Luntha, anayenera kuyika izo mu dongosolo. Lidalitsike Dzina Lake Loyera! Iye ali Mmodzi Amene amayika mwezi ndi nyenyezi mu dongosolo la zowalitsa. Iye anayika chirichonse mu dongosolo lake. Ndipo Iye adzawuyika mpingo Wake mu dongosolo, Iwo udzatembenuka monga momwe Iye akufunira kuti Iwo uzitembenuka, kummawa, kumadzulo, kumpoto, kapena kummwera, kapena chirichonse chimene chiri,

pamene ife tingakhoze kutengera malingaliro achipembedzo awa kunja kwa malingaliro athu ndi kudziponyera tokha mwathunthu ku Kalvare. Iye adzawayika iwo mu dongosolo ngati ife titi tidzangokhala odzipereka monga mitengo ndi chirengedwe Chake china. Inu simunawuwonapo mwezi ukuti, “Ine sindiwala usikuuno, zina za inu nyenyezi muwale mmalo mwanga.” Koma ife, ayi, ndife osiyana, inu mukuona.

<sup>46</sup> Tsopano, Babeloni, penyani momwe Babeloni ankawonekera. Iye akuwonekera koyamba kwa Baibulo. Iye akuwoneka mkati mwa Baibulo. Ndipo iye akuwoneka kotsiriza kwa Baibulo. Tsopano, apo pali chinachake. Tsopano, iye anayamba ndi Nimrodi. Nimrodi anayambitsa Babeloni mu Chigwa cha Shinara, pafupi ndithu pakati pa Mtsinje wa Tigirisi ndi Efurate, ndipo Efurate ankadutsa mopyola. Ndipo—ndipo momwe kuti msewu uliwonse kupyola mu dziko lonse ilo unkalondolera molunjika ku Babeloni! Ndipo chimodzi chirichonse cha zipata zimenezo zinali pafupi mapazi mazana awiri kupingasa, zipata zimenezo zopangidwa kuchokera ku mkuwa. Ndipo pamene iwe umafika mkati mwa mzinda wa Babeloni, msewu uliwonse umalondolera molunjika ku mpandowachifumu.

<sup>47</sup> Tsopano, inu mukhoza kupita ku Roma lero, ndipo msewu uliwonse ukalondolera ku Roma. Ndipo kuli Maria wamng’ono namwali atakhala pa ngodya iliyonse, mu kukhota kwa msewu, ali ndi Khristu mwana mu dzanja lake, akulozera njira imeneyo cha ku Roma. Mwaona? Iye akupezeka koyamba kwa Baibulo, iye akupezeka pakati pa Baibulo, ndipo pano iye ali ku mapeto a Baibulo. Tsopano ine ndikungofuna kuti ndiwerenge mopitiriza kwa maminiti pang’ono chabe, kotero kuti inu mumvetsa maziko a izi, onani. Chabwino.

*Ndipo ine ndinawona mkazi... (tsopano upenyeni mpingo, pamene inu mukuwona mkazi muziganiza za “mpingo,” mwaona)... ine ndinawona mkazi ataledzera ndi magazi a oyera, . . .*

<sup>48</sup> Tsopano, kodi mawu woti *woyera* amachokera kuti? Mawu oti *woyera* amabwera kuchokera ku “iye woyerayo” kapena “iye woyeretsedwayo.” Woyeretsedwa! Chabwino.

*. . . Ine ndinawuwona iye ataledzera ndi magazi a oyera, . . .*

<sup>49</sup> Tsopano, ngati mkazi uyu ali mpingo, iye akuzunza oyera. Ndipo iye ali mpingo wawukulu kwambiri, iye ali nazo mphamvu zolamulira pa dziko lapansi. Iye ali pamwamba pa madzi ambiri, ndipo iye. . . mafumu a dziko lapansi akuchita ziwerewere ndi iye. Chabwino, kodi iye ndi yani? Zikukhala ngati chinsinsi. Tsopano Mzimu upita ku. . . Inu mukudziwa, pali kuyenera kukhala mphatso zisanu ndi zinai zauzimu mu

mpingo, mpaka nzeru, ndi imodzi ya kumvetsa, ndi imodzi ya machiritso, ndi ina ya zina zotero.

... *ndipo ndi magazi a ofera a Yesu: . . .*

<sup>50</sup> Zikuwoneka ngati kuti iwo sankasamala mochuluka zimene Yesu ananena, izo zinali zimene mpingo unkanena. Ndiko kulondola. Ndipo ndiko kulondola, aponso.

... *ndipo pamene ine ndinamuwona iye, ine ndinadabwa ndi kuzizwa kwakukulu.*

<sup>51</sup> “Ine ndinadabwa ndi kuzizwa. Ine . . . Icho chinali—chinthu chozizwitsa chokhudza iye, momwe kuti ine ndinadabwira, momwe kuti iye. . .” Tsopano ndiroleni ine nditenge malo a Yohane ndi kuyesera kutsegula izo pang’ono pokha, mwaona. Yohane anati, “Apo iye wakhala. Iye akunyengezera kukhala mpingo wa Chikhristu. Iye ali nawo mwayi wonse wa ku ndalama za dziko. Iye ali nawo mafumu a dziko lapansi mkati pa mapazi ake. Iye ali chinthu cholemera ndi chamangamanga, ndipo iye angakhoze bwanji kuledzera ndi ofera a Yesu? Iye angakhoze bwanji kuwazunza oyer? Iye angakhoze bwanji kuwapha ofera amenewo a Khristu, ndipo komabe iye akudzinenera kukhala Mkhristu iyemwini, mpingo wa Chikhristu?” Tsopano penyani.

*Ndipo mngelo ananena kwa ine, Kodi iwe unazizwa chifukwa chiani? Ine ndikuwuzwa iwe chinsinsi cha mkazi, ndi cha chirombo chimene chikumunyamula iye, ndi chimene chinali. . . mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi.*

<sup>52</sup> Tsopano, uku ndi kuwerenga wamba chabe pano tsopano. Inu muzigwire izi, izi zikhala zophweka kwambiri.

*Chirombo chimene iwe unachiwona chinaliko, ndipo kulibe; ndipo chidzatsikira kunja—kukwera kuchokera ku phompho lopandamalire, ndipo chidzapita ku chiwonongeko: ndipo iwo amene akukhala pa dziko lapansi adzadabwa, amene maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo kuchokera ku maziko a dziko, pamene iwo awona, pamene iwo—pamene iwo anachiwona chirombo chimene chinalipo, chimene kulibe, ndipo komabe chiripo.*

<sup>53</sup> Tsopano, tsopano izi ziyenera kutsina, kotero pano izo ziri. Iye anati, tsopano zindikirani, kuti pamene onse, osati pang’ono chabe, koma onse amene akukhala pa dziko lapansi ati adzadabwe, onse a iwo adzadabwa. Dziko lonse lidzadabwa za mkazi uyu. Apo pali gulu limodzi lokha limene silidzakhala likudabwa za izi, ndipo ndilo iwo amene anali nalo dzina lawo mu Bukhu la Moyu wa Mwanawankhosa.

<sup>54</sup> Tsopano, ine basi mwina ndikhoza kukanikizira izi pomwe apa, chifukwa ife tipita mu izo mu maminiti angapo. Mwaona?

Ndi liti pamene maina awo anayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa? Kuchokera liti? Chitsitsimutso chotsiriza chimene iwo anakakhalako? Usiku umene iwo anapita ku guwa? Usiku umene iwo anajowina mpingo? Ine sindikuyesera kuti ndikuvulazeni inu, koma, ine ndikukuuzani inu, Baibulo linati maina awo anayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa “chikhazikitsireni maziko a dziko.” Chimodzimodzi! Pamene Mulungu, mu chiyambi, anawona kuti Iye akanadzatuma Mwana Wake, ndipo Iye akanati adzatenge malo a ochimwa, pamene Magazi a Mwana wa Mulungu anakhetsedwa, Baibulo linati Magazi Ake anakhetsedwa maziko a dziko asanayikidwe. Ndi angati amadziwa Baibulo limanena zimenezo, kuti Magazi a Khristu anakhetsedwa asanakhalepo maziko a dziko? Pamene Magazi amenewo anakhetsedwa, membala aliyense wa Thupi, maina ake analembedwa ndi Magazi amenewo pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa pa maziko a dziko. Kodi inu mukuwopsyezedwa chotero ndi chiyani? O, m'bale! Icho chimatsegula zitseko, sichoncho?

<sup>55</sup> Chabwino, tsopano tiyeni tingowerenga izi pomwe pano ndi kuwona ngati zomwe ngati izo zikunenedwa mokhoza, mwaona. “Ndipo mngelo ananena kwa ine, ‘Chotero kuti . . .’” Ine ndikukhulupirira ndi ndime ya 8. “Ndipo chirombo chimene iwe unachiwona . . .” Chabwino, ndi zimenezo.

*Chirombo chimene iwe unachiwona chiriko, ndipo kulibe; ndipo chidzakwera kuchokera ku phompho lopandamalire, . . . (tsopano, ife tikubwerera ku zimenezo, koma ine ndikufuna kutenga zina izi, chifukwa ife tikufika pa izo) . . . ndipo chidzapita ku chitayiko: ndipo iwo amene akukhala pa dziko lapansi adzadadwa, amene maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo kuchokera ku maziko a dziko, . . .*

<sup>56</sup> “Pakhala pali gulu pa dziko lapansi,” mwa kuyankhula kwina, “limene liti lidzanyengedwe,” pakuti iye anawanyenga iwo. Ndipo panali gulu limodzi lokha limene silinali lonyengedwa, ndipo ilo linali limodzi limene linali nalo dzina lake pa Bukhu la Moyo chikhazikitsireni maziko a dziko. Ife tifika mu izo kanthawi kotsatira.

<sup>57</sup> Tsopano zindikirani mkazi, mpingo, iye anali Chinsinsi Babeloni. Ife tikumuona iye akuwonekera ndi Nimrodi. Kodi cholinga cha Nimrodi chinali chiyani? Nimrodi anayambitsa mzinda ndi kupangitsa yonse ya mizinda ina kuti izipereka msonkho kwa mzinda uwu. Kodi ife tingakhoze kuwona chinthu choterocho lero? Kodi alipo malo oterowo lero? Kodi ulipo mpingo umene uli nawo ulamuliro pa fuko lililonse mu dziko? Ndithudi. Kodi alipo malo lero amene amapangitsa fuko lililonse kupereka msonkho kwa iwo? Kodi alipo malowo? Tiyeni tipitirize ndi kukawerenga zonse za izi, pang'onong'ono



chabe, kotero kuti inu mumvetse chithunzi chonse cha izi. Chabwino. . .

. . .chimene anawona *chirombo* chimene  
*chinalipo*, . . . *ndipo kulibe, ndipo komabe chiripo*.

*Ndipo pano pali mtima umene uli nayo nzeru.*

<sup>58</sup> Tsopano, ndi angati akudziwa kuti nzeru ili imodzi ya mphatso za Mzimu? Tsopano, kodi ndi mtundu wanji wa gulu limene, akuyankhula kwa ilo, ndiye? Iye ayenera kuti akuyankhula kwa gulu la anthu amene ali ndi—mphatso za Mzimu zikugwira ntchito mu mpingo uwu.

. . . *pano ziri kwa mtima umene uli nayo nzeru.*

<sup>59</sup> Tsopano, inu muyime, pezani izo zonse kupyola mu mibadwo ya mpingo iyi pano, kuzisolola. Mzimu Woyera ukuyankhula momwe mphatso izo ziti zizidzagwirira ntchito mu masiku otsiriza. Tsopano, ife tiri nazo mphatso za machiritso zikugwira ntchito. O, izo—izo zikuyenda bwino. Chabwino, m'bale, apo ziripo mphatso zina! Iyo ndi imodzi yokha ya izo. Iyo ndi chinthu chaching'ono chosawerengedwa chabe. Chabwino, pano pali mphatso yayikulu mwapatali apa pomwe. Imene ikanati ikhale yopambanitsa, mphatso ya Mzimu Woyera ya nzeru yoti iyike Mawu a Mulungu palimodzi ndi kuwusonyeza mpingo pamene ife tikuyima, kuposa kungomupangitsa winawake kuchiritsidwa? Ife tonse tikufuna kukhala bwino; koma ine kulibwino moyo wanga ukhale bwino, kuposa kuti thupi langa kukhala liri bwino, nthawi iliyonse. O, mai! Mvetserani Mzimu Woyera ukuyankhula kupyolera mwa Yohane pa Patmo, unati, "Pano ziri kwa nzeru, muloleni iye amvetsera kwa Izi." Tsopano ife tikupeza chithunzi chikujambulidwa apa pomwe.

*Pano pali, ndipo pano pali mtima umene uli nayo nzeru. Mitu isanu ndi iwiri ili mapiri asanu ndi awiri, pamene mkaziyo akhalapo.*

<sup>60</sup> Ulipo mzinda umodzi wokha umene ine ndikuwudziwa mu dziko, ilipo mizinda iwiri imene ine ndikuyidziwa, imene ili ndi mapiri asanu ndi awiri kapena kuposerapo mwa iyo. Cincinnati uli umodzi wa iyo, umene ukuyenera kukhala kuti nkhani yopeka ya Cincinnati, nkhandwe ina yake, inu mukudziwa izo, zina zotero. Koma iwo uli nawo oposa amenewo mwa iwo. Koma palibe mpingo umodzi umene umalamulira Cincinnati. Alipo malo amodzi okha mu dziko lonse amene ali nawo mpingo ukukhala pa mapiri asanu ndi awiri, umene ukulamulira dziko lonse. Tsopano, ine ndangobwera kumene kuchokera kumeneko, zinthu zonse zimenezo. Ndipo ine ndinawona kumeneko pamene iwo anati, "Pano pali kwa nzeru." Chivumbulutso 13, "Muloleni iye yemwe ali nayo nzeru awerenge chiwerengero cha chirombo, pakuti ndi chiwerengero cha munthu." Osati gulu la anthu, gulu la amuna, koma "m" munthu. "Ndipo chiwerengero chake

chiri mazana asanu ndi limodzi makumi asanu ndi limodzi-ndi mphambu zisanu ndi chimodzi.”

61 Ine mowirikiza ndamvapo kuti pamwamba pa mpandowachifumu wa papa wa ku Roma, panalembedwa, “Vicariivs Filii Dei.” Ine mowirikiza ndinkadabwa ngati izo zinali zoon. Kujambula mzere, ndi kujambula izo mu mawerengero mu mawerengero achiroma, ndi kuwona ngati izo ziri. Ndi chimodzimodzi zoon. Ine ndinayima pafupi *chotero* kwa korona wa patatu wa papa, mu galasi. Ulamuliro wa gehena, kumwamba, ndi purigatorio, mwaona. Koter, zinthu zimenezo, ine ndabwera kumene kuchokera kumeneko, ndabwera kumene kuchokera ku Roma ndipo ndikudziwa kuti ndi zoon. Tsopano, ife tikudziwa kuti izo zajambulika apa.

*Ndipo pano mafumu asanu ndi awiri: asanu agwa (amene analipo pa nthawi imeneyo), ndipo imodzi ilipo (ndiyo imodzi imene yabwera tsopano, imene inali Kaisara), ndipo ina ndi yotibe ibwere (imene inali Herode, yemwe anali woyipa); . . .*

62 Tsopano penyani, penyani momwe izo ziliri zangwiro.

*. . . ndipo pamene iye akubwera, iye ayenera kupitiriza kwa danga lalifupi.*

63 Kodi alipo aliyense akudziwa utali wa momwe Herode analamulirira? Miyezi isanu ndi umodzi. Anawakhwekhwereza amayi ake kupyola mu msewu pa mtengo umodzi wa kavalo. Ndipo anayatsa mzindawo, ndi kuziyika izo pa Akhristu. Ndi kumakayimba pa mbali ya phiri pamene iwo anali—pamene iwo anali kuwuyatsa mzinda. Isanu ndi umodzi—miyezi isanu ndi umodzi. Ndipo penyani, “Ndipo chirombo . . .” Tsopano penyani, penyani mthakati yemwe iye anali. Mukuona? Tsopano penyani.

*Ndipo chirombo chimene chinaliko, ndipo kulibe, ngakhale . . . ndi chachisanu ndi chitatu, ndipo chiri cha chisanu ndi chiwiri (khalidwe la chachisanu ndi chiwiri), ndipo chikupita ku chitayiko.*

64 Aliyense akudziwa chimene *chitayiko* chimatanthauza, ndi “gehena.” Ndipo penyani kumene iye anatuluka kuchokera iko, “gehena.” Ndi chiyani chimenecho? Phompho lopandamalire. Palibe maziko kwa chiphunzitso cha Chikatolika. Palibe Baibulo kwa chiphunzitso cha Chikatolika. Palibe chinthu chotero ngati Baibulo lililonse kwa chiphunzitso chirichonse cha Chikatolika, ayi konse. Iwo samadzinenera kuti ali. Wansembe ananena kumtunda uko, wansembe wamng’ono uyu kumtunda kuno ku Mpingo wa ku Mtima Woyera anabwera kumeneko, iye anati, “O, iye . . .” Ine ndinali kumuwuza iye za kumubatiza Mary Elizabeth Frazier. Iye anati, “O, inu munamubatiza iye molingana ndi njira yomwe mpingo woyambirira wa Chikatolika unkatatizira.”

Ine ndinati, “Linali liti limenelo?”

Iye anati, “Mu Baibulo, Baibulo lanu.”

65 Ine ndinati, “Kodi mpingo wa Katolika unkabatiza choncho? Kodi kumeneko ndi kuphunzitsa kwa mpingo wa Katolika?”

“Eya.”

66 Ine ndinati, “Mu kudalirika kwa mpingo wa Katolika, nchifukwa chiyani iwo wasintha mochuluka chotero?” Mwaona?

67 Iye anati, “Chabwino, inu mukuona, inu nonse mumakhulupirira Baibulo. Ife timakhulupirira mpingo.” Mwaona? “Ife sitamasamala chimene Baibulo limanena, ndi chimene mpingo umanena.” Ndiko kulondola chimodzimidzi. Ngati inu munayamba mwafikako ku chiwonetsero cha izo, yesani izo kamodzi, inu mukuona. Iwo samasamala chimene Baibulo limanena, Ilo liribe kanthu kochita ndi iwo, iwo amasamala chimene mpingo umanena. Mwaona?

68 Koma ife sitisamala chimene mpingo unena. Ife timakhulupirira chimene Mulungu amanena. Pakuti Baibulo, izo zinalembedwa, “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo Anga akhale Choonadi.” Ndicho chifukwa ife sitiri zipembedzo.

69 Tsopano penyani, mvetserani kwa izi miniti yokha. “Mafumu asanu, amene anagwa, mafumu asanu.” Ngati inu mukufuna zimenezo kuchokera ku mbiriyakale, ine ndisonyeza izo kwa inu. “Ndipo imodzi ilipo, ndipo imodzi ikubwera.” Tsopano penyani, “chirombo.” Tsopano, chirombo sichinali mfumu. Iye anali mmodzi yemwe aliko, yemwe kulibe; ndipo komabe iye aliko, ndipo kulibe; komabe iye aliko, ndipo kulibe. Ndi chiyani chimenecho? Kusinthana kwa mapapa, mphamvu, chirombo chikulamulira. Ndi pamene Roma wachikunja anatembenezidwa kuti apange Roma waupapa Roma wachikunja anatembenezidwa, ndiyeno iye anadzakhala waupapa, chimene, iwo anali ndi papa mmalo mwa mfumu, ndipo papa ali mfumu yauzimu. Ndicho chifukwa iye ali mfumu yauzimu yovekedwa korona, akudzitcha kuti ali wolowa mmalo wa Yesu Khristu. Ndi zimenezotu. Tsopano zindikirani.

70 Ndipo ife tikufuna tibweretse chiphunzitsa cha Chikatolika icho kuchokera pamenepo ndi kukuwonetsani inu momwe icho chapitirira mpaka mu mipingo ya Chiprotestanti, onani, momwe iye akanali kukhalabe mu mpingo wa Chiprotestanti, zochuluka za izo. Mosiyana, chimodzimidzi, kwa Baibulo, mtheradi mosiyana. Tsopano, “chirombo chimene chinaliko, chimene kulibe.” Tsopano kumbukirani, onse a iwo adzanyengedwa pa dziko lapansi, amene dzina lawo silinalembedwe kuchokera ku maziko a dziko. Tiyeni tiwone.

*Ndipo chirombo chimene chinaliko, ndipo kulibe, (ndime ya 11) ndipo komabe chiri chachisanu ndi chitatu, ndipo...cha chisanu ndi chimodzi, ndipo chikupita mpaka ku chitayiko. Iye adzapitirizabe*

mpaka iye atagunda phompho lopandamalire pa mapeto a msewu.

*Ndipo nyanga khumi zimene iwe unaziwona ndizo mafumu khumi, . . . (Tsopano penyani apa. Ngati inu mukufuna kuwona chinachake chogunda, penyani izi) . . . ndizo mafumu khumi, amene sanalandire ufumu apabe; koma alandira mphamvu monga mafumu ora limodzi ndi chirombo.*

<sup>71</sup> Iwo sali mafumu ovekedwa korona; iwo ali olamulira mwankhanza. Onani, iwo sanali mafumu ovekedwa korona konse, koma iwo analandira mphamvu ngati mafumu, ora limodzi, mu ulamuliro wa chirombo. Ndimu mu nthawi pang'ono chabe iyi ya mdima pakali pano imene olamulira mwankhanza akuwukapo, onani, "Kulandira mphamvu ngati mfumu, ora limodzi, ndi chirombo." Tsopano, chabwino.

*Awa ali nawo mtima umodzi, ndipo adzapereka mphamvu zawo ndi nyonga kwa chirombo.*

*Awa adzapanga nkhondo ndi Mwanawankhosa, ndipo Mwanawankhosa adzawalaka iwo: (ulemerero!) pakuti iye ali Ambuye wa mbuye, ndi Mfumu ya mafumu: ndipo iwo amene ali ndi iye ali kutchedwa, osankhidwa, ndi okhulupirika.*

<sup>72</sup> Ndikukhumba ine ndikanakhoza kulalikirira ulaliki pakali pano pa izo, "osankhidwa" maziko a dziko asanayikidwe, ndipo akukhala mokhulupirika mu kuyitanidwa kwawo! Aleluya! Ndizo ziri. Iwo ali kutchedwa "osankhidwa" ndi "okhulupirika." *Ndi ali cholumikizira, mwaona, osankhidwa ndi okhulupirika.* Iwo adzamalaka iye, ziribe kanthu kaya iwo akhale aakulu chotani.

<sup>73</sup> Ndipo chikominisi chachikulu ichi, kachitidwe ka chikominisi kamene ife tiri nako lero, musati mudandaule za iko. Izo zikugwira ntchito chimodzimodzi mu manja a Mulungu, ine ndikhoza kutsimikizira izo mwa Baibulo ili. Iye amupanga iye kuvutika chifukwa cha wofera aliyense yemwe iye anamupha. Inde, bwana. Inu muwapenye mafumu awa onse akugwirizana limodzi, ndipo adzamuda iye. Ndipo fuko lonse, dziko lonse likusesa chikominisi. Chifukwa chiyani, iko kayenera kukhala kachitidwe ka Mulungu kuti alilange ilo. Inu mukuti, "Dikirani miniti, M'bale Branham, chikominisi kachitidwe ka Mulungu?" Mtheradi, ndithudi, iko ndi kachitidwe ka Mulungu. Baibulo linanena choncho. Koma icho chikusuntha kuti chikapange chiweruzo pa osakhala aumulungu ndi anthu a mchigololo ochititsa manyazi. Ndi chiyani chatsalira mu dziko ili? Kodi ife tiri ndi chiyani? Kuno tsiku lina . . .

<sup>74</sup> Ine ndiyimikira pa phunziro langa miniti chabe ngati nkotheke. Ine ndinali kuwerenga mu gawo la Lemba pamene kuti mwana wamchigololo sadzalowa msonkhano wa Ambuye

kwa mibadwo khumi ndi inai. Ndi angati akudziwa zimenezo? Ndiko kulondola, Deteronome 23, mwana wamchigololo. Ngati mkazi agwidwa ku tchire, ndiko, kutali ndi chitetezero cha munthu, ndipo mwamuna akamugonjetsa mkazi ameneyo, mwamuna ameneyo adzayenera kuti amukwatire iye. Ziribe kanthu kuti iye anakhala wachiwerewere, iye ayenera kuti azikhala naye iye mpaka iye atafa. Ndipo ngati mkazi yu akakwatiwa ndi iye, akunyengezera kuti iye ali namwali, ndipo iye asali, ndiye iye akhoza kuphedwa chifukwa cha icho. Ndipo ngati mwamuna ndi mkazi amene ali okwatirana, ndipo iwo akabala mwana wamchigololo, ameneyo, msonkhano wa Ambuye iye sadzalowamo, kwa mibadwo khumi ndi inai; ndipo zaka makumi anai ndizo m'badwo, kuti zikhale zaka mazana anai mbewu imeneyo isanachoke konse mu Israeli.

<sup>75</sup> Mulungu amadana nalo tchimo! Inu mukuyembekeza bwanji kuti musambire pamwamba pa Magazi Oyera wa Ambuye Yesu, basi chifukwa kuti ndinu wa chipembedzo chinachake ndipo mukuyembekeza kuti mupite mkati? Inu muyenera kubwera ku malo a Mulungu kapena inu simubwera konse. Kulondola! Dikoni, mlaliki, chirichonse chimene ife tingati tikhale, chiribe kanthu koti nkuchita nazo izo. Iwe umabwera mwa njira ya Mulungu.

<sup>76</sup> Mibadwo khumi ndi inai. Munthu ali muno pakali pano yemwe anali kukambirana zimenezo ndi ine. Anati, “Ife tikudziwa bwanji yemwe ati adzapulumutsidwe konse ndiye?”

<sup>77</sup> Ine ndinati, “Apo ndi pamene inu muyenera kukhala wa Chikalvini wabwino.” Dzina lanu linayikidwa mu Bukhu asanayikidwe maziko a dziko. Mulungu amatenga mtsempha wa magazi umenewo, izo ziri kwa Iye. Mwaona?

“Chabwino, izo ziri ndi chiyani . . .”

<sup>78</sup> Mvetserani, inu anthu aang’ono lero. Ine sindikudziwa kaya inu mumabwera ku mpingo uno, kapena kumene inu mumabwera, inu anyamata aang’ono ndi asungwana. Kodi inu munazindikira, zinthu zimene inu muli kuchita, ngati ulipo m’badwo wina, ana anu adzaweruzidwa chifukwa cha zimene inu mukuchita? Kodi inu mulibe kulemekeza kapena khalidwe labwino? Asungwana inu amene muli kunja kuno mutavala akabudula aang’ono akale awa ndi zinthu paliponse, inu mukudziwa, zimenezo zikunyezimiritsa pa mwana wanu wamkazi. Kodi inu mumadziwa kuti agogo anu aakazi anali—adama, ndipo amayi anu msungwana wa makolasi, ndipo ndicho chifukwa muli wodolola podzivula lero? Ndithudi! Kodi ana anu adzakhala chiyani? Inde, bwana. Mulungu anati Iye adzachezera kusaweruzika kwa makolo pa ana ndi ana awo, ku mibadwo itatu ndi inai.

<sup>79</sup> Ndipo kodi inu mukuzindikira, m'bale wanga, nthawi iliyonse imene inu muchita izo zimene ziri zolondola, zimenezo zidzachezera pa ana anu?

<sup>80</sup> Penyani pano, tiyeni titenge Ahebri, mutu wa 7. Baibulo linati, pamene—pamene Melkizedeki anakomana ndi Abrahamu akubwerera kuchokera kokapha mfumu, ndipo anamudalitsa iye, ndipo anati. . . Tsopano, Levi, akuyankhula za kupereka zachikhumi. Anati, “Levi anali nako kulamulidwa kuchokera kwa Ambuye kuti azilandira zachikhumi kuchokera kwa m'bale wake.” Ndipo Levi yemwe ankalandira zachikhumi, anapereka chachikhumi, pakuti iye anali akadali mu ziuno za Abrahamu pamene iye anakomana ndi Melkizedeki. Ndipo Abrahamu anali agogo-a abambo ake. Abrahamu anabala Isaki, Isaki anabala Yakobo, Yakobo anabala Levi; Levi, bambo, agogo aamuna, agogo-a abambo ake. Ndipo pamene Levi anali mu ziuno za Abrahamu, Baibulo linati iye anapereka zachikhumi kwa Melkizedeki. Aleluya!

<sup>81</sup> Musati mulole aliyense kuti akuwuzeni inu kuti kachitidwe ka mtundu uliwonse mu dziko kangakhoze konse kusokoneza gudumu lalikulu la Mulungu, iye akusuntha patsogolobe! Izo zinakonzedwa kumbuyo uko ku chiyambi. Palibe adierekezi kapena adierekezi okwanira amene angakhoze kusokoneza dongosolo Lake.

<sup>82</sup> Tsopano, Baibulo silinati “mwakuyankhula kwina” iye anapereka icho, Baibulo linati “iye anapereka zachikhumi” pamene iye anali mu chiuno cha agogo-a abambo ake. Ulemerero! Ndiwo Ambuye anga. O, Iye anazidziwa izo ngakhale dziko lisanapangidwe nkomwe. Iye anadziwa chirichonse. Ndipo mwa Abrahamu iye anapereka zachikhumi.

<sup>83</sup> Ndipo mlongo, m'bale, inu mungakhoze bwanji kuthamanga kunja kuno, ndipo anthu kumakhala ndi kumathamanga thamanga ndi akazi a amuna, ndipo akazi kumaswa mabanja, ndi—ndi kumakhala momwe inu mukuchitira, kodi inu mukuyembekeza kuti m'badwo wina udzakhala chiyani? Pano pali chimene icho chiri, icho chakhala tsopano si kanthu koma gulu chabe la apathengo, gulu losokonezeka-lobadwa mwa chivundi. Ndipo pali chinthu chimodzi chatsalira cha izo, ndipo ndizo tsiku la atomiki limene ife tikukhalamo. Ndiko kulondola chimodzimodzi. Ife tiri pa nthawi yotsiriza.

<sup>84</sup> Nditakhala mmawa uno, kutali mmbuyo kutsidya mu mapiri a Kentucky, ka mnyamata kakang'ono, iwe sukanakhoza konse kufika mapazi khumi kwa iye, akupanga manyuchi a mchewere, mwinamwake sanali kudziwa nkomwe kumene kunali dzanja la kumanja ndi kumanzere, pamene iye anamva. . . Ine ndinali nditafika pa malo oyikidwa. Ine sindinkadziwa kumene ine ndinali, ine ndinali mu kathengo kena chabe. Ndipo ine ndinali kupita chabe kumtunda uko kupita kukasaka agologolo. Ndipo

pamene ine ndinakhala pansi pamwamba apo, ine ndinayamba kuyankhula kwa iye, ndipo mnyamata uyu ananena kuti iye amapita mu nkondo. Ndipo tinafika popeza kuti, iye tinayamba kuyankhula za Ambuye, ndipo iye anati, “Mlaliki, kodi inu simukukhulupirira kuti ife tiri pa mapeto a nthawi?” Kutali uko kumtunda uko mu mapiri amenewo!

<sup>85</sup> Ine ndinati, “Zedi, ife tiri. Zedi, mwana, ife tiri pa mapeto a nthawi.”

<sup>86</sup> Ndife pano. Ili ndi ora limene ife tikukhalamo, m’bale. Ife tiri mu malo. Kodi inu simungakhoze kuwona momwe amayi mmbuyo kutaliko, ndi adadi, momwe iwo ankakhalira, ndi agogo aamuna ndi agogo aakazi? Kodi inu simungakhoze kuwona momwe bambo ndi mayi akhalira moyo? Nzosadabwitsa kuti ife tiri mu kuvunda lero. Nzosadabwitsa kuti iwe ukhoza kulalikira mpaka mutu wako kusokonezeka, iwo azivala akabudula mofanana basi ndi kulavulira mu nkhope yako. Iwo azisuta ndufan ndi kuwuzira iwo kumene pa iwe, ndi kuti, “Samalira ntchito yako yako.” Chifukwa chiyani? Chifukwa ndilo fuko limene iwo anatuluka kuchokeramo. Ine ndifika ku zimenezo molunjika, *Mbewu ya serpenti*, ife tipeza kumene iye akusunthira mkati, kuwona chifukwa iwo akuchitira monga choncho. Iwo ndi ana a Mdierekezi chikhazikitsireni maziko a dziko. Ndi kulondola. Ndipo ife sitiri kanthu otsalira kwa izo, basi—basi chiweruzo chiri chinthu chokhacho chimene chatsalira. Sitingakhoze kukhala ndi china chirichonse koma chiweruzo. Mulungu adzangofufuta chinthu chonsecho kuchichotsa, ndipo anthu achita izo okha okha. Mulungu sanalinge kuti izo zikhale mwa njira imeneyo, koma Iye anadziwa kuti izo zikanadzakhala mwa njira imeneyo. Ndicho chifukwa Iye anati Iye akanadzanyenga onse amene anakhala pa nkhope ya dziko lapansi, kupatula iwo amene maina awo analembedwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa asanayikidwe maziko a dziko.

<sup>87</sup> Tiyeni chiyani. . . tiwerenge mopitiriza pang’ono tsopano. Tsopano, tsopano ine ndikukhulupirira ife tiri pa ya 12.

*Ndipo nyanga khumi zimene iwe unaziwona ndizo mafumu khumi, amene sanalandire ufumu apabe; koma alandira mphamvu monga mafumu ora limodzi ndi chirombo.*

*Awa adzakhala ndi mtima umodzi, ndipo adzapereka mphamvu zawo ndi nyonga kwa chirombo.*

*Ndipo awa adzapanga nkondo ndi Mwanawankhosa, ndipo Mwanawankhosa adzawalaka iwo: pakuti iye ali Ambuye wa mbuye, ndi Mfumu ya mafumu: ndipo iwo amene ali ndi iye ali—ali kutchedwa, osankhidwa, ndi okhulupirika.*

*Ndipo iye ananena kwa ine, Madzi amene iwe unawaona, kumene akhalako hule, ali anthu, . . . khamu, . . . mafuko, ndi malirime.*

*. . . nyanga khumi zimene iwe unaziwona pa chirombo, izi zidzadana naye hule, . . .*

<sup>88</sup> Penyani izo tsopano, *nyanga khumi izi*, “maufumu” khumi awa. Onani, kuti chirichonse chikugwera mkati, chimene olamulira mwankhanza awa. Penyani kumene olamulira mwankhanza amatsamirako. Kodi izo zikutsamira kuti? Basi—mungondiiza ine wolamuliramwankhanza yemwe samatsamira cha ku chikominisi. Mwaona? Ndipo iwo adzatani? “Adzadana naye hule,” mkazi, mpingo. Koma chiyani? Penyani chimene chiti chikachite icho.

*. . . awa adzadana naye hule, ndipo adzamupanga iye bwinja ndi wamaliseche, ndipo adzadya thupi lake, ndi kumutentha iye ndi moto.*

<sup>89</sup> Iwo adzachiphulitsa chinthu chimenecho kuchichotsapo pa mapu, basi motsimikiza monga ine ndiri kuyima pano. Ife tikanangokhala nawo nthawi kuti titenge phunziro ilo pamenepo la mpingo umenewo, ndi kuliyendetsa ilo mpaka pansu kupyola mu Lemba, pamene Ilo linati, werengani, “mafumu onse a dziko lapansi ili, ndi eni a ngalawa onse, ndipo onse adzabuma, chifukwa cha Babeloni wamkulu atapezana ndi bwinja lake mu ora.” Ora limodzi, nthawi yake inali itafika! Ndipo, o, momwe iye anati, “Sangalalani, inu ojera, ndi inu nonse aneneri ojera, pakuti Mulungu wabwezera magazi a ojera ndi abale anu pa iye.” Onani, ndiko kulondola. Zedi, chikominisi chikusewera kumene mu manja a Mulungu. Monga ngati Mfumu Nebukadinezara anasewerera kumene mu manja, kuti abwere kudzawatenga Ayuda aja pamene iwo anayenda kupita amaliseche.

<sup>90</sup> Ndipo tchimo likhoza kupitirira kumawononga, mbewu yolungama ikhoza kutsalira mkati mmenemo ndipo mbewu zikhoza kupitirira kumavunda, ndi kumavunda ndi kumavunda mpaka patapita kanthawi iyo nkutha. Izo zikufika pa malo chifukwa amayi awo ndi abambo ndi ena otero akhala chotero patsogolo pa ife, ndipo—ndipo kuyipa kumeneko, palibe kanthu katsalira kwa ife. Ndipo kodi inu mukudziwa chimene Yesu ananena? Ngati Iye akanapanda kuidula ntchitoyo mofupika, sipakanakhala ngakhale mnofu uliwonse ukanapulumsidwa.

<sup>91</sup> Kodi inu mukukhoza kuona, kodi inu mukukhoza kuona chifukwa ife tiri nawo awa? Ine sindikuchitira ndemanga. Ma Arthur Godfrey ndi aliyense, inu mukudziwa, kukhala Elvis Presley, ndi—ndi ziwuno mpaka pansu ndi maovololo, ndi tsitsi likugwera pansu pa makosi awo, ndi njira zonse izi zimene a zaka zongopitirira khumi akuchitira. Nchiyani chikuchita izo? Ndi chiyani icho? Chifukwa izo zikubwera kuchokera ku gulu



la amene anakhalapo-mmbuyo, anthu apathengo. Palibe kanthu katsalira! O, iwo adzayima ndi kuyimba, “Pafupi, Mulungu wanga, kwa Inu,” monga mtola-nyemba Ernie ndi ena onse awo monga choncho, akuyimba nyimbo ya mtundu wina, ndi zina zotero monga choncho. M’bale, inu mukudziwa chiyani? Icho, ndicho mwamtheradi chinyengo. Inde, bwana.

<sup>92</sup> Mwamuna alibe ntchito mu guwa ili amene amapita kunja uko ndi gwedemula ndi kwasakwasa ndi mtundu wonse uwo wa zinthu. Iye alibe chidutswa chimodzi cha ntchito kuseri kuno. Ili ndi la kwa aunsembe, oyitanidwa ndi Mulungu. Atumiki oyitanidwa ndi Mulungu malo awo ndi kuseri kuno. Ndipo sayenera kumbuyo kuno omwe ali onga awo. Ndilo lomwe liri vuto ndi izo lero, iwo awupanga mpingo mosachulukuka kuposa mphanga ina. Mphanga ndi yabwinoko, inu mukafuna kumachita zimenezo, izo ziri kwa inu. Koma ndiroleni inu ndikuwuzeni inu, pali kusiyana kuchulukuka kuti uyesere. . . pakati pa mphanga ndi mpingo. Inde, bwana. Iwe ukafuna kuti uzichita zinthu zimenezo mu mphanga, ndi kumakhala nawo maphwando a mtundu wonsewo ndi zina zotero, izo ziri kwa inu. Koma, m’bale, mpingo uyenera kuti ukhale wosesedwa kuchokera pa guwa njira yonse mpaka ku pansi. Ndiko kulondola. Ine sindikutanthauza kusesedwa ndi mazenera atsopano ndi zina zotero. Ine ndikutanthauza ndi kachitidwe-kachikale, ka chitsitsimutso chotumizidwa ndi Mulungu chimene chiti chidzabalalitse chinthucho kuchokera ku mbali imodzi kupita ku imzake. Inde, bwana. Monga kuyatsa nyali, nyali ya magetsi pa gulu la mphemvu zitazungulira chisononkho cha apulo. Inde, bwana, izo zimamwazikana pamene kuwala kufalikira.

<sup>93</sup> Tsopano penyani, “Iwo ali nawo mtima umodzi, akupereka mphamvu zawo.” Ine ndiri pansi pa izo tsopano. “Nyanga khumi.” Inde, tsopano.

*Pakuti Mulungu wayika mu mitima yawo kuti akakwaniritse chifuniro chake, (apo inu mukupita), ndi kuti agwirizane, ndi kupereka maufumu awo kwa chirombo, mpakana mawu a Mulungu adzakhala atakwaniritsidwa.*

*Tsopano, ndipo mkazi amene iwe unamuwona ali mzinda wawukulu, umene umalamulira pa mafumu onse a dziko lapansi.*

<sup>94</sup> Tsopano, palibe chifukwa cha kumakankhira mozungulira, ife tikudziwa uwo ndi ufumuwolowezana wa Chikatolika. Palibe chifukwa ayi kuti aliyense. . . Ine—ine ndikukhulupirira izo basi molimba monga ine ndikukhulupirira kuti ine ndalandira Mzimu Woyera. Ine ndikukhulupirira izo mwabwino basi monga ine ndikukhulupirira kuti ine ndine Mkristu nditayima pano lero, kuti ufumuwolowezana wa Chikatolika umenewo ndiwo—

m...Mzinda wa Vatikani ndiwo—mzinda umene ukukhala pa mapiri asanu ndi awiri. Ufumuwolowezana wa mpingo ndiwo chirombo chimene chinaliko, chimene kulibe, ndi iwo ndiwo Babeloni. Uli chirichonse chitajambulidwa chimodzimodzi basi, mwangwiro basi njira yonse kupyola mu Malemba, ndi mpingo wa Katolika.

<sup>95</sup> Tsopano, tsopano pano pali nsonga yanu yonjenjemeretsa. Inu mukuti, “Chabwino, inu simukundigunda ine, M’bale Branham.” Koma ndiroleni ine ndikufunsi inu chabe chinachake. Tiyezi tipite mmbuyo momwe tsopano ku ndime ya 5.

*Ndipo pa mutu wake panali...patalembedwa,  
CHINSINSI, BABELONI WAMKULU, MAYI WA  
ZOTEMBEREREDWA, MAYI WA TIMAHULE NDI  
ZOTEMBEREREDWA ZA DZIKO LAPANSI.*

<sup>96</sup> Kodi iye anali chiyani? H-u-l-e. Ndipo iye anali m-a-y-i. Chiyani? M-a-y-i, iye anali atabala chinachake. Mayi wa ana aamuna? Wa timahule! Kahule ndi chiyani? Chinthu chomwecho ngati h—ngati hule, mkazi wopanda khalidwe. Nchiyani chinamupanga iye kukhala wopanda khalidwe? Chiphunzitso chake. Iye anali kunyengezera kukhala mpingo wa Chikristu, koma anali akupereka mbalume zopangidwa ndi anthu. Ndipo pano iye ananena kuti iye anali...Ngati iye anali bungwe loyamba, ndiye izo zikuwoneka ngati pali mabungwe ena atuluka kuchokera mwa iye. Iye anali mayi wa timahule. Ndi kulondola uko? Mayi wa timahule. Sakanakhoza kukhala mayi tsopano wa anyamata. Sakanakhoza kukhala mayi wa... Iye anayenera kukhala mayi wa akazi. Ndipo, ngati iwo anali akazi, iwo anali mpingo. Tsopano tiyezi tifufuze. Chimene chinatuluka mwa...

<sup>97</sup> Bungwe loyamba linali chiyani? Mpingo wa Katolika. Bungwe lachiwiri linali chiyani? Luterana. Bungwe lachitatu linali chiyani? Zwingli. Ilo linafika mpaka ku chiyani? Kalvini. Ndiyeno ilo linafika mu Anglikani, ndipo Anglikani kupitirira mpaka ku Amethodisti. Amethodisti, kodi Amethodisti anabala chiyani? Kuchokera pamenepo panabwera Alexander Campbell. Ndipo kuchokera mwa Alexander Campbell kunabwera John Smith; kuchokera mwa Alexander Campbell kunali mpingo wa Chikristu, ndiye iwo anali nayo inai kapena isanu ya Mpingo wa Khristu ndi timalingaliro tating’ono tonse ito tinatulukira kunjani. Ndiye apa pakubwera mpingo wa Baptisti, iwo unali nazo zochulukira za zazing’ono zotulukira kunjani. Ndipo kuchokera mu mpingo wa Methodisti kukubwera—kuchokera mwa mpingo wa Methodisti kukubwera, kukubwera poyamba, Amethodisti Achiwesile, ndiye iwo anaphwasukana nthawi zinai kapena zisanu. Ndiye iwo anabwera ku mtundu wina wa Methodisti, ndiyeno iwo kuchokamo kachiwiri, ndiye iwo anabwera ku Free Methodisti. Ndipo—ndiyeno iwo anabwera

kuchokera kumeneko ku Nazerini. Ndipo kuchokera ku Nazerini kupita ku Pilgrim Holiness, ndipo Pilgrim Holiness kupitirira mmusi. Timalingaliro tating'ono basi tikutulukira kunja munga choncho, kukhala akumatulukirabe mopitirira mmusi, limodzi lirilonse la iwo aang'ono—toyambitsa tating'ono mmbuyo umo anabwera mopitirira mmusi. Ndipo kodi limodzi lirilonse la iwo linachita chiyani? Iwo potsiriza anatsirizira mu Pentekoste.

<sup>98</sup> Ndipo kodi Pentekoste inachita chiyani? Chinthu chomwecho chimene mayi wawo anachita, iwo anapita mmbuyo momwe ndipo anapanga bungwe. Ndipo kodi ilo linakhala chiyani? Chi—chipembedzo. Yendani mulowe mu chimodzi; chinthu choyamba, “Chiphunzitso chanu nchiyani?” Mnyamata, iwo amakupesa iwe ndi chipesu cha mano-abwino, mwaona, kuti apeze chimene iwe uli, chimene iwe unakhulupirira. Ndipo ngati iwe sugwirizana nawo chabe iwo molondola, m'bale, iwe wachotsedwa pakali pano. Ndipo ndiko kulondola.

<sup>99</sup> Ndipo musati muganize basi chifukwa inu mukuti ndinu wa Chipentekoste kuti ndinu wotetezeka. M'bale, adzakhala alipo basi Achipentekoste ambiri ochoka pa msewu munga amene ali pa msewu, ine ndikutsimikiza. Mwaona?

<sup>100</sup> Tsopano, mabungwe onse awo, ngati iwo akanangosiya dalitso la Pentekoste ilo lizipita, osalipanga bungwe ilo, kungolisunga ilo mu ubale ndi kulola Mzimu Woyera kuti uchite tsankholo. Mzimu Woyera umasankha. Anania, Safira anabwera mkati nthawi yina, ananena *zakuti-ndi-zakuti*, ndipo Mzimu Woyera unati, “Nchifukwa chiyani iwe unanama?”

<sup>101</sup> Koma ife timati, “Tsopano, ameneyo ndi M'bale Yonasi, musati muyankhule kanthu koyipa kokhudza iye tsopano, iye ndi wolipira bwino kwambiri yemwe ife tiri naye mu mpingo. Ine ndikudziwa kuti iye ali nawo Mzimu Woyera, ine ndinamumva iye akuyankhula mu malirime ndipo ine ndamuwonapo iye akufuula mu Mzimu.” Izo ziribe kuchulukira koposa kutsanulira nandolo pa chikopa chowuma cha ng'ombe. Mukuona? Palibe chinthu chochita nacho icho. Mulungu amachita kunenako. Iye ayenera kunena ngati iye ali kapena iye sali. Mwamtheradi. “Koma ife timatengera izo ku chipembedzo chathu. Koma ife tinamuthamangitsira iye kunja kwa—kunjwa kwa Assemblies, Aumodzi anamutenga iye.” Aumodzi akumutenga iye kwa kanthawi, ndiye iwo amukankhira iye kunjwa chifukwa... Iwo akumutenga iye kupita uko ndipo a Yesu Yekha amutola iye. A Yesu Yekha amunyamula iye kwa kanthawi, ndiyeno chinthu chotsatira chimene kumutenga iye ndi Mpingo wa Mulungu, kumutola iye. Mpingo wa Mulungu wa Uneneri ukumutenga iye, ndipo kachitidwe ka Tomlinson kamutenga iye. O, mai! M'bale, ngati ife sitinathe! Ndimo mu Pentekoste, chitsitsimutso chotsiriza. Ndipo tsopano iwo ali nako kuchuka kwa buluu, ndipo iwo ali nawo opembedza mafuta, ndi ma—ndi magazi mu

nkhope. Ndipo, o, chifundo, ine sindikudziwa kumene iwo apita tsopano. Chinthu chimodzi chabe chimene. . .

<sup>102</sup> Chinthu chonsecho chakhala chovunditsidwa. Kodi inu mumadziwa kuti Baibulo linanena kuti izo zidzafika povunditsidwa? Kodi inu mumadziwa kuti—kuti Baibulo limanena kuti tsiku lino lidzakhala pano, pamene ngakhale magome a Ambuye adzakhala odzaza ndi masanzi? Ndipo anati, “Ndi ndani yemwe Ine ndingakhoze kumuphunzitsa Chiphunzitso? Ndi yani yemwe Ine ndingakhoze kumupanga kuti andimvetse Ine? Pakuti lemba liyenera kukhala pa lemba pa lemba, pa mzere pa mzere.” Ndi ndani yemwe Iye angakhoze kumuphunzitsa Chiphunzitso? Iwo amene atengedwa kuchokera pa maere, amayi. Mukuona?

<sup>103</sup> Tsopano, muno mulibe—muno mulibe mkazi, mkazi wauthakati mu tawoni yino koma yemwe angakhoze kubala mwanawamkazi waunamwali. Iye ali pamene iye abadwa. Tsopano, ndipo iye akhoza kupita bwino. Koma ngati inu simuzindikira kuti mayi ake akhala a chikhalidwe chimenecho, msungwana ameneyo, nthawi zisanu ndi zinai pa khumi, adzachita chimodzimodzi basi monga mayi ake amachitira. Tsopano, inu mukudziwa kuti ndiko kulondola. Mkazi wachikulire amene amapita ku nyumba ya a mbiri yoyipa, akhoza kubala msungwana wamng’ono, ndipo iye akhoza kukhala usinkhu wa zaka khumi ndi zisanu ndi chimodzi, basi woyera ndi wakhalidwe monga wamoyo aliyense, koma, ngati iye akhalabe mwa njira imeneyo. Koma, chinthu cha icho chiri, iye amabwerera mmbuyo ndi kumachita monga mayi ake.

<sup>104</sup> Tsopano, mpingo wa Katolika unali wachiwerere wakale woyamba yemwe anatulukirapo ndi ziphunzitso zimene iye anadzipangira yekha, zamatsenga, zomwe, Baibulo linati, “Iye anabwera kuchokera ku phompho lopandamalire ndipo adzapita kubwerera ku chitayiko.” Baibulo linanena zimenezo. Tsopano, iwo amaphunzitsa kuti ndiko kulakwitsa. Ndi kulakwitsa malingana ndi Mawu a Mulungu. Ndiyeno pano pakubwera mpingo wa Methodisti umene unabadwa kuchokera mwa iwo, dona wamng’ono wokongola, koma kodi iye anachita chiyani? Iye anapotokera mmbuyo momwe ndi kuchita zinthu zomwezo zimene mayi ake amachita. Kulola osonkhana ake kumavala akabudula, kuwalola iwo kusuta ndudu, kuwalola iwo kumapitiriza ndi kumangochita monga ngati iwo ayenera. Palibe kanthu kakunenedwa za izo. M’busa wachikale wamng’ono wophikidwa mwatheka mmbuyo kuseri uko, kuguwa kumbuyo uko, akuchita mantha kuti iye malipiro adzamuthera tsiku lina, kapena chiwaya cha masikono.

<sup>105</sup> Ndiroleni ine ndikuuzeni inu, m’bale, ine kunalibwino ndizilalikirira Uthenga, ndi kumadya zikondamoyo ndi kumwa madzi a mngalande, ndi kumanena Choonadi za iwo. Ngati

aliyense wa osonkhana anga akadayima ndi kuyenda kutuluka, ngati ine ndawauza iwo Choonadi. Inde, indedi.

<sup>106</sup> Chavuta ndi chiyani? O, ndi chiphatso cha zakudya. “Chabwino, inu mukudziwa, ndine m’busa wa mpingo wawukulu kwambiri umene ulipo mu mzinda.” Inu Abaptisti ndi Amethodisti, kumamvetsera kwa mneneri wabodza. Tsopano, ndizo zamwano, koma chirichonse chimene chimaphunzitsa mosiyana kwa Baibulo ili ndi mneneri wabodza. Ine sindikusamala kaya izo zikhala zopukutidwa motani, ndi uneneri wabodza. Ndiko kulondola.

<sup>107</sup> “O, chirichonse chiri bwino bola ngati inu muli nalo dzina lanu pa buku.” Inu mukhoza kukhala nalo dzina lanu pa mabuku dazeni; ngati ilo palibe pa Buku la Moyo, inu mwatayika! Inu mukhoza kukhala nthawizonse wabwino, inu mukhoza kukhala womvera basi ndi woyera ndi wamakhalidwe monga inu mungakhoze kukhalira, izo sizidzakhala ndi chinthu chimodzi choti nkuchita ndi izo.

<sup>108</sup> Esau anali pawiri mnyamata yemwe Yakobo anali, pamene izo zifika pakukhala mamuna, kuwasamalira abambo ake okalamba osapenya ndi china chirichonse. Ndipo Yakobo anali shasha pang’ono wokanirira pafupi ndi chilolo cha amayi ake, mnyamata wamng’ono wachikazi. Koma Mulungu anati, “Ine ndamukonda Yakobo ndipo ndamukana Esau,” mnyamata aliyenseyo ali asanabadwe. Aroma 8 amanena choncho. Ndiko kulondola chimodzimodzi.

<sup>109</sup> Mulungu amadziwa chimene chiri mwa munthu. Ndipo Iye amadziwa chimene chiri mu mpingo, naponso. Ife timakhala moyo ndi Mkate wa Moyo, Mkate wa Mawu a Mulungu. Tsopano, ndicho chifukwa ife sitiri chipembedzo.

<sup>110</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti ndikupatseni inu kena kakang’ono...Ine ndikufuna ndikupatseni inu kufotokoza kwakung’ono kumene ine ndinachilemba apa. “Wamkulu...” Tsopano mu Chivumbulutso, mu 19:2, ine ndiri ndi chinachake ndasonyeza apa, ine ndikufuna kuyang’anapo ndi kupenya chimene icho chiri tsopano.

*Pakuti choona ndi cholungama chiri chiweruzo chanu: pakuti iye waweruza hule lalikulu, limene linavunditsa dziko lapansi ndi ziwerewere zake, ndipo wabwezera magazi a antchito ake pa dzanja lake. Ndiko kutha kwa mpingo wa Katolika.*

<sup>111</sup> Tsopano, ife panonso tikufuna kuti inu muzindikire, ndiponso pano, kuti chipembedzo, kuti chipembedzo chirinso kupezeka mu Malemba apa, kuti...Ndipo Baibulo silimayankhula konse za chipembedzo. Chipembedzo chinabwera kuchokera ku mpingo wa Katolika. Iye ali mayi woyamba wa chipembedzo ndipo chipembedzo chirichonse chabwera choncho mpaka pansu. Tsopano, izi zikhala chabe

zotsina pang’ono, izo zizikhala zotsinirabe pang’ono nthawi yonse, onani. Koma ine—ine ndikufuna inu kuti muwone kuti zipembedzo sizinabadwe kapena kudzozedwa ndi Mulungu, izo zinadzozedwa ndi Mdierekezi. Mpingo wa Mulungu uli . . .

<sup>112</sup> Ife sitiri ogawanika, tonse thupi limodzi ife; chiyembekezo chimodzi ndi Chiphunzitso, amodzi mu chikondi. Ndiwo Mpingo wa Mulungu wamoyo. Mosasamala chimene iwo, zinthu zimenezo, ife tiri amodzi palimodzi! Ndiko kulondola. Kaya iye ndi wa Methodisti kapena Baptisti, m’bale, ngati iye ali wobadwa kachiwiri ndi wodzazidwa nawo Mzimu Woyera, iye ndi m’bale wanga, ife tikuyenda phewa kwa phewa. Kulondola. Inde, bwana. Sizipanga kusiyana kulikonse.

<sup>113</sup> Mose. Nthawizina mwina akhoza kumayang’ana pozungulira ndi kunena, “Inu mukudziwa gulu lija la Achipentekoste otentheka, M’bale Branham, inu mumapitiranji konse kwa gulu monga limenelo?” Inu mukudziwa chiyani? Mose anayang’ana pa ana a Israeli, iye anayang’ana kunja kuchokera pa zenera lomwelo limene Farao anayang’anirapo kunja. Farao anayang’ana pa iwo monga gulu la oponda-matope, koma Mose anayang’ana panja pa iwo ngati osankhidwa a Mulungu. Iye anadziwa kuti iwo anali nalo lonjezo. Chifukwa chiyani? Iye anadziwa izo mwa Mawu. Ndipo mwa chikhulupiriro . . . Pamene iye anayikidwa pa mpandowachifumu kuti akhale Farao, ndi dziko lonse likugona pa mapazi ake, atakhala pamenepo ndi kumatsanulira vinyo mkamwa mwake, ndipo akazi okongola akumukupizira iye, monga mfumu, kapena wolamuliramwankhanza, kapena mfumu ya dziko, Mose wamng’ono pa usinkhu wa zaka makumi anai, anali nawo mu dzanja lake, pamene iye anayang’ana panja pa gulu la oponda-matope ilo; koma iye anadziwa kuti iye anali mmodzi wa iwo. Aleluya! Ndi zimenezotu. Iye anadziwa kuti iye anali mmodzi wa iwo. Ndipo mwa chikhulupiriro, chokha, iye anasankha!

<sup>114</sup> Aliyense ayenera kupanga kusankha. Inu muyenera kupanga kusankha. Inu muyenera kupanga kusankha tsopano. Inu muyenera kupanga kusankha mmawa. Inu muyenera kupanga kusankha mawa usiku, ngati inu mutakhale moyo. Iwe umayenera kusankha nthawizina. M’bale, nthawi yaitali kalelo ine ndinasankha; Baibulo ili linali dikishonare langa, Baibulo ili linali Bukhu langa la Moyo, Baibulo ili linali Mawu a Mulungu. Baibulo ili ndi limene ine ndimakhala nalo moyo. Baibulo ili liri chimene ine ndikuyima nacho.

<sup>115</sup> Chotero Mose anayang’ana kunja pa ana a Israeli, ndipo osati kokha kuti iye anati, “O, iwo ndi anthu odabwitsa. Ine ndiribe kanthu kowatsutsa iwo. O, ayi, ine sindingayankhule mawu amodzi mowatsutsa iwo.” Ndimo momwe anthu ambiri amachitira lero. “O, Achipentekoste awo ndi anthu awo amene ali nawo Mzimu Woyera, ndi anthu awo amene amakhulupirira mu machiritso Auzimu, o, ine—ine—ine ndiribe kanthu kotsutsa

izo.” Koma ameneyo sanali Mose. Iye anakana Igupto ndipo anakhala mmodzi wa iwo, iye anapita panja pakati pa abale ake. Iye anali mmodzi wa iwo.

<sup>116</sup> M’bale, apo ndi pamene ine ndikutengera njira yanga. Ine nditenga njira ndi onyozeka apang’ono a Ambuye, ngati iwo alipo odzaza dzanja kapena chirichonse chimene chiri. Iwo ali nalo lonjezo, ndipo ine ndikuwona maina awo mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Iwo ndi abale anga. Ndiko kulondola. Tengani kusankha kwanu ndi kuyima ndi iwo. Cholondola kapena cholakwika, kuyima pamene mulimonse. Ngati iwo akulakwitsa, athandizireni iwo ku cholondola. Kulondola. Iwe sumawapanga iwo abwino mulimonse pa kuwakankha iwo mozungulitsa. Mwaona, yeserani kuwakoka iwo achokemo.

<sup>117</sup> Charlie, monga iwo ananena zokhudza M’bale Allen, zokhudza moto umene iwo...magazi mu manja. Ine ndinati, “Palibe, palibe pamene ine ndinamunyozapo A. A. Allen.” Ine ndinati, “Ngati ine ndikanakhoza kumalalikira monga A. A. Allen ine sindikanamakhala konse ndi utumiki wa machiritso.” Tsopano, pamene izo zifika pa kusagwirizana pa za magazi ngati kukhala umboni wa Mzimu Woyera, mu manja mwako, ine sindigwirizana nazo zimenezo. Koma pamene izo zifika pa ubale, iye ndi m’bale wanga. Ine ndimayima phewa kwa phewa ndi iye mu nkondo. Ndiko kulondola. Ngati iye akulakwitsa, ine ndiyesera kuti ndimuthandize iye. Ndipo ngati iye sali kulakwitsa, ngati ine ndiri kulakwitsa, ine ndikufuna iye kuti andithandize ine. Ndipo umo ndi momwe ife titatengere izo, kumapitirira limodzi. Tsopano penyani apa.

...iye anali *CHINSINSI, BABELONI...MAYI WA TIMAHULE...*

<sup>118</sup> Tsopano kodi inu mukuona momwe mpingo lero, amzanga, kodi inu mungakhoze kuwona momwe mipingo iyi lero momwe ikungokhala mulimonse momwe iyo ikufunira kuti azikhala? “Zabwino mwanngwiro, kumapitirira basi patsogolo,” nkhumba kudya nkhumba, osalabira ayi. “Bwanji, palibe chovulaza mu kuchita zimenezo. Bwanji, inu mungoyesera kuti mukhale wa kachitidwe kachikale.” Tsopano penyani chiphunzitsa chawo. Tsopano ine ndikufuna... Tsopano penyani. Ndicho chizolowezi chawo. Kodi inu mukuona kuti zaka pang’ono zapitazo kuti mpingo wa Katolika unali umodzi wokha umene unali kulolezedwa kuti azipita ku chiwonetsero cha zithunzi? Mpingo wa Methodisti sukanaganizira za chinthu choterocho, ndi zipembedzo zonse izo, “Ayi, izo ndi ntchito za Mdierekezi.” Chabwino, ine ndikudabwa chimene chinachitika. Inde, bwana.

<sup>119</sup> Ndipo inu mukudziwa, inu mukhoza kuwatenga asungwana aang’ono Achikatolika awo, iwo amatuluka kunja ndi zazing’ono izi... (Tsopano, ena a inu anyamata achikulire muli aakulu monga ine ndiriri)...kutuluka ndi kupita ku chinthu

chaching’ono ichi kumene iwo anali nazo zolekezera mmaondo. Mnyamata uja, ine ndikulingalira, ali mu gehena usikuuno. Ine sindikudziwa, ine sindiri womuweruza wake. Koma pamene iye anapanga nyimbo yoyamba yauve ija imene inazembera pa wailesi, popanda kupimidwa, ija ya “Funyululani izo, asungwana, funyululirani izo; funyululirani izo mmusi ndi kuwonetsa maondo anu okongola.” Ndi angati akuyikumbukira imeneyo pamene poyamba iyo inatuluka zaka zapitazo? Uko kunali kupulumuka koyamba apo pomwe. Ndiko kulondola. Ndipo pamene iwo anamutenga mnyamata uyu wochokera ku Texas, ndi kuwatengera akazi awo kunja kumeneko ndi kumagwiritsa ntchito zovala zamkati izo kuti awapange iwo kuti aziwoneka monga ngati iwo anali chinachake chimene iwo sanali, ndi zinthu zotero monga izo, ndi kuwalola iwo kuti azipitirira nazo zimenezo. Ndipo tsopano kodi iwo akuchita chiyani? Izo zinamka zikukwawira mkati. Ndi mzimu.

<sup>120</sup> Bambo anali kuyankhula kwa ine tsiku lina, iye anati, “Ine sindikudziwa chomwe ine nditi ndichite. Ine ndinali naye mnyamata wabwino woonamtima, ndipo mnyamata ameneyo akufika pakati iye akutenga zimene iye akuyikapo manja ake.”

Ine ndinati, “Chifukwa chiyani?”

“Iye akuyanjana ndi mbava.”

<sup>121</sup> Iwe ukamadzipachika pafupi ndi winawake yemwe ali mbava, iwe udzakhala mbava iwe mwini. Mayi anga okalamba achi Kentucky anakonda kuti, “Ngati iwe ugoni pansi ndi garu yemwe ali ndi utitiri, iwe utenga utitiri, nawenso.” Inu mumutenge—inu mumutenge mkazi yemwe asali wabwino, ndi kumulola msungwana, ndi kumuyika iye ndi—mnyamata wabwino wakhalidwe, ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa iye ali wauve monga mwana wa garu. Mutembenezire izo mosinthanitsa. Iwe umadziwika ndi gulu lako. Dzipatuleni nokha! “Tulukani muchoke pakati pa iwo,” linatero Baibulo, “khalani inu olekanitsidwa!” Ndiko kulondola.

<sup>122</sup> Ngati zipembedzo zawo zikupita mmbuyo ku chivundi choterocho monga kuwalola anthu awo... Chabwino, kuno tsiku lina, mpingo wawukulu bwino wa Chibaptisti, iwo anachita kulekeza. Kutu alalikira maminiti makumi awiri okha, mwamunayo amayenera, chifukwa abusa amayenera kuti akasute. Osonkhana onse anapita panja. Onse a iwo anyaima panja apo mu mizere yosuta, ndi kubwerera kachiwiri, abusa ndi onse a iwo. Ine ndinapita ku Mpingo wa Osonkhana, kumeneko mwamuna anakhala, atavala mwinjiro wawukulu wautali, atayima pamenepo, anati, atatsamira pa guwa monga *chonchi*, akuyankhula zokhudza mtundu wina wa duwa umene iye anawupeza pa phiri. Ndizo zokhudza zonse zimene zinali kwa izo. Ndipo anabwerera kukhala pansu, ndipo zala zake zinali zachikasuni ndi utsi wa ndudu. Inde. Ndipo kuyankhula



zokhudza kuti akazi, kuti amuna anali kupita kuti akasewere . . . Kodi ndi sewero lanji la Chijermani ili limene iwo amasewera ndi izo, mochuluka kwambiri iwe—iwe umachita ndi makadi, inu mukudziwa? Ilo linali . . . O, ine ndimaganiza kuti ine ndilikumbukira ilo. Nokonoko, iwo amati akhale ndi sewero la nokonoko. Ine ndikuganiza kuti—kuti ndi pamene iwe umachita, ndiko kusewera ndi makadi osewera nawo wamba. Masewero a nokonoko mu chipinda cha pansi. Mai, ubwino! Ndiko kumene maziko ake ali. Palibe zodabwitsa! Amachitira chiyani izo, ndiyeno nkumafuula zokhudza mpingo wa Katolika kunjira kuno pa malo wachiona ndani awa ndi kumasewera wachiona ndani. Bwanji, inu Achiprotetanti muli basi auve monga iwo aliri, kotero inu mungakhoze kunena chiyani zokhudza izo? M'phika sungakhoze kunena ketulo “yakuda.” Ndithudi ayi. Ndipo inu mumachita, ndi kuti, iwo anganene, “Chabwino, ndine wa Presbateria. Ndine wa Methodisti.” Sindinu kanthu mpaka inu mutabadwa kachiwiri. Ndiko kulondola. Ndipo pamene inu mukuchita zimenezo, inu mukudziwa kuti pali chinachake mkati mwa ine chimakuuzani inu zinthu zimenezo ndi zolakwika, ndipo inu mutulukamo mu izo motsimikiza basi monga inu muli olekeza mu mawondo kwa bakha. Inu mukudziwa izo ndi zoono. Ndithudi. Inde, bwana. Chinthu chimenecho chikumka mopitirira mmenemo, bwanji?

. . . *MAYI WA TIMAHULE* . . .

<sup>123</sup> Limodzi la masiku awa mayi wachikulire adzati, “Inu mukudziwa chiyani? Zitachitika zonsezi, wokonedwa, ife tonse ndife ofanana.” Ndipo inu mukudziwa chimene icho chiri ndiye? Chitaganya cha Mipingo yonse kuti ipite ku chiyanjano limodzi monga iwo aliri tsopano. Ndipo inu mukudziwa chimene chiti chidzachitike kwa gulu laling'ono monga ili? Inu mudzalipira chifukwa cha zimenezo, ambwana. Ndiko kulondola chimodzimodzi.

<sup>124</sup> Koma musati mudandaule, Mwanawankhosa adzamulaka iye! Pakuti Iye ali Ambuye wa mbuye ndi Mfumu ya mafumu, ndipo Mulungu adzapita kuti akatsogolere mpingo Wake, mmalo mwa chipembedzo. Iye adzatsanulira Mafuta a golide awo a Mzimu Woyera pa mpingo umenewo, m'bale, Moto udzagwa kuchokera Kumwamba, ndi zizindikiro ndipo zodabwitsa zidzachitika monga zimene inu simunayambe mwaziwonapo kale. Inde, bwana. “Musawope ayi, nkhosa zapang'ono, ndi chifuniro chabwino cha Atate anu kuti akupatseni inu Ufumu.” Inde, bwana. “Iye amene apirira mpaka ku mapeto!” Apo inu mukupita. Sungani kolondola popita mu msewuwo, sungani mutu wanu choloza ku Kalvare. Baibulo ili liri kulondola. Musati mudandaule.

<sup>125</sup> Tsopano penyani, pali zina za zizolowezi zimene iwo ali nazo. Ena a makhalidwe amene iwo ali nawo. Ife tikhoza kumangopitirizabe. Chinthu choyamba inu mukudziwa, izo

zinawukhira kupita mu mipingo ya Chiprotestanti. Ndiye akazi Achikatolika anayamba ku. . . “Bwanji, izo sizinali zoyipa kuvala akabudula aang’ono, malingana ngati iwe umapita ku tchalitchi ndi kuyika mpango pa mitu yawo.” Mtundu wina wa mwambo. “Kusadya nyama iliyonse pa Lachisanu.” Ndipo, o, nkuti kumene inu munayamba mwapezapo kuyika mpango pa mutu wako polowa mu tchalitchi? Ine ndikufuna inu kuti mundisonyeze ine Lemba. Ndiwo uneneri wabodza. Izo ziri pati mu tchalitchi kuti iwe umayenera kuti uzivala chipewa mu tchalitchi? Pamene iwe uvala chipewa pa mutu wako, iwe umanyozetsa Khristu, ndiko kulondola; amuna, ndi omwe ine ndikukamba za iwo. Akazi, inu muli nacho chophimba, koma ine nditsutsa aliyense kuti andisonyeze ine pamene ziri chipewa kapena mpango. Ndi tsitsi lanu! Ndipo inu mwalidulamo ilo lonse. Tsopano bwanji za izo? O, iwo amati, “Ndiko kachitidwe kachikale.” Ngati iko kali, ndi Baibulo! Mawu a Mulungu ndi olondola.

<sup>126</sup> Kuyankhula kuno osati kale litali za mkazi yemwe anatsuka mapazi a Yesu, ndipo anatenga tsitsi lake, inu mukudziwa, ndipo—ndipo anawapukuta iwo ndi ilo. Ine ndinati, “Njira yokha imene mkazi akanakhoza kuti achitire zimenezo, ili kuyima pa mutu wake kuti apeze tsitsi lokwanira pansi apo kuti atsukire mapazi Ake ndi kuwapukuta iwo.” Ndiko kulondola. O, icho—ndi—ndi chamanyazi kuwona momwe. . . Kuno, nyengo ya chisanu, akuyenda pozungulira atavala chikhoto chachabechabe chaching’ono monga choncho, ndipo thupi lawo lamaliseche likuwonekera.

<sup>127</sup> Bwanji, mukuti, “Nchifukwa chiyani inu mukuwatola akazi?” Inu mukusowa kuti mutoledwe.

<sup>128</sup> Ndipo inu amuna amene mumawalola akazi anu kumachita zimenezo, m’bale, ine—ine sindikudziwa choti nkuganiza za inu. Tsopano, ndiko kulondola.

<sup>129</sup> Ndipo inu azibusa, ine sindikulingalira kuti inu muli pano. Koma ngati inu mumuwona munthuyo, inu mumuuzeye iye kuti abwere, adzandiwone ine. Mwaona? Ngati iye alibe kulemekeza kwinanso kwa Khristu kopusu kuwalola osonkhana ake kuyanjana ndi izo popanda. . . Tsopano iye. . . Iwo akhoza kumachita izo kunjira uko kuseri kwa iye, koma ngati iye sakuwawuza iwo zokhudza izo, iye sali wantchito wokwanira wa Yesu Khristu. Ndiko kulondola chimodzimidzi. Iye sali wokwanira kuti akhale wantchito wa Khristu. Wantchito wa Khristu ayenera kuti akhale wopanda mantha ngati chiri choyambitsa chimene chimabwera ku Baibulo. Ndithudi. Koma apo iwo ali, iwo amapita kunjira ndipo iwo amachita izo mulimonse.

<sup>130</sup> Ndiyeno, chinthu choyamba inu mukudziwa, Achiprotestanti amayenera kutengera icho. Inu Amethodisti

abwino, ndi inu Achibaptisti, ndi inu Achipresbateria ndi Anazerini, Pilgrim Holiness, ndi nonse a inu. Chinthu chomwecho, kupita kunja kumene, zisanu ndi chimodzi kwa mmodzi, ndi theka la dazeni kwa winayo. Pamenepo inu muli, “mayi wa timahule.” Chipembedzo chanu, “Malingana ngati iwo anayambira ku likulu, kodi izo zinapanga kusiyana kotani?” Mwaona? Zimapanga kuchuluka konse kwa kusiyana. Iwo sanayambire konse ku Malikulu *amenewo*. Zikhoza kuyambira ku malikulu anu pansu pano, koma osati Limodzi ilo kumwamba uko. Zimatengera kumene inu mukuchokera. Ndizo zoonza.

<sup>131</sup> Tsopano ine sindikuganiza kuti ife tiri nayo nthawi kuti titenge chimodzi china ichi, mwinamwake ine kulibwino ndizisiyire izi kwa mmawa. Chabwino, tiyeni tingotenga chimodzi chaching’ono chachifupi ichi. Ife tiri nawo pano “ubatizo mu madzi,” ife tiri nakonso “kukonzedweratu,” ndi, o, zinthu zambiri. Kotero tiyeni tingotenga izi, chimodzi chaching’ono chachifupi ichi cha “alaliki aakazi,” ndi kuchitenga chimodzi ichi.

<sup>132</sup> Tsopano, tsopano, mlaliki wachidona, ine sindikufuna kukuvulazani kumverera kwanu, koma ine ndikufuna ndikuuzeni inu chinthu china. Inu mulibe chidutswa chimodzi cha Lemba, palibe chimodzi mu Baibulo. Eya, ine ndikudziwa kumene inu mukupitako, ndipo ine ndakhalapo nazo zonse zanu. . . Eya, “Ndipo ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera.” Tsopano, ngati abusa anu sadziwa chimene dzina lakuti “kunenera” limatanthauza, iwo—iwo sakudziwa, alibe ntchito yochuluka kwambiri kuseri kwa guwa, poyesera kukuuzani inu kuti mukhale mlaliki. Mwaona? Chifukwa izo mwamtheradi, ziri zotsutsidwa kuchokera ku Genesis mpaka Chivumbulutso. Tsopano ndiroleni ine ndikuwonetseni inu pano, onani.

<sup>133</sup> Tsopano ine ndikufuna kuti inu mutembenuze ndi ine ku l Timoteo 2:11. Ingotembenuzani kuno ndipo ife tipeza izi tsopano, ndipo ife tipezanso izo pano, ndiponso Machitidwe 2 anu. Ndipo ingo—ingomvetserani apa chimene Lemba liri nacho kuti linene za phunziro ili.

<sup>134</sup> Tsopano, winawake anapitirira kunena kuti, “Chabwino, M’bale Branham, inu ndi wodana ndi akazi wachikale basi.” Ine sindine wodana ndi akazi ayi. Ine ndine. . . Ine kungoti sindimakonda kuwawona akazi akuyesera kutenga malo amene iwo sayenera mmenemo. Inu mukumbukira ku Bwalo la ngalawa la a Howard cha kuno, amodzi a mabwalo la ngalawa opambana kwambiri amene alipo pa Mtsinje wa Ohio, iwo anamuyika mkazi pamenepo, penyani chimene chinachitika. Iwo amupatsa mkazi ufulu kuti azivota, penyani chimene chinachitika.

<sup>135</sup> Ndiroleni ine ndikuuzeni inu pakali pano. Osati kuti ndiwasende akazi, ine ndikufuna kuti amuna amvetse kuti inu muli mu izi nanunso. Koma ndiroleni ine ndikuwuzeni inu

chinachake, m'bale, fuko ili ndi fuko la mkazi. Ine nditsimikizira zimenezo kwa inu, mwa Lemba, mwa chirichonse chimene inu mukufuna kutsimikizira nacho. Ichi ndicho. Nchiyani chimene chmawoneka pa ndalama yathu? Mkazi. Kodi iye akupezeka pati mu Chivumbulutso umu, inu mwamuwona iye? Iye ali chiwerengero cha khumi ndi zitatu, naponso, chirichonse chimene iye anayambitsa. Nyenyezi khumi ndi zitatu, milozo khumi ndi itatu, zigawo khumi ndi zitatu, khumi ndi zitatu, chirichonse chinali khumi ndi zitatu kuyamba ndi kuyamba. Iye amapezeka mu mutu wa 13 wa Chivumbulutso. Mkazi, khumi ndi zitatu!

<sup>136</sup> Ndipo mu 1933 pamene Ambuye, pamene ife tinali kukhala ndi misonkhano kuno kumene Mpingo wa Khristu uja wayima tsopano, nyumba yakale ya Masonic, masomphenya a Ambuye anabwera kwa ine kuno ndipo ananeneratu kuti, "Germany akanadzawuka ndi kuchita kuyika Mzere wa Maginot uja kumeneko." Ambiri a inu mukukumbukira zimenezo. "Ndi momwe akanati adzalimbikitsidwire onse mmenemo, ndipo Achimereka akanalandira kumenyedwa kwakukulu pamalo omwewo apo pa mzere umenewo. Ndiponso anafotokoza chimene chikanati chidzachitike, ndi zokhudza Roosevelt ndi zinthu zimenezo, momwe iye akanati apikisane ndi kupanga nthawi yachinai ija." Mwangwiro, chimodzimodzi basi momwe izo zinadzachitikira. "Ndiponso ananena kuti magalimoto akanamapitirira kumawoneka mochulukana ngati dzira, mpakana kuti masiku otsiriza iwo akanadzakhala basi mwa mawumbidwe a dzira." Tsopano Iwo anati, "Izo zidzachitika kuti magalimoto amenewo sakanamati azidzayendetsedwa ndi gudumu la chiwongolero, icho chikanadzakhala chinachake chimzake chikuwayendetsa iwo. Ndi magalimoto amenewo amene iwo akuwatulutsa pakali pano, oyendetsedwa ndi mphamvu yakutali, pofuna kutetezeka. Ndiko kukhoza. Iwe siwumadzakhoza kulowa mu mzinda ndiye, chigawo cha mailosi-makumi awiri, iwe udzangokhoza kumapita mailosi makumi awiri. Iwe sungakhoze kugunda galimoto lina, chifukwa ndi yoyendetsedwa zolamulidwira kutali. Mukuona, izo zikuyenda monga choncho pakali pano. Ndipo ine ndinati, "Kumbukirani, mu tsiku limenelo, nthawi ya mapeto isanafike, nthawi yotsiriza isanafike, kuti mkazi. . . Tsopano, inu nonse musunge izi zitalembedwa. Kudzakhala kuli mkazi wamphamvu kwambiri ati adzawuke, mwina adzakhala Purezidenti, kapena wolamuliramwankhanza, kapena mkazi wina wamphamvu kwambiri mu United States uyu. Ndipo iye adzamiza pansu pa chikopa cha akazi. Tsopano, inu muzikumbukira, ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE."

<sup>137</sup> Onani, ndipo iye akulakwitsa. Ndipo kodi iye wadzipereka yekha ku chiyani? Ndiroleni ine ndikuuzeni inu. Khalani auzimu, tsegukani, penyani. Nchifukwa chiyani akuchita

zimenezo? Kuti awupatse mpingo wa Katolika malo kuti ubwere mkati. Mwaona? Inu mumapembedza ochita pa kanema awa ndi zinthu zina zonse zosiyana izi apa. Mukukumbukira ulaliki umene ine ndinalalikira? Margie, iwe ukukumbukira, zaka zapitazo pa—kuwukiridwa kwa United States ndi kulandidwa kwa Boma la Chimereka. Ndipo momwe ine ndinati iye anawuka mu Paris titatha kuwapulumutsa iwo kumeneko kuchokera kwa akazi aja, vinyo ndi nthawi yayikulu, ndipo iye anakayatsa mpaka mu Hollywood momwe. Tsopano mmalo moti ife tiwatumize ku Paris kuti akatenge okopa malonda, iwo amawatumiza kuno kuti adzatenge okopa malonda. Kodi nchiani chinachita izo? Izo zinayamba. . .Ife sitikanakhoza kuwalola ana anu kuti azipita ku chiwonetsero cha kanema, koma izo zinafika mpaka mu televizioni, zasunthira mopitirirabe kunja ndipo zavunditsa chinthu chonsecho, kumuthamangitsira iye mopitirira kunja. Ndipo pano ife tiri lero asungwana onse aang’ono ndi anyamata onse monga mtundu wina wa ochita pa televizioni awa. Ndi chiyani icho? Ndiko kukonza njira. Mnyamata, mkazi mmodzi wa mbiri-yoyipa akhoza kutumiza anthu ochulukirapo ku gehena kuposa malo onse ogulitsirako mowa amene inu mungakhoze kuwayika mu mzinda. Ndiko kulondola. Mpenyeni iye akupita pansu mu msewu ndi zovala zake zonse atazivulira pansu, sindikusamala yemwe mwamunayo ali, ngati iye ali mwamuna wathanzi mwabwino, pamene iye ayang’ana pa mkazi iye ali wokakamizidwa kukhala nacho chinachake chikudutsa pa iye. Tsopano ingokhalani woona mtima. Ine sindikusamala.

<sup>138</sup> Ine ndakhala nawo Mzimu Woyera kwa zaka. Iwe sungakhoze kuyang’ana pa mkazi ndipo iye atavala mwatheka. . .ine—ine ndimanyamula mtanda wawung’ono mu galimoto yanga, ambiri a inu munawuona iwo. Winawake ananena kwa ine, “Kodi ndinu Mkatolika?” Akatolika anapezera kuti gawo pa mtanda? *Mtanda* umatanthauza “Chikhristu.”

<sup>139</sup> A Cicilia Oyera aang’ono akale awo ndi zinthuzo ndizo chilemba cha Chikatolika. Ife sitimakhulupirira mu zinthu zotero monga zimenezo. Ife timakhulupirira mwa Khristu. Iwo ali nayo mitundu yonse ya anthu akufa amene iwo amawapembedza. Ndi mawonekedwe apamwamba a zamizimu. Ndizo zonse zimene izo ziri, kupembedza akufa. Palibe chinthu choterocho, ayi.

<sup>140</sup> Ine ndinamufunsa wansembe ameneyo, ine ndinati, “Bwanji ndiye—ndiye ngati. . .Petro anali Papa woyamba?”

Iye anati, “Ndiko kulondola.”

<sup>141</sup> Ine ndinati, “Ndiye nchifukwa chiyani Petro anati, ‘Apo palibe mkhalapakati wina pakati pa Mulungu ndi munthu koma Mwamuna uja Khristu Yesu.’ Ndipo inu muli nawo akazi akufa zikwi zisanu ndi chinthu chirichonse amene inu mukuwapanga

akhalapakati. Tsopano nchiani chinachitika?” Apo inu muli. Iwo alibe yankho la zimenezo. Ndiko kulondola.

<sup>142</sup> Ndipo tsopano zina za chiphunzitso chawo, chiphunzitso chawo chabodza, gulu la aneneri abodza Achiprotestanti labwera mozungulira ndi kumaphunzitsa zimenezo, ndipo inu anthu Achiprotestanti mwazimeza zimenezo. Ndiko kulondola chimodzimidzi. Zipembedzo ndi mawonekedwe a maubatizo, ndi madongosolo osiyana ndi zinthu zimene inu mukupyolamo, zimene ziri mwamtheradi osati Zamwamalemba. Ndi zotsutsana nazo mu Lemba, komabe inu mumagwetseredwa kumene pansu kwa izo. Ndicho choonadi.

<sup>143</sup> Tsopano mvetserani kwa izi zokhudza alaliki aakazi. Chabwino, chinthu choyamba chingakhale, ine ndikufuna—l Timoteo 2:11. Tsopano mvetserani chimene Iyo ikunena apa.

*Lolani akazi anu aphunzire mwa kachetechete ndi kumvera konse.*

*Koma ine sindiri kulola mkazi kuti aziphunzitsa, kapena kuti azichita ulamuliro pa mwamuna, koma kuti akhale mu kachetechete.*

<sup>144</sup> Ine ndiribe udindo woyika izo mmenemo. Ine ndiri ndi udindo wa kukuuzani inu kuti izo ziri mmenemo. Mwaona? Mwaona?

*Lolani akazi anu aphunzire mwa kachetechete ndi kukhala mwa kumvera konse. (Ngati inu munayamba mwapitako ku mpingo wa Orthodox ndi kukawawona iwo, onani. Mwaona?)*

*Koma ine sindiri kulola mkazi kuti aziphunzitsa, kapena kuti azichita ulamuliro (kaya kukhala m'busa, dikoni, kapena chirichonse monga izo) pa mwamuna, mwaona, kuchita ulamuliro pa amuna, koma kuti akhale mwa kachetechete.*

*Pakuti Adamu anayamba kupangidwa, ndipo kenako Eva.*

<sup>145</sup> Kodi inu mumadziwa... Tsopano mvetserani, akazi. Inu akazi abwino olungama Achikhristu muli chinthu chopambana chimene Mulungu akanakhoza kumupatsa mwamuna kapena Iye akanamupatsa iye chinachake chosiyana. Inde, bwana. Mwaona? Mkazi sanali nkomwe mu chirengedwe choyamba. Mkazi sali cholengedwa chopangidwa ndi Mulungu. Iye ali chopangidwa kuchokera kwa mwamuna. Mulungu anamupanga mwamuna zonse mwamuna ndi mkazi. Ndipo Iye anawalekanitsa iwo, ndipo mwamunayo atakhala kale pa dziko lapansi ndipo atatchula zinyama ndipo atakhala kuno nthawi yayitali, Iye anatenga nthiti kuchokera mu mbali ya Adamu ngati chopangidwa kuchokera pa china kuti amupange mkazi

kwa iyo. “Adamu anapangidwa choyamba, ndipo kenako Eva.” Tsopano penyani.

*Ndipo Adamu siyemwe ananyengedwa, koma mkaziyo pokhala atanyengedwa anali mu kulakwa.*

146 Mulungu anatenga mwamuna; Mdierekezi anatenga mkazi. Yang’anani pa izo molunjika kumene mu nkhope. Nchiyani chikuchita izo lero? Yang’anani pa mpingo weniweni wa Mulungu, iwo uziti, “Yesu!” Wotsutsakhristu aziti, “Maria!” Penyani mizimu imeneyo, onani, apo iyo ili. “Tikuoneni, Maria, mayi wa Mulungu, wodala muli inu pakati pa akazi, ndipo mutipempherere ife ochimwa tsopano mu tsiku la imfa lathu. Ameni.” Maria amawapempherera? O, mai, ubwino! Mwaona, apo inu mukupita, “akazi,” womvera Mdierekezi. Khristu, chinthu chopembedzedwa, ndipo Mmodzi yekhayo! Apo inu muli, apo inu muli.

147 Adamu analengedwa poyamba, ndipo kenako Eva. Adamu sananyengedwe ayi. Ndipo inu mukanakhoza bwanji kukhala ndi m’busa wamkazi, dikoni? Adamu sananyengedwe ayi, koma mkaziyo ananyengedwa. Iye anali makamaka. . . Iye sanali kuganiza kuti iye anali kulakwitsa, koma iye anali. Mkazi pokhala atanyengedwa anali mu chilakwitso. Chifukwa iwo ali. . . Nthawi iliyonse imene—maliro akupita pansu mu msewu, mkazi anayambitsa iwo. Nthawi iliyonse imene mwana analira kwambiri, mkazi anayambitsa zimenezo. Nthawi iliyonse imene winawake anamwalira, mkazi anayambitsa zimenezo. Tsitsi lirilonse la imvi, mkazi anayambitsa zimenezo. Chirichonse, ndipo imfa, mkazi anayambitsa izo. Chirichonse chimene chiri cholakwika, mkazi anayambitsa icho. Ndiyeno nkumuyika iye mutu wa mpingo, m’busa, o, bishopu nthawizina. Manyazi pa iye.

148 Tsopano ndiroleni ine ndikutembenezireni inu mu imodzi ina yokha, mu miniti yokha, onani. Tsopano tiyeni titembenuze ku I Akorinto 14:32 kumeneko, ndipo tiwone zimene Paulo akunena cha apa, ndiyeno ife tipita kwa zina zochulukira mu miniti chabe. Ndiyeno ife sitikufuna kuti tikusungeni inu motalika kwambiri, kotero inu mudzakhale otopa kwambiri mmawa mwakuti inu simungakhoze kubwereranso. Chabwino, ine ndikufuna kuti ndiwerenge. Ndi angati amakhulupirira kuti Paulo anali mphunzitsi wodzozedwa? Tsopano, kumbukirani, Paulo analemba izi kwa Timoteo nayenso. Mwaona? Ndizo, tsopano, I Akorinto 14:32. Tsopano tiyeni tiyambire pomwe apa ndi kuyamba kuwerenga apa, 14:34, ine ndikukhulupirira.

*Lolani akazi anu akhale chete mu mipingo: . . .*

149 Kodi inu munamva zimene iye ananena?

*Lolani akazi anu akhale chete mu mipingo: pakuti sikuli kololedwa kwa iwo kuti ayankhule; koma iwo akulamulidwa kuti akhale pansu pa kumvera, . . .*

<sup>150</sup> Kodi inu muli nako kuwerenga kwa mmalire pa izo? Ngati inu muli, pitani nako mmbuyo ndi kuwona ngati iko sikakutenga Genesis 3:16. Pamene Mulungu anamuuza Eva, chifukwa chakuti iye anali atamvetsera kwa serpenti mmalo mwa mwamuna wake, kuti mwamuna akanati azilamulira pa iye masiku onse a moyo wake. Mkazi angakhoze bwanji kubwera ndi kulamulira pa mwamuna, kukhala m’busa kapena dikoni, pamene Baibulo linanena kuti “mloleni iye akhale womvera” monga momwe izo zinaliri mu pachiyambi pamene Mulungu. . . Mulungu sangakhoze kusintha. Inu simungakhoze kuwapanga Mawu kunena chinthu chimodzi *apa* ndi china cha *apa*. Iwo samachita zimenezo. Ndi chinthu chomwecho nthawi zonse. Kotero pachiyambi, ndiko kumene. . .

<sup>151</sup> Izi zisanafike pakutha, ngati ine nditapeze mwayi, ine ndikufuna kuti ndikuwongolereni vuto lija la chikwati ndi chilekano kwa inu. Ine sindinachitepo zimenezo mu mpingo uwu pano. Koma penyani pangano la pawiri ili. Limodzi likunena kuti mkaziyo akhoza kukwatiwa, ndipo lina linanena kuti mwamunayo sangakhoze kukwatira, ndipo limodzi ili likunena *izi, izo*, kapena *chimizake*. Ingodikirani miniti ndipo muwone chimene Baibulo likunena pamene ife titi tifike ku zimenezo. Mwaona? Chabwino. Tsopano penyani apa.

*Mulole akazi anu akhale chete mu mipingo: . . . sikuli kololedwa kwa iwo kuti ayankhule; koma iwo akulamulidwa kuti akhale pansi pa kumvera, monganso linena lamulo.*

<sup>152</sup> Ndiye, mu Chipangano Chakale iwo sanali kuloledwa kuyankhula, chifukwa Paulo ananena apa kuti iwo sanali. Ndi kulondola uko? “Mulole akazi anu akhale chete, ndiko kumvera.” Tsopano ngati inu mukufuna kutsata kuwerenga kwanu kwa mmalire pamenepo, tengerani iko mmbuyo ku Genesis 3:16. Mwaona? Chabwino. “Pansi, monga pansi pa lamulo.”

*Ndipo ngati iwo . . . kuphunzira chirichonse, mulole awo . . . akawafunse—akawafunse amuna awo kunyumba: pakuti ndi chamanyazi kuti mkazi ayankhule mu mpingo.*

*Chiyani? . . .*

<sup>153</sup> Tsopano yang’anani pa chisonyezo cha funso icho pa limodzi lililonse la Mabaibulo anu, pa “Chiyani” ameneyo? Nchiyani chimene chinamupangitsa Paulo kuti anene zimenezo ndi kuti achite izo monga choncho? Tsopano, ngati inu mutati mupeze konse makalata amene Akorinto analemba kwa Paulo. Tsopano, inu mukhoza kuwapeza iwo mu laibulale yabwino iliyonse. Mwaona, amene Akorinto analemba kwa Paulo, iwo analemba ndipo anamuuza iye. Zitachitika kuti akazi awa amene anali atatembenezidwa. . . Iwo anali ndi m—mulungu



wamkazi kumeneko yemwe anali kutchedwa “Diana,” ndipo iye anali ku Efeso, nayenso. Ndipo Akorinto ankapembedza yemweyo, chifukwa uko kunali kupembedza kwachikunja. Ndipo iwo anaupenza mwala kunja mmunda tsiku lina, iwo unkawoneka ngati mawonekedwe a mkazi. Iwo anati, “Mulungu ndi mkazi, ndipo iye anagwetsera pansi fano lake kwa ife.” Ndipo kachisi wawo anali patali kupitirira kachisi wa Solomoni, iwo anatero, azambiriyakale. O, iye anali yense nsangalabwi, wokometsedwa ndi golide; kumene, kachisi wa Solomoni anali wopangidwa ndi nkunguza ndi wokometsedwa ndi golide. Mwaona? Ndipo iye anali patali kupitirira ameneyo! Ndipo ameneyo, ndiye, ngati Mulungu anali m—mkazi, bwanji, zedi, iye akanakhoza kukhala nawo ansembe aakazi. Zedi, ngati Mulungu ali mkazi, ndiye mlaliki wamkazi akulondola. Koma Mulungu ndi Mwamuna, Baibulo linati Iye anali Mwamuna. Iye ndi Mwamuna. Mwaona? Ndipo ngati Mulungu anali Mwamuna, ndiye ayenera kukhala mwamuna.

Tsopano zindikirani apa, “Chiyani?”

<sup>154</sup> Tsopano, ena a ansembe aakazi awo, pamene iwo anatembenezidwa kuchokera ku chikunja kupita ku Chikhristu, iwo ankaganiza kuti iwo akanakhoza kusunga udindo wawo ngati mlaliki, kungobwera chomwecho mpaka kwinaku. Ngati iwo ank'alalikira kumeneko za Diana, iwo akanabwera mpaka kuno ndi kum'alalikira za Khristu.

<sup>155</sup> Iye anati, “Chiyani? Anabwera Mawu a Mulungu kwa . . .” Ingomvetserani kwa Izi. M'bale, atumiki angakhoze bwanji kuchita zimenezo? Ndime ya 36.

*Chiyani? kodi mawu a Mulungu anabwera kuchokera kwa inu? kapena kodi iwo anabwera kwa inu nokha?*

*Ngati munthu aliyense adziganizira yekha kuti ali mneneri kapena wauzimu (sasowa ngakhale kuti akhale mneneri; munthu woganiza mwauzimu basi), msiyeni iye azindikire kuti zinthu zimene ine ndikulemba kwa inu ziri malamulo a Ambuye. (Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?)*

*Koma ngati iye . . . ngati wina akhala wosadziwa, ingomusiyami iye akhale wosadziwa.*

<sup>156</sup> Tsopano, ndizo basi zomveka monga ine ndikanadziwira kuziyika izo. Mwaona? Iye anati, “Ngati munthu ali munthu wauzimu, kapena mneneri, iye adzazindikira kuti zimene ine ndikulemba pano ndi Malamulo a Ambuye.” Koma anati, “Ngati iye—ngati iye ati akhale mbuli, ingomusiyani iye akhale mbuli.” Mukuona, chinthu chokhacho chimene inu mungakhoze kuchichita. Ngati iwo akufuna kumapitirizabe mu izo, inu mukungoyenera kuwalola iwo kuti azipita, chifukwa iye anaziwona izo zikuyamba kumeneko.

157 Ndipo mkazi wina anandiuza ine, iye anati, “O, Paulo anangokhala wachikulire wodana ndi akazi.”

158 Iye sanali wodana ndi akazi ayi. Inu mukudziwa, Paulo anali mtumwi, ndipo kwa mpingo wa Amitundu. Penyani apa. Kodi inu mumadziwa kuti Paulo. . . Ndi angati amene akukhulupirira kuti ndizo zimene Paulo ankalalikira? Kodi ndi zimene iye—iye ananena apa? Ndipo Paulo anati. . .

159 Inu mukuti, “Chabwino, dikirani miniti tsopano, M’bale Branham. Miniti chabe! Tsopano, abishopu athu amanena kuti ndi zabwinobwino. Oyang’anira aakulu, a assembly amanena kuti ndi zabwinobwino. Abishopu aumodzi amanena kuti ndi zabwinobwino.”

160 Ine sindikusamala zimene iwo amanena, ndi zabodza! Ndipo ine ndinakuwuzani inu kuti ife tikhomerera izi molimba. Ndi aneneri abodza akunena chomwecho. Pakuti Baibulo linati, “Ngati munthu aliyense akudziganizira yekha kuti ali wauzimu, kapena mneneri, muloleni iye avomereze kuti zimene ine ndikunena ziri Malamulo a Ambuye.” Ndipo ngati mzimu wake suli kugwirizana ndi Mawu amenewo, iye ali mneneri wabodza kuyamba ndi kuyamba. Ine kulibwino ndikhale wodana ndi akazi kuposa wokonda akazi, kumapita ndi chinthu chotero monga icho, kuti ndizilekerera zinthu zotero monga zimenezo, mpingo wa Mulungu wosiyana kwa malangizo a Mulungu. Ndipo Paulo anati, tengani Agalatiya 1:8, Paulo anati, “Ngati mngelo wochokera Kumwamba akanati alalikire Uthenga wina uliwonse kuposa uwo umene ine ndalalikira kwa inu, msiyeni iye akhale wotembereredwa.” Tsopano kodi inu muchita chiyani ndi Izo.

161 Tsopano inu mukuti, “Nanga bwanji za pamene Ilo linati, ‘Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera,’ mu Yoweli, ndi—ndi pamene Petro anazifotokoza pa Tsiku la Pentekoste?” Ndi kulondola chimodzimidzi.

162 Kodi inu mumadziwa, mu Chipangano Chakale, kuti njira yokhayo, ndipo njira yokhayo tsopano, imene aliyense akanakhoza kubwera mu pangano kupyolera, mwa. . . Abrahamu anali mmodzi yemwe anapatsidwa lonjezo, ndipo—chisindikizo cha lonjezo chinali mwa mdulidwe. Ndi angati akudziwa zimenezo? Uyo anali Mulungu kutsimikizira.

163 Monga m’bale wa Chibaptisti, iye anati, “M’bale Branham, bwanji, ife Achibaptisti tinalandira Mzimu Woyera.”

Ine ndinati, “Inu munaulandira liti Iwo?”

Anati, “Ora limene ife timakhulupirira.”

164 Ine ndinati, “Paulo anati, ‘Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?’” Mwaona? Ine ndinati, “Tsopano, inu Achibaptisti bwerani mudzatenge zina za Izo,

ndipo tidzakambirana zina za chitetezero Chamuyaya ndi inu,” ine ndinatero.

“Koma, chabwino, mumazipeza pati inu izo monga choncho?” Mwaona?

<sup>165</sup> Iye anati, “Kodi inu munalandira Iwo chikhulupirireni chanu?” Iwo anali okhulupirira, ndipo ali nako kufuula ndi chisangalalo ndi chinthu chirichonse. Iwo anali asanalandire Mzimu Woyera apobe, Paulo anati iwo anali asanalandire. Mwaona? “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?”

Iwo anati, “Ife sitikudziwa ngati ulipo Mzimu Woyera uliwonse.”

Anati, “Ndiye inu munabatizidwa motani?”

<sup>166</sup> Iwo anati, “Ife tinabatizidwa.” Koma mwabodza, onani, kotero iye anali oti abatizidwense kachiwiri. Chabwino.

<sup>167</sup> Tsopano zindikirani izi tsopano, kuti alaliki aakazi awa, pamene iwo anabwera umo, iwo ankaganiza kuti iwo akanatenga ulamuliro wawo. Koma ndizo mwamtheradi zosaloledwa ndi Mulungu kuti achite chomwecho. Ndi kulola . . . basi pamene ife tiri kumene pa phunziro ili apa, akazi awa, onani, mwa izo. Tsopano, Ilo linati, “Ngati pakhala munthu aliyense pakati panu, yemwe ali wauzimu, kapena mneneri, msiyeni iye avomereze kuti zimene ine ndikulemba ziri Malamulo a Ambuye. Koma ngati iye ali mbuli, ingomusiyani iye akhale mbuli.” Ndipo ndicho chifukwa . . . Kachisi yu samayima ndi kumadzoza alaliki aakazi, madikoni aakazi, kapena chirichonse choti mkazi azichita ngati udindo wa mpingo uno, ndi chifukwa Lemba ili liri apa ndi ndizosabisika.

<sup>168</sup> Tsopano, Baibulo linanena kuti, “Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera.” Tsopano, kodi mawu oti “kunenera” amatanthauza chiyani? Yang’anani pa ilo. Ndiko “kunena chinachake, pansu pa kudzoza,” kapena “kulosera chinachake,” ndi mawu apawiri.

<sup>169</sup> Monga ngati kuyeretsa kumatanthauza kukhala “wotsukidwa, ndi kuyikidwa pambali kwa utumiki,” Mwaona? Kapena, ndiwo mawu apawiri otanthauza mochulukuka kuposa chinthu chimodzi, monga ife tiri nazo zochulukuka za izo mu Chingerezi apa.

<sup>170</sup> Monga, ife timanena mawu a “board.” Chabwino, kodi *board* angatanthauze chiyani? Inu mukuti, “Chabwino, iye akutanthauza kuti iye analipira *gulu lake*.” “Ayi, iye sanatero, iye amatanthauza kuti iye *anabowola bowo*.” “Ayi, iye sanatero, iye amatanthauza kuti iye *anamukola iye*.” Kapena, inu mukuona, mawu chabe, ndipo iwe umayenera kudziwa chimene iwe ukuchiyankhula. Mwaona?

<sup>171</sup> Ndipo ndimo momwe izo ziliri, mawu apawiri awa, pamene, “Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera.” Tsopano, njira yokha imene Mulungu. . .

<sup>172</sup> Wa Chibaptisti uyu anati, “Chabwino, ife talandira Mzimu Woyera.” Ine ndinati. . . “Ndiye pamene ife tinaukhulupirira iwo.” Ine ndinati. . . Tsopano, onani, iye anati, “Mulungu anamupatsa Abrahamu. . .” Iye anati, “Abrahamu anakhulupirira Mulungu.” Ndimo momwe iye anayikira izo. Iye anati, “Abrahamu anakhulupirira Mulungu ndipo iko kunawerengedwa kwa iye kukhala chilungamo.” Ndi angati akudziwa kuti ndizo zoono? Tsopano penyani momwe—kuphweka kwake momwe Satana angakhoze kuzembetsera izo pa m’bale. Onani, mophweka basi. Tsopano, ilo ndi Lemba.

<sup>173</sup> M’bale, ine ndikukuuzani inu, mu izi mkati, umu apa, inu muyenera kukhala muli odzozedwa inu musanalowe mu izi. Iwe uyenera kuti uzilowa mu malo achinsinsi ndi kupemphera. Anthu amati, “Bwanji iwe sumapita kunja ndi kumakawawona anthu?” M’bale, ngati iwe ukupita kuti ukayankhule kwa anthu, kapena kuwaphunzitsa iwo, iwe kulibwino uzikhala kwa wekha ndi Mulungu kwa kanthawi iwe usanati ukalowe pa guwa limenelo. Ndithudi, mwaona, chifukwa Satana ndi wothyathyalika, wothyathyalika kwambiri.

<sup>174</sup> Iye anati tsopano, zindikirani, iye anati, “Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo iko kunawerengedwa kwa iye kukhala chilungamo.” Ndiko kulondola. Iye anati, “Tsopano, ndi chiyandinso chimene Abrahamu angakhoze kuchita kupatula kukhulupirira?”

Ine ndinati, “Ndizo zonse zimene iye akanakhoza kuchita.”

<sup>175</sup> Iye anati, “Ndi zochuluka zina zomwe inu mungakhoze kuchitira kapena wina aliyense kupatula kukhulupirira?”

<sup>176</sup> Ine ndinati, “Ndizo zonse zimene ife tingakhoze kuchita. Koma penyani, m’bale, ndiye Mulungu anayanjanitsa, kapena anazindikira chikhulupiriro cha Abrahamu. Iye anamupatsa iye chisindikizo, chizindikiro cha mdulidwe ngati chisindikizo cha pangano. Mwaona, Iye anamupatsa iye. Iye anati, ‘Tsopano, Abrahamu, Ine ndazindikira chikhulupiriro chako, kotero Ine ndati ndikupatse iwe chizindikiro tsopano kuti Ine ndakulandira iwe.’”

<sup>177</sup> Kotero iye anamudula Abrahamu, ndipo chimenecho chinali chisindikizo cha pangano. Ndipo tsopano mu tsiku ili. . . Tsopano, mkazi sakanakhoza kukhala nawo mu pang’ano limenelo; mkazi wokwatiwa yekha. Fufuzani izo, sakanakhoza kumudula wamkazi; kotero iye amayenera kubwera mkati, kwakuti iye ndi mwamuna wake ali mmodzi. Iwo salinso awiri; iwo ali mmodzi. Ndi angati akudziwa zimenezo? Lemba limanena choncho. Kotero iye pokhala wokwatiwa, ndiye iye—iye amakhala mmodzi. Ndi kumapita mpaka pansa apa ndipo

penyani apa mu Timoteo, ananena chinthu chomwecho, anati, “Tsopano komabe iye adzapulumutsidwa mu kubala ana, ngati iye apitirira mu chikhulupiriro ndi chiyero ndi khalidwe loyenera lonse.”

178 Tsopano, komano, mdulidwe wa Chipangano Chakale unali mu thupi, koma mu Chipangano Chatsopano ichi, Yoweli anati, “Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa thupi lonse, ndipo ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera.” Tsopano, mawu okuti *kunenera* sikuti amatanthauza kuphunzitsa. *Kunenera* kumatanthauza kuti mwina “kunena chokuchitikira, pansi pa kudzoza,” kapena “kulosera chinachake chimene chikukonzekera kuti chichitike.” Ndipo ife tikudziwa kuti kunali aneneri aakazi mu Chipangano Chakale. Iwo sakanakhoza konse kuyankhula mu nyumba, kuyankhula mu mpingo, mwa osonkhana, ngati mphunzitsi. Koma, onani, Anna ndi ambiri a iwo mu kachisi, iwo anali aneneri aakazi, ndipo Miriamu anali mneneri wamkazi kapena chinachake monga choncho. Iye anali nawo Mzimu pa iye, ndizo zoono, koma iye anali nawo malire ake a malo. Akazi akhoza kukhala aneneri aakazi lero, mwamtheradi; koma osati aphunzitsi, ndi zina zotero, kuseri kwa nsanja kuno. Ngati inu mutero, inu mukulipanga—inukulipanga Baibulo kudzitsutsa Lokha. Baibulo silingakhoze kunena chinthu chimodzi *pano*, ndi chinthu china cha *apa*. Ilo liyenera kuti lizinena chinthu chomwecho nthawi zonse kapena Ilo siliri Mawu a Mulungu. Mwaona? Koteri, “Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera,” zikutanthauza kuti iwo mwina “adzakhala akumanenera” kapena “kuchitira umboni.” Tsopano, inu mukayang’ane zimenezo, ndipo inu mukatenge dikishonare ya Baibulo ndi kuwona ngati iko sikuli kulondola. “Ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera.”

179 Tsopano, Baibulo ndiponso limayankhula za mkazi yemwe ankanyengezera iyeyo, kapena kudzitcha kuti iye... Izi zingagwire ntchito kwa onse mpingo wa Katolika, ndipo zikhoza kugwira ntchito naponso ndi—ndi phunziro laling’ono ili limene ife tikuti tiyankhulepo tsopano. Tiyeni titembenuzire cha ku Bukhu la—la Chivumbulutso, ndipo tiyeni titenge pafupi mu—mutu wa 2 ndi ndime ya 20, basi pamene ife tikanali pomwepa pafupi ndi pamenepo, kuti inu mukhoze kuzindikira apa ndi kungowona momwe mwaudierekezi chinthu icho chingakhoze kukhalira, pa kuyankhula mu masiku otsiriza ano zimene zikanati zidzachitike, momwe kuti awa, chimene akazi awa akanati adzakhale. Kumbukirani, mpingo wa Katolika ndi mkazi. Ife tangowerenga kumene zimenezo, sichoncho ife? Mvetserani kwa izi tsopano, momwe Ilo likunenera, Chivumbulutso 2:20, “Tsopano komabe...” Iye akuyankhula kwa mpingo wa Tiyatira uwu, onani, “tsopano komabe,” umene uli m’badwo wa mpingo wapakati kumeneko, unadutsa kupyola mu Mibadwo ya Mdimba.

Tsopano komabe *Ine ndiri nazo zinthu pang'ono zokutsutsa iwe, chifukwa iwe ukulola mkazi uja Yezebeli, yemwe amadzitcha yekha mneneri wamkazi, kuti aziphunzitsa ndi . . . kuwalefula antchito anga ndi kuchita ziwerewere, ndi kudya zinthu zoperekedwa nsembe kwa mafano. Mwaona?*

<sup>180</sup> Tsopano, ngati inu munayamba mwazindikirapo, penyani mibadwo ya mpingo iyi, ndiye ife titseka. Ndiyeno mmawa ife tidzatenga zinthu zina izi. Penyani. Mu. . . Pansi pa—zoyikaponyali za golide za kachisi wa Chiyuda, mkati, mwa mkate ndi zina zotero, umo munali zoyikaponyali zisanu ndi ziwiri zagolide. Nonse a inu mukudziwa zimenezo, onani. Ndipo pali mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Izo zikukamba mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo mofanana. Tsopano ngati inu muzindikira mu Chivumbulutso 1, ife tikumupeza Yesu akuyima mu mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo, zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide, pamene iye anapotoloka ndipo anawona Mmodzi wonga Mwana wa Munthu atayima wovekedwa ndi. . . Momwe izo zinaliri, iye anali Mkwatibwi akuyima mu zoyikaponyali zitajambulidwa pamenepo.

<sup>181</sup> Tsopano, mu Chipangano Chakale, iwo ankatenga zimenezi, muni umodzi uwu ndi kuwuyatsa iwo, kutenga muni winawo ndi kuyatsira umodzi winawo, kuyatsira umodzi winawo, umodzi kuyatsira umzake monga choncho, mpaka iwo atayatsa zoyikapomiyuni isanu ndi iwiri yonseyo.

<sup>182</sup> Ngati inu mutazindikira pa chiyambi, pamene Mulungu anayamba kuchita ndi Ayuda, ndipo iwo ankapita kupyola mu m'badwo wagolide. Ndiyeno m'badwo wa mdima kwambiri wa zochitika za Chiyuda, Mulungu anali naye Myuda, anali mu ulumuliro wa Ahabu. Ndipo ngati inu mutazindikira, kuwerenga mibadwo ya mpingo imeneyo pamenepo, Iye akubwerera mmbuyo kwa iyo kachiwiri. Iye anati, tsopano, zinthu pang'ono zapitazo, ndipo anati. Tsopano, kumene mu M'badwo wa Mdima uja, zaka mazana khumi ndi asanu kumeneko, kapena nthawi ya Ahabu, choyamba, ndi Ayuda. M'badwo wa mdima kwambiri umene iwo anali nawo, pamene Ahabu anakwatira Yezebeli ndipo anabweretsa kupembedza mafano kulowa mu Israeli, ndipo anawapangitsa anthu onse kupembedza motsatira Ahabu, motsatira mulungu wa Yezebeli. Inu mukukumbukira, iwo anatenga, nayimika misitu, ndipo anagwetsera pansi maguwa a Mulungu. Ndipo Elisha analira kumeneko, iye anali “mmodzi yekhayo,” ndipo Mulungu anali nawo mazana asanu ndi awiri amene anali asanagwadire nkomwe bondo lawo kwa Balaamu apabe. Inu mukukumbukira zimenezo? Ndiwo mtundu uja wa Mpingo wosankhidwa umenewo ukutulukira. Onani pamenepo, mwaona momwe izo ziliri?

<sup>183</sup> Tsopano, mu mpingo uwu, ngati inu mutazindikire mpingo woyamba, mpingo woyamba, mpingo wa Efeso, unali mpingo

wawukulu. Iye anati, “Inu muli nawo moyo, panobe.” Ndipo ngati inu mutazindikira mpingo uliwonse, iwo unayamba kumathima, kumathima, kumathima, mpaka iwo unafika ku Tiyatira. Ndiye zaka mazana khumi ndi asanu. Ndiye iwo unatulukira ku mbali yinayo, “Ndipo inu muli nako kuwala pang’ono chabe. Limbikitsani izo zimene inu muli nazo, kuwopa kuti choyikapomiyuni chanu chingati chichotsedwe.” Ndipo izo zinafika mpaka pansi ndiye mpaka ku m’badwo wa mpingo wa Filadefiya, ndiyeno mpaka mu m’badwo wa mpingo wa Laodikaya.

<sup>184</sup> Tsopano, pano pali kukongola. O, mai, ine ndimangokonda izi, M’bale Smith. Onani, penyani pa izi. Tsopano, mu m’badwo wa mpingo uwu, monga ife tinadutsiramo. . . Tsopano penyani izi. M’badwo woyamba wa mpingo unali wa Efeso, m’badwo wa mpingo wa Efeso. Tsopano, uliwonse wa mibadwo ya mpingo iyo, mpaka iyo inafika ku zaka mazana khumi ndi zisanu izi, ngati inu mutazindikira. . . Kawerengeni izo tsopano pamene inu mupita ku nyumba usikuuno, ngati inu muli nayo nthawi, kapena mmawa molawirira, inu musanabwere ku tchalitchi, pa mutu wa 1, wa 2, ndi wa 3 wa Chivumbulutso. Inu mupezamo, umodzi uliwonse wa mibadwo ya mpingo imeneyo, Iye anati, “Inu muli nazo mphamvu pang’ono, ndipo inu simunakane Dzina Langa,” mpaka Iye atafika ku zaka mazana khumi ndi asanu izi za Tiyatira, M’badwo wa Mdima. Ndiye Iye unatulukira ku mbali inayo, ndipo anati:

. . . inu muli nalo *dzina kuti* inu muli amoyo, koma inu ndinu *akufa*.

<sup>185</sup> Ndipo iyi, palibe yina ya mibadwo ya mpingo iyi, uwo kapena m’badwo wa mpingo wa Filadefiya, siyinatenge konse Dzina limenelo kachiwiri. Siyinhale nalo konse Dzina limenelo, chifukwa iyo ilo linatukamo pa nthawi imeneyi. Tsopano, o, momwe ife tingakhoze kuyikira izo kwa ophunzitsa mwa bodza awo tsopano, pomwe apo, kukuwonetsani inu kuti ndi mayi, mpingo wa Katolika manthu wa izo zonse, momwe iwo uliri “Mayi, Chinsinsi, Babeloni.” Ndipo ndicho icho, penyani, m’badwo wa mpingo uwu pano pamene iwo unatuluka, iwo unali nako kuwala pang’ono, ndiye iwo unayamba kumathimira, thimira, ndiyeno iwo unabwera kudzalowa mu bungwe kumbuyo kuno, zaka mazana khumi ndi asanu izi. Ndipo iwo unabwera kunja tsopano, osati monga mpingo wa Ambuye Yesu Khristu, koma ngati mpingo wa Katolika. Kodi Lutera unatuluka chiyani? Monga mpingo wa Chilutera? Abaptisti unatuluka chiyani? Monga mpingo wa Baptisti. Osati Dzina Lake, osati Dzina Lake; dzina lina, “inu muli nalo dzina.” “Pakuti palibe dzina lina linapatsidwa pansi pa Kumwamba limene inu muyenera kupulumutsidwa nalo, kupatula Dzina la Yesu Khristu.” “Inu muli nalo dzina kuti inu muli amoyo, koma ndinu akufa,” ndizo ndi chipembedzo chimenecho.

<sup>186</sup> “O, ine ndine wa Presbateria,” ndipo ndinu wakufa! “O, ine ndine wa Baptisti,” ndi wakufa! Ndinu wamoyo kokha pamene inu mukhala wamoyo mwa Khristu Yesu. Ndiko kulondola. Ndipo maubatizo Anu abodza mu madzi, ubatizo wabodza, kukonkha, kutsanulira, mmalo mwa kumiza, kugwiritsa ntchito “Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera” mmalo mwa Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Zinthu zonse zabodza zimenezo zikubwera mpaka pansi, Baibulo likuyankhula, monga mwakutsanulira izo mmenemo basi molimba monga izo zingakhozere. Ndipo pano ife timalekererana kumene motsatira ndi iwo, “Chabwino, mpingo wanga umakhulupirira Izo njira-*iyi*.” Koma Baibulo limanena *Izi*. Mwaona? Palibe zinthu zoterozo, palibe zinthu zoterozo.

<sup>187</sup> Ndipo mulibe malo mu Baibulo pamene iwo anayamba asololerapo kunjira lirime lawo ndi kulandira ukalisitiya woyera, ndipo wansembe nkumwa vinyo ndi kumawutcha iwo Mzimu Woyera. Palibe konse mu Baibulo pamene iwo anayamba agwiranapo chanza ndi kupereka dzanja lamanja la chiyanjano ndi kumazitcha izo Mzimu Woyera. Palibe pamene aliyense anayamba wawukapo ndi kuti, “tsopano ndine wokhulupirira,” ndipo ndalandira Mzimu Woyera. Ngati izo zinatero, pano pali njira imene Machitidwe 2 akanamawerengedwera, “Ndipo pamene tsiku la Pentekoste linafika mwathunthu, akuyenda pa msewu anabwera wansembe wa Chiroma, ndipo iye anali atatembenuza kolala lake mozungulira. Iye akuyenda chokwera, ndipo anati, ‘Nonse inu tulutsani lirime lanu tsopano ndi kulandira ukarisitiya woyera, mgonero woyamba.’” Kodi iyo siyikanakhala njira yina yowerengera Machitidwe 2?

<sup>188</sup> Chabwino, inu Achiprotetanti ndinu oyipa mofanana. Kubwerera tsiku limenelo, “Tsopano pamene ife tikubwera kwa inu Achimethodisti, kuwayika iwo ku dzanja lamanja, kuwapatsa iwo dzanja lamanja la chiyanjano, ndi miyezi isanu ndi umodzi pa kuyesedwa.” Kodi inu mumawerenga pati zimenezo mu Machitidwe 2? Mwaona? Inu mukuzitenga kuti zimenezo? Mwaona?

<sup>189</sup> Ilo linati, “Pamene iwo anali onse mu malo amodzi ndipo mwa cholinga chimodzi!” Sikuti kunabwera konse bishopu ayi nachita *izi*, ndipo sikuti kunabwera konse wansembe nachita *izi*. “Koma uko kunadza mkokomo kuchokera Kumwamba monga Mphepo yamkuntho waliwiro lamphamvu, ndipo Iyo inadzaza nyumba yonseyo momwe iwo anali atakhalamo.” Iyo ndiyo njira imene iwo anawulandirira Iwo, inde, bwana, ngati mphepo ya mkokomo waliwiro lamphamvu likubwera kuchokera ku Ulemerero. Osati ku msewu kapena kuchokera ku chipembedzo china.

. . . inu muli nalo *dzina lakuti* inu ndinu amoyo, koma ndinu *akufa*.



<sup>190</sup> Mwaona, zikhulupiriro zanu ndi zipembedzo zatchingira Mulungu kutali monga choncho, mpaka, “Ife timakhulupirira izi, ndipo ife timakhulupirira kuti masiku a zozizwitsa anapita.” Ndi mneneri wabodza amene amanena zimenezo. Ndi mneneri wabodza yemwe amakuuzani inu kuti “inu mukhoza kugwirana chanza ndi kulandira Mzimu Woyera.” Ndi mneneri wabodza yemwe amakuuzani inu kuti “inu mumalandira Mzimu Woyera pamene inu mukhulupirira.” Ndi mneneri wabodza yemwe amakuuzani inu “kuti inu muyenera kutsanuliridwa ndi kukonkhedwa mmalo mwa kubatizidwa.” Ndi mneneri wabodza yemwe amakuuzani inu “kuti mubatizidwe mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” pamene palibe Lemba la izo mu Baibulo. Ndiko kulondola. Palibe Lemba mu Baibulo limene limakuuzani inu kuti muzibatizidwa, pamene aliyense anayamba wabatizidwapo, kokha mu Dzina la Yesu Khristu; ophunzira a Yohane okha, ndipo iwo anachita kubwera ndi kudzabatizidwanso mu Dzina la Yesu Khristu kuti alandire Mzimu Woyera. Ndiko kulondola. Tsopano, sindicho chiphunzitso cha a Yesu Yekha; ine ndikuchidziwa chiphunzitso cha a Yesu Yekha, sindicho chimenecho ayi. Ndicho Chiphunzitso cha Baibulo ili. Ndiko kulondola.

<sup>191</sup> Koma apo inu muli. Kodi inu mukuchita nacho chiyani icho? Uyo ndiye mayi wanu. Uyo ndiye mayi wa zikhulupiriro zimenezo.

<sup>192</sup> Tsopano, ngati inu mutayang’ana kumene mmbuyo mu Baibulo ndi kundiuza ine pamene winawake anayamba wakonkhedwapo. Amethodisti, Apresbateria, Akatolika, ndiwuzeni ine pamene munthu mmodzi anayamba wakonkhedwapo, mu Baibulo. Mundiuze ine pamene mmodzi anayamba watsanuliridwapo, mu Baibulo, kwa kukhululukira kwa tchimo. Tchulani izo. Kodi inu mungakhoze kuzipeza izo? Ngati inu mutero, bwerani kwa ine, ndipo ine ndidzayenda pansu mu msewu uwu ndi cholembedwa pa nsana wanga, ndi kumati “mneneri wabodza, ine ndakhala ndikulakwitsa.” Kapena inu mupeze malo amodzi mu Baibulo lonse pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, momwe magawo makumi asanu ndi atatu pa zana a inu mwabatizidwira. Ndipezereni ine Lemba limodzi pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mwa njira imeneyo, ndipo ine ndidzayika cholembedwa pa nsana wanga, “mneneri wabodza,” ndi kuyenda pansu mu msewu ndi icho monga *chonchi*. Ndipo ndiwonetseni ine pamene aliyense anayamba wabatizidwapo, mu mpingo watsopano, amene sanasowe kubwera ndi kudzabatizidwanso mu... osati mu Dzina la a Yesu Yekha, koma mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu. Ndiko kulondola. Onani ngati izo siziri zolondola.

<sup>193</sup> Ndipo, pano, nchiyani icho? Iye anali mayi wa timahule. Nchiyani chimene chinamupanga iye kahule? Nchiyani

chinamupanga iye hule? Chiphunzitso chake! Nchiyani chinawapanga iwo kahule? Chiphunzitso chake!

<sup>194</sup> Ndipo ndicho chifukwa ife sitimanyengerera ndi zipembedzo zawo ndi mbalume zawo. Ife timakhala oyera ndi Baibulo ili. Ine sindikudziwa ndi mwabwino bwanji momwe inu muti mukhalire nalo, koma inu mwaphunzitsidwa Izo, mulimonse. Kulondola. Izo ziri kwa inu. Ine sindingakhoze kukupangani inu kukhala mwa ilo. Ine ndingakhoze kokha kukuuzani inu chimene chiri Choonadi. Ndicho chifukwa ife sitiri chipembedzo. Ine sindikana—sindikanafuna kuti tidziditse tokha kuti tilowe mu zinthu monga zimenezo, kuchita kugwera pansa ku mtundu wina wa mbalume. Ine kulibwino nditenge njira ndi onyozeka apang'ono a Ambuye. Ine kulibwino ndikhale woyera ndi wangwiro pamaso pa Mawu ndi Mulungu, ndi kuyima pamenepo, ndi kunena kuti palibe magazi a munthu pa chovala changa. Ndicho chifukwa ife timakhala ku Branham Tabernacle. Ndicho chifukwa ife sitiri a Assemblies. Ndicho chifukwa ife sitiri Aumodzi. Ndicho chifukwa ife sitiri a Yesu Yekha. Ndicho chifukwa ife sitiri Amethodisti. Ndicho chifukwa ife sitiri Abaptisti. Ndi ka kachisi chabe—kakang'ono pano. Ife tiribe chipembedzo ayi konse. Ndife afulu, mwa Khristu. Ndicho chifukwa ife timakhala momwe ife timachitira. Ndipo Mulungu watidalitsa ife ndipo Mulungu akutithandiza ife.

<sup>195</sup> Tsopano, ife tikhoza kukuuzani inu chifukwa chimene ife timatenga mgonero, kukuuzani inu chifukwa chimene ife timatenga kutsuka-mapazi, chifukwa chimene ife sitimalola mamembala kudya iwo ngati ife tidziwa kuti iwo ali mu tchimo. Ndipo ndicho chifukwa masabata awiri kapena atatu awa ine ndakhala ndikupita kuchokera kwa membala mmodzi kwa mmodzi wina, kumene inu mwakhala mukukhala nato timakangano tanu tating'ono pozungulira nanunso. Kupita mozungulira, mmodzi asakuyankhulana kwa winayo, kumadutsana wina ndi mzake pa msewu ndi kumatembenuza mitu yawo, manyazi pa inu, amene mwatengera chikho chodala cha Mulungu pamwamba apa, pa guwa pano. Ndipo chifukwa inu abale ndi alongo ndi iwo mumafika pa telefoni ndi kumageya zokhudza wina ndi mzake, inu simuli oyenera kuti muzitchedwa Mkristu pamene inu muli mu njira imeneyo. Kulondola. Inu mukhale kutali ndi matelefoni amenewo, ngati inu simungakhoze kuyankhula zabwino za winawake inu musati muziyankhula konse. Kumbukirani, Mulungu adzakufunsani inu mlandu. Malingana ngati mtundu wa mzimu umenewo uli mwa inu, inu mukudziwa kuti inu simuli mwabwino ndi Mulungu. Ndipo ngati inu simukumverera . . .

<sup>196</sup> Ngati munthu ali mu kulakwitsa, pitani kwa iye, kayanjinitidweni. Ngati inu simungakhoze kuyanjanitsidwa, tengani winawake ndi inu. Nzosadabwitsa kuti Mulungu sangakhoze kuwupatsa khalidwe mpingo Wake, chifukwa

inu simukuchita izo molondola. Mmalo mofika pa foni ndi kuyankhula za mmodzi *uyu*, *chimene* chakhala chikuchitika, ndipo timipatuko tating'ono ndi zina zotero, kuzungulira nato monga choncho. Mmalo mochita zimenezo, nchifukwa chiyani inu simuli kumachita chimene Baibulo limanena? Ngati m'bale wina wakhala atagonjetsedwa mu kulakwitsa, pitani kwa iye ndipo mukawone ngati inu simungakhoze kuyanjanitsidwa ndi iye. “Chabwino, tsopano iye anandichitira ine!” Ine sindikusamala zimene iye anachita, pitani kwa iye mulimonse! Ilo silinanene kuti iye azibwera kwa inu. Inu mupite kwa iye ngati iye akulakwitsa. Inu mukuti, “Chabwino, iye anali mu kulakwitsa, iye anayenera kuti abwere kwa ine.” Sindizo zimene Baibulo linanena. Baibulo linanena kuti inu muzipita kwa iye. Ngati iye ali wolakwitsa, inu mupite kwa iye.

<sup>197</sup> Ndiyeno ngati iye sati amvetsere kwa inu, ndiye tengani winawake ndi inu ngati mboni.

<sup>198</sup> Ndiyeno ngati iye safuna kumuwona mboni ameneyo, ndiye, nenani, tsopano ine ndiwatenga abusa anu. Ndiye inu mumuwuze iye, kuti, “Ine ndikazinena izo kwa mpingo, ndipo mu masiku makumi atatu kuchokera pano, ngati inu abale simukhala mutazikonza zimenezo. . . M'bale uyu apa akulolera kuti ayanjanitsidwe. Inu simukufuna kuchita izo. Ndipo ngati inu simukonza zimenezo mu masiku makumi atatu, ndiye nchiyani chimene chiti chichitike, inu simulinsu mmodzi wa ife.”

<sup>199</sup> Baibulo linati, “Ngati iye sawumvera mpingo, ndiye msiyeni iye akhale kwa inu monga wakunja ndi wamsonkho.” Inu mukuona, malingana ngati m'bale ali pansu pa chitetezero icho cha mpingo, Magazi a Khristu akumutetezera iye. Ndicho chifukwa ife sitimawufikitsa mpingo pomayenda mwa njira yomwe iwo umachitira. Tsopano, ine sindiri. . . Ichi ndi chiphunzitso cha Baptisti—cha mpingo wa Baptisti, kapena Branham Tabernacle pano, ngati inu muzichita izo. Mwaona, bwanji simukhoza. . .

<sup>200</sup> Inu mumafika pano ndipo titi, mwa chitsanzo, amuna awiri, titi Leo ndi ine. Chabwino, inu muyenera kuti munene. . . ndi ine kuti, “Chabwino, iye—iye anandilakwira ine.” Izo sizipangitsa kusiyana kulikonse, ndipo ine ndikuyenera kuti ndipite kwa iye. Chabwino, iye ndi membala wa mpingo uno. Iye—iye wakhala Mkristu. Iye amatenga mgonero pano pa chotchinga ndi ine. Ndipo ife takhala obatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu. Timayenda moyenera ngati abale pamaso pa wina ndi mzake, ndiye chinachake chinachitika.

<sup>201</sup> Izo si munthuyo, magawo makumi asanu ndi anai pa zana a nthawi ndi Mdierekezi yemwe wafika pakati pa anthuwo. Izo si anthuwo, ndi Mdierekezi. Ndipo malingana ngati inu mumulola Mdierekezi kuti azichita zimenezo, inu mukumupweteka m'bale wanu. Ndiko kulondola.

202 Chabwino, chinachake chalakwika naye Leo ndi ine, tiyeni tipite tikachikonze icho. Ndipo ngati inu mukuwona kuti pali chinachake, ndi ntchito yanu kuti mubwere kwa ife, ndi kuti, “Anyamata nonse inu bwerani kuno ndipo khalani limodzi, ife tati tichikonze chinthu chimenechi. Tsopano, ndiyeno ngati izo zifika mpaka pamenepo—pamenepo, kufika popeza ndiye, pano ife tiri, ine nditi chabwino, chinthu choyamba, ngati ife—ife sitingakhoze kugwirizana, ndiye inu mubwere ku mpingo monga choncho.

203 Ndiyeno ngati nthawi yonse imene inu simuchita kanthu za izo, o, Magazi a Yesu Khristu amatiteteza ife tonse. Mwaona? Koma ndiye khansara yakale iyo—iyo idzayambitsa khansara yina, ndi khansara imeneyo iyambitsa khansara yina, ndipo chinthu chonsecho, chidzakhala chodwala pa mpingo wonse. Ndiye inu mufika pa malo amene inu mukubwera mu tchalitchi, ndi basi wozizira, kuchita kufika poti mukhale ndi wosamalirapamalo kuti azibwera kudzaswa chisanu motsogola osonkhana asanafike kuti alowe mkati. Tsopano, inu mukudziwa kuti ndizo zolondola. Ndipo ozizira! Winawake kukhala pamenepo, inu mukudziwa, ndipo basi osati nkunena kanthu. “Ife poyamba tinali auzimu kwambiri.” Chabwino, chinachitika nchiyani? Inu munali kuthamangadi bwino, ndi chiyani chinali chovuta? Mwaona, machimo anu akulekanitsani inu. Mulungu adzakuyimbani inu mulandu chifukwa cha izo, abale. Tsopano chiwongoleni chinthu chimenechi.

204 Palibe kanthu kalakwika ndi ine, palibe kanthu kalakwika ndi Leo; ndi Mdierekezi yemwe wafika pakati pathu. Ndiko kulondola. Fikani pokonza chinthucho. Pitani kwa iye. Ndiye ngati iye samvera, kapena ine sindimvera, njira iliyonse imene izo ziri, ndiye kachineneni icho ku mpingo. Ngati iye sabwera kuti adzayanjanitsidwe kwa mpingo umenewo mu masiku makumi atatu, ndiye iye achotsedwa kuchokera pansu pa chitetezero cha Yesu. Ife timumasula iye. Ndiko kulondola chimodzimodzi. Ndiye penyani chimene chiri chikuchitika. Mumulole Mulungu achite kupereka khalidwe ndiye. Inu mwachotsapo manja anu. Inu mwachita chopambana chimene inu mukanakhoza. Ndiye mumulole Mulungu akhale naye iye kwa pang’ono pokha, Iye amutembenezira iye kwa Mdierekezi. Iye adzabwera ndiye. Ngati iye satero, moyo wake wangokhala wa danga lalifupi.

205 Ndipo inu mukukumbukira mu Baibulo pamene panali m’bale yemwe sanali kudzikonza ndi Mulungu? Ndi angati akukumbukira mulanduwo? Iye ankagona ndi amayi ake aang’ono, ndipo iwo samakhoza kumufikitsa iye poti nkuwongoledwa. Paulo anati, “Mutembenezireni iye kwa Mdierekezi, kwa kuwonongeka. Inu mumazipeza kuti, mu II Akorinto, iye anawongoledwa.

<sup>206</sup> Ine ndiri naye m'bale, mzanga wabwino, ine ndikanakonda pano kutchula dzina lake. Iye ndi m'bale wolalikira, ndipo m'bale wolalikira uyu, dzina lake ndi M'bale Rasmussen. Ambiri a atumiki inu mwakhala pano usikuuno, dzina lake liri pa mapepala anu. Ndi ochokera muzipembedzo aja a ku Chicago. Ndipo penyani. Iye anali ndi mnyamata, mtumiki, ndipo iye anapita ndi kukakwatira msungwana wa Chikatolika, anayamba kutayika monga choncho, ndipo iye amamka akuchita *izi*, izo ndi *zimzake*. Ndipo—ndi zina zonse, anafika mu vuto lina. Ndipo adadi ake anapita kwa iye, anati, “Tsopano tapenya, mwana, kodi iwe uyanjanitsidwa kwa adadi?” Iye anawutcha mpingo wawo gulu la oyera odzigudubuza, abambo ake. Iye anati, “Tsopano tapenya, kodi iwe upita ukakonze chinthu chimenecho ndi mpingo uwu?”

<sup>207</sup> Iye anati, “Tsopano, abambo, ndinu abambo anga, ndipo ine sindikufuna kulowa mu vuto lirilonse ndi inu.”

<sup>208</sup> Chabwino, anapita ndipo anakatenga mmodzi wa madikoni ndipo anapita ku nyumba yake uko. Anati—anati, “Wesile, ine ndikufuna kuyankhula kwa iwe.” Anati, “Kodi iwe ukonza chinthu ichi kwa mpingo?” Ndipo iye anawapatsa iwo mayankho-awiri aafupi monga choncho. Anati, “Kumbukira, Wesile, ndine m'busa wa mpingo umene uja. Ndine abambo wako, koma ine ndikupita ndikachite chimene Mulungu anena kuti ndichite. Ine ndikukupatsa iwe masiku makumi atatu kuti ukakonze izo ndi mpingo umenewo, kapena ife tikuchotsa iwe kuchokera pa Kukhalapo kwa Mulungu. Ndiwe mwana wanga yemwe; Uyo ndi Mpulumutsi wanga.” Anati, “Ine ndimakukonda iwe. Ndipo iwe ukudziwa kuti ine ndimakukonda iwe, Wesile, ine ndikanakhoza kufa pakali pano chifukwa cha iwe, koma iwe uyenera kubwera molunjika ndi Mawu a Mulungu, waona.” Anati, “Ndine m'busa, ndine wolishya wa nkhosa zimenezo, ndipo ngati ndiwe mwana wanga kapena yense yemwe iwe uli, iwe uyenera kufola ndi Mawu a Mulungu. Ngati iwe suchita zimenezo, ndiye ine sindiri woyenera kuti ndikhale m'busa Wake.”

<sup>209</sup> Mnyamata, uyo ndiye m'busa. Ndiye mwamuna. Kodi inu simukuganiza choncho? Ndiye mwamuna. Iye anamuza mnyamata wake zimenezo, ndi kumupweteka iye, iye anati. Koma ananena chiyani? “Kodi iwe umupweteka ndani, munthuyo kapena kupweteka Mpulumutsi wako?” Koteri iye anati, “Ndiye ife tinapitirira nazo.”

<sup>210</sup> Ndipo anati, “Iye sanafune kuti achite zimenezo. Ndipo ife...ine ndinawuuzza mpingo, ndipo anati, ‘Mwana wanga yemwe, Wesile, iye akukana kuti andimvere ine mu vuto ili. Iye akukana kuti awamvere madikoni. Ndinu mboni wa izi, M'bale *Wakuti-ndi-wakuti*?’ ‘Inde, ine ndiri.’ ‘Chabwino, pa eyiti koloko Lamlungu lotsatira, masabata anai kuchokera pano, ngati iye sakhala atakonzza izo bwino ndi mpingo uno, ife timupereka

Wesile, mwana wanga wamwamuna, kwa Mdierekezi, kwa chiwonongeko cha thupi, magazi awa, Magazi a—a Yesu Khristu ndipo mpingo uwu sizimutetezanso iye motalikiranso.”

<sup>211</sup> Ndipo usiku umenewo unabwera, anayima pa guwa, anati, “Iye ali nawo maminiti awiri enanso.” Nthawi inafika, iye anati, “Tsopano, monga mwana wanga wamwamuna, Wesile Rasmussen, ndipo ndinanena kwa osonkhana awa ndi kwa Inu, Mulungu Wamphamvuzonse, ife tachita zonse zimene ife tikanakhoza kuchita, molingana ndi Mawu anu ndi malangizo a Wanu—a Mwana Wanu, Mpulumutsi wathu, anatisiyira ife, ife tsopano. . . Ine ndikumpereka mnyamata wanga, ndi mpingo uno limodzi ndi ine, kwa—kwa Mdierekezi, kwa chiwonongeko cha thupi lake, kuti mwo wake udzakhoze kupulumutsidwa.” Ndizo zonse zimene zinanenedwa. Palibe kanthu kamene kanachitika kwa sabata kapena awiri, mwinamwake mwezi kapena iwiri.

<sup>212</sup> Usiku wina Wesile uja anayamba kudwala. Ndipo pamene iye anayamba kudwala, iye anapitirira kungodwalirabe. Iye anawayitana adokotala. Adokotala anabwera uko ndipo anamuyesa iye. Iye anali ndi malungo a handrede ndi faifi, samakhoza kupeza chifukwa cha iwo. Ankangopitirira kumadwalirabe. Adokotala anati, “Mnyamata, ine sindikudziwa chimene chinachitika kwa iwe.” Iwo sanali kudziwa choti nkuchita. Anati, “Ife tiyitana katswiri.” Iwo anayitana katswiri ndipo katswiri anabwera mkati mmenemo. Iwo anamutengera iye ku chipatala, anamuyesa iye, china chirichonse, iye anati, “Ine sindingakhoze kukuuzani inu basi, mnyamatayu ali chabe—akungowoneka mwaimfa.” Mkazi wake atayima poteropo, akulira ndi chirichonse monga choncho. Ndipo ana atayima mozungulira bedilo, ndipo aliyense monga choncho. Iye anati, “Iye akupita, ndizo zonse.” Anati, “Kugunda kwake ndi kupuma kukungomatsikira pansu nthawi zonse.”

<sup>213</sup> Iye anati, “Kawayitaneni bambo.” O, inde, ndiyo njira yochitira izo. Ndi imeneyo. “Kawayitaneni bambo.” Ndipo abambo ake anathamangira kumeneko ku chipatala mwaliwiro kwambiri kuti akamuwone iye. Iye anati, “Bambo, ine sindingakhoze tsopano, koma Mulungu akumva mawu anga, ine ndikonza chirichonse bwino. Ine ndikonza izo bwino. Inde, ine nditero.” Inde, bwana, m’bale, apo pomwe kupuma kwake kunayamba kubwerera kwa ubwino.

<sup>214</sup> Ndipo Lamlungu lotsatira, iye anali atayimirira pamaso pa mpingo, iye anati, “Ine ndachimwa pamaso pa Mulungu mu kukhalapo kwa mpingo uwu. Ine ndinakana kuti ndimvere mawu a abusa. Ine—ine ndinakana kuti ndiwamvere adikoni pano.” Ndipo anati, “Ine ndikuwupempha mpingo uno kuti undikhululukire ine chifukwa cha choyipa chimene ine ndachichita monga choncho.” Anati, “Mulungu wapulumutsa moyo wanga.” Ine ndikukuuzani inu, iye anafola moyenera. Eya.

Ndicho chimene icho chiyenera kukhala, mukuona. Mukuona? Inu, ngati inu mutangochita izo njira ya Mulungu! Mukuona?

<sup>215</sup> Tsopano, onani, momwe ife timachitira, ife timakhala ndi msonkhano wa gulu, ndipo ife timanena kuti, “Chabwino, tsopano, kodi ife timusunge . . .” Ine sindikunena Kachisi, koma ine ndikutanthauza ife anthu Achiprotectanti, ife timakhala ndi msonkhano wa gulu, “Ndipo kodi inu mukuganiza chiyani za Yonasi? Kodi inu mukuganiza kuti ife tichite nawo chiyani iwo? Ine ndikuganiza kuti angapange membala wabwino wa Amethodisti kuposa momwe iwo amachitira ndi ife.” Ndi zimethozotu. Izo, ndiko kulakwitsa. Ndicho chifukwa ife sitiswa kumatsatira miyambo yawo ndi bishopu wina woti tizichita kumutcha iye, kapena ena, nchiyani chimene inu mumawatcha iwo, bambo wabomalo mu mpingo wa Chipentekoste uwu, Mkulu wa Bomalo, kumuyitanira iye mkati kuti adzawone khalidwe la munthu uyu.

<sup>216</sup> Baibulo limatiuza ife choti tichite. Ndicho chifukwa ife sitimapusitsidwa ndi zipembedzo zawo. Ife timakhala afulu kwa chinthu chimenecho. Ameni. Simupenga pa ine, monga muli? Musati inu muchite zimenezo. Ine mwinamwake ndipeza mafunso ena owopsya bwino mawa usiku, koma ife tidza . . . Ndiko kulondola, mwaona.

<sup>217</sup> Kumbukirani, ayi, ine ndikunena izi tsopano. Inu anthu amene muli pano ochokera ku mipingo yosiyana ya zipembedzo, chipembedzo chanu . . . M’bale, ine sindikunena kuti inu sindinu Mkhristu. Ine sindikunena kuti chipembedzo chanu mulibe zikwi za Akhristu okondeka mmenemo. Ine ndikuyesera kunena chifukwa chimene ife sitiri chipembedzo. Chifukwa ine sindikanakhoza basi kuyima nazo zimenezo. Ayi, bwana, ine ndithudi sindikanatha, ngakhale kuyesa kumakuuzani inu choti muchite. Ngati Mulungu anandiyitana ine kuti ndizilalika Uthenga, ndiye ine ndilalikira Iwo momwe Mulungu akundiwuzwa ine kuti ndizichita Izo. Ndizo basi—momwe izo zinalembedwera umu mu Baibulo. Ngati izo sizigwirizana ndi Izi, ndiye ndizo izo . . . Mulungu adzandiweruza ine chifukwa cha izo. Koma ngati ine—ngati ine—ngati ine ndiwona nkhandwe ikubwera, kapena mdani akubwera, ndipo ine nkulephera kuwachenjeza iwo, ndiye Mulungu adzandifunsa ine. Koma ngati ine ndikuchenjezani inu, ndiye izo ziri kwa ine ndiye. Mwaona?

<sup>218</sup> Kumbukirani, umo mu masiku otsiriza, nthawi zowawitsa izo zidzabwera, anthu adzakhala odzikonda okha, onyada, odzitukumula, amwano. Mwaona, amwano, “O, iwo ndi gulu la zitsiru. Masiku a zozizwitsa anapita kale. Palibe chinthu choterocho.” Iye ndi mneneri wachikulile wonyenga. “Tsopano, ife tikudziwa kuti akazi athu ali nako kuganiza kochuluka monga amuna athu.” Ine sindikutsutsa zimenezo pang’ono, koma Baibulo la Mulungu linati msiyeni iye kunjira kwa guwa. Ndizo—

ndizo zabwino mokwanira kwa ine, onani, ndiko kulondola. Chabwino. Mwaona? Ndipo anati, “Chabwino, tsopano, zipembedzo zathu, ife tiri nawo anthu abwino ambiri monga inu muli nawo ku Kachisi uko.” Ine sindikunena izo pang’ono, koma Baibulo limatsutsa zipembedzo. Ndiko kulondola. Ndipo koteru, tsopano, ine sindikunena kuti inu mulibe mamembala abwino mu tchalitchi chanu. Izo nzodabwitsa. Iwo ndi anthu abwino. Ena a anthu abwino kwambiri, ine ndimakomana nawo iwo monse mwa iyo, Akatolika ndi onse kupyola. Onse a iwo, ine ndimakomana nawo mamembala abwino.

<sup>219</sup> Tsopano, momwe ife tikuti tibweretsere izi tsopano, amzanga, ngati Ambuye alola, mu kuphunzira kotsatira kungapo uku, mwinamwake ine ndikulolani inu kuti mudziwe mawa mmawa ngati ife tiyenera kuti tithamange mawa madzulo kapena ayi, mwaona, kuti tizitulutse izo. Chifukwa chimene ife tikuyesera kuchita izi, ine ndikufuna kuzibweretsa izo pansu ku malo tsopano. Tsopano, ngati inu mukufuna kuti mumubweretse winawake limodzi nanu, ndinu olandiridwa mwangwiwo kuti muchite zimenezo. Koma kumbukirani tsopano, musati—musati mupite kutali mukungoyesa kuti mupeze zolakwika, kapena kubwera kuno. Ine ndikungoyankhula kwa anga—osonkhana anga, inu mukuona. Ine sindimaphunzitsa izi kunja kwa osonkhana anga pano, chifukwa ndiyo ntchito ya munthu wina, yemwe ali m’busa wa nkhusa zimenezo. Ndipo ine ndiri chabe. . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

<sup>220</sup> Kubwerera kumene ku Genesis, iye azikoka izo mopyola kumene ndi kuwona pamene izo ziri. Tsopano ife tikupita mmbuyo ku Genesis kuti tikapeze chifukwa chimene mwana wapathengo sakanati alowe mu msonkhano wa Ambuye kwa mibadwo khumi ndi inai. Momwe izo zimatengera. . . Izo zikanakhala zaka mazana anai kuti tchimo limenelo litheretu. Momwe ife titi tipezere momwe kuti ku—kusalungama kwa makolo kukuchezeredwa kwa ana ndi ana, momwe izo zinayambira mu Genesis, ndi zina zotero.

<sup>221</sup> Ndiyeno inu mudzawona momwe izo, kupita njira yonse mmbuyo, kuti Mulungu, asanakhalepo maziko a dziko, atomu imodzi isanaphulike konse mmbuyo umo pasanakhale konse zowalitsa mmwamba kukhala ziripo konse, Mulungu anadziwa cholengedwa chirichonse ndi chirichonse chimene chikanadzakhalapo konse pa dziko lapansi. Kodi alipo aliyense pano, inu simukanakhoza kufotokoza chimene mawu, ndi kuwaswa iwo apo, ndi kunena chimene mawu oti “wopandamalire” amatanthawuza? Monga ngati kutembenezira kamera yanu ku—ku kopandamalire, iyo basi—ndiyo kuchokera pamenepo mpakana. Ndizo zonse, mwaona, kupandamalire. Ndipo ife sitingakhoze, mu malingaliro amalire, kumvetsa konse chimene malingaliro opandamalire akanakhoza kulingalira. Mwaona, ife sitingakhoze kuchita zimenezo. Inu,



inu simungakhoze kuchita zimenezo. Mukuona? Koma ngati inu mukanangoti mupenye, kugwira mu Mzimu, inu mukhoza kukumverera iko kutali komwe uko, ndi—ndiyeno nkubwerera kuno mu Lemba ndipo inu muwona tsopano, kuwona, kutali maziko a dziko asanayikidwe konse.

<sup>222</sup> Tsopano, Baibulo linanena kuti Yesu Khristu anali Mwanawankhosa wa Mulungu. Tsopano mvetserani mwatcheru kwenikweni, kotero ngati ena a inu simukhalapo muno mawa kuti mumve izo ndikuzitsirizitsa. Baibulo linanena kuti Yesu Khristu anali Mwanawankhosa wa Mulungu wophedwa kuchokera ku maziko a dziko. Ndi kulondola uko? Kodi Iye anaphedwa liti? Kuchokera ku maziko. Ndilo dziko, ngati ilo linapangidwa kuchokera ku mulu wa maatomu oswedwa, amene anachoka ku dzuwa kutali, ilo lisanakhale chimenecho. Ndiye pasanakhale konse atomu itayamba yaswekapo mu dzuwa, ngati iyi inali chowalitsa chochokera pa dzuwa, imene ikanakhala mazana bilioni trilioni, trilioni matrilioni a zaka mmbuyo pasanakhale konse ngakhale chowalitsa chimodzi chamwamba, Khristu anaphedwa. Pamene lingaliro lalikulu la Mulungu likhazikika pa chinthu chimodzi, ndi chinthu chotsirizidwa. Pamene Mulungu anati, “Lolani kuti kukhale,” izo zatsirizidwa kale. Ngati izo zinatenga zaka mazana mabilioni kuti zithe, ndi zotsirizidwa kale mwamsanga monga pamene Iye ananena izo. Ndipo pamene Mwanawankhosa anaphedwa kuchokera ku maziko a dziko, Baibulo lomwelo, Mzimu womwewo unalemba ndipo unati, “maina athu anayikidwa mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko asanakhalepo.”

<sup>223</sup> Kotero munthu yemwe analemba nyimbo, “*Pali Dzina Latsopano Lalembedwa Umo Mu Ulemerero*,” iye anali nalo tanthauzo labwino, koma iye sanali mwamalemba. Mwaona? Dzina limenelo linalembedwa umo mu Ulemerero pamene dziko...pamene dziko linali lisanayambe konse. Pamene Mwanawankhosa anaphedwa, maina athu anayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa.

<sup>224</sup> Ndiroleni—ndiroleni ine ndingokutengerani inu Lemba limodzi laling’ono. Kodi inu muyembekezera miniti imodzi yokha? Ili langobwera mu malingaliro anga tsopano. Ine ndikuganiza ine ndikhoza kutembenukira kumene kwa ilo. Ine sindiri wotsimikiza. Ndipo tsopano ine ndikupepesa kamba kokusungani inu motalika chonchi, koma ine ndinakuuzani inu kuti ukanakhala mpaka pakati pa usiku, izo siziri kwenikweni moyipa chotero. Koma ine—ine ndikungofuna kuti—kuti nditenge izi, Lemba limodzi ili lokha kwa izo. Tembenezani ndi ine tsopano ku Bukhu la Aroma, ndipo ine ndikufuna kuti—kuti muwerenge izi ndi ine. Tsopano, tiyeni tiwone, Aroma, ngati ine ndingakhoze kuzipeza izo, poyandikira ndi apa pomwe. Tsopano tiyeni titenge Aroma 8, ndipo—ndipo tiyeni tiyambire

ndime ya 28 ya mutu wa 8 wa Aroma, ndipo ine ndikufuna inu kuti muwerenge basi mwapemphero ndi ine tsopano. Mvetserani pano basi chimene Mulungu ananena tsopano.

*Ndipo ife tikudziwa kuti zinthu zonse zimachitira ubwino kwa iwo amene amakonda Mulungu, kwa iwo amene ali . . . oyitanidwa molingana ndi cholinga chake.*

*Pakuti amene iye anawadziwiratu, . . .*

225 Yemwe anakupatsani inu . . . kodi mungakhoze kuwerenga ndi ine? “Pakuti iye . . .”

*Pakuti iwo amene iye anali atawadziwiratu, iye naponso anali atawakonzeratu, chabwino, kuti akapangidwe mwa fano la Mwana wake, kuti iye akakhoze kukhala woyamba kubadwa pakati pa abale ambiri.*

*Kuwonjezera apo amene iye anali atawakonzeratu, iwo iye naponso anawayitana: ndipo omwe iye anawayitana, iwo iye naponso anawalungamitsa: ndipo omwe iye anawalungamitsa, iwo iye ndiponso anawapatsa ulemerero.*

226 Kuchokera ku maziko a dziko, pamene Mulungu anayang’ana pansi. Tsopano, Mulungu samayendetsa udindo Wake, kuti, “Chabwino, tsopano, ine ndipita kuti . . . O, kodi ife tichita chiyani tsopano?” Mwaona? Palibe kanthu . . .

227 Kumbukirani, kusalungama, tchimo ndilo kulungama kutapotozedwa. Mdierekezi sangakhoze kulenga. Kodi nonse—nonse mukumvetsa zimenezo? Ndicho chiphunzitsa cha mpingo uno. Mdierekezi sangakhoze kulenga. Iye akhoza kupotoza chimene Mulungu wachilenga. Tsopano, kodi kupotoza ndi chiyani? Pano, inu nonse mukuoneka ngati akulu, mochulukira. Mvetserani kwa izi. Ndife anthu okwatira. Ndipo inu amuna okwatira ndi inu akazi okwatiwa mukhoza kukhala limodzi monga mwamuna ndi mkazi, ndipo akazi amenewo ali basi mofanana ngati iwo sanachitepo . . . iwo ndi anamwali mwakutalika konse ngati inu muzikhala ndi mwamuna wanu. Ndiko kulondola. Tsopano, ndizo zololedwa ndi mwalamulo, ndipo ndi zonse zabwino, ndi zodzozedwa ndi Mulungu kuti muzichita chomwecho. Mkazi wina akhoza kuchita mchitidwe womwewo wa mkazi wanu. Umodzi wa iwo, ndinu wolungama pamaso pa Mulungu; ndipo mchitidwe womwewo kwa mkazi wina, ndiwe wotsutsidwa pamaso pa Mulungu, ku imfa. Ndi chiyani chimenecho? Chilungamo chopotozedwa, mwaona, chilungamo chopotozedwa. Tsopano, Mdierekezi sangakhoze kulenga, koma iye amapotoza zimene Mulungu walenga kale.

228 Bodza ndi chiyani? Ndi choona chopotozedwa. Winawake anati, o, “Ilo linali Loweruka usiku, naini koloko, eya, Bill Branham anali mu Jeffersonville.” Kukhoza. “Kumusi uko kwa Anthony, ataledzera.” Bodza. Chinali chiyani icho? Ine

ndinali mu Jeffersonville, izo nzoona. Icho chinali chilungamo chitapotozedwa kukhala bodza. Mukuona chimene ine ndikutanthawuza? Onani, bodza limapotoza cholondola. Ndi chinachake chimene chinanena kumene ine ndinali. Tsopano, ngati izo zikanati, “Ku tchalitchi, akulalikirira.” Kukhoza. Ndicho chilungamo, iye ananena zoon. “Ku tharaveni, akumwa.” Bodza. Zopotozedwa, mwaona, choona chitapotozedwa. Mukuona zimene ine ndikutanthauza? Kusalungama konse ndi chilungamo chitapotozedwa.

<sup>229</sup> Imfa, ndi chiyani iyo? Moyo wopotozedwa. Matenda? Thanzi lopotozedwa. Iwe umayenera kukhala uli munthu wabwino wamphamvu. Chabwino, ngati uli wodwalika, ndi chiyani chimenecho? Thanzi lako lapotozedwa. Mwaona, ndizo zonse zimene ziripo kwa izo. Ndi chiyani icho? Inu poyamba munali akazi aang’ono okongola, ndi amuna okongola wamphamvu, tsopano inu mukuchita makwinya ndi kuyamba kukalamba, ndi chiyani chimenecho? Moyo wapotozedwa, onani, kubwerera mmbuyo mozungulira kachiwiri. Mwaona? Ndipo izo zimayenera kubwerera mmbuyo, lidalitsidwe Dzina la Ambuye, Mulungu walonjeza kuti azibwezera izo mmbuyo. Ndipo basi motsimikiza monga ziri. . .ngati izo ziri, ife tikudziwa kuti ziri pano; koteri basi motsimikiza monga izo ziliri, Mulungu wati abweretsa mmbuyo izo kachiwiri. Iye analonjeza izo ndipo analumbirira kuti Iye adzachita zimenezo. Ndicho chimene chimatipatsa ife. . .

<sup>230</sup> Tsopano, kodi ife tikuyenera kukhala anthu a mtundu wanji? Tsopano zindikirani momwe zinthu izi zimachitikira. Tsopano, iwo amene Iye anawadziwiratu, Iye anawayitana; iwo amene Iye anawayitana, Iye anawalungamitsa iwo. Liti? Maziko a dziko asanayikidwe, dziko lisanayambe konse. Tsopano, ngati ife tikanakhoza kutenga Lemba ili ndi kulilungamitsa ilo kwenikweni, ife tikanatenga maora pa ilo, koma ife—sitikufuna kuchita zimenezo. Koma kusalungama konse uku kuno, ndiko chilungamo chitapotozedwera ku kusalungama. Ndicho chimene Mdierekezi amachita. Tsopano, pamene iwe ufika pa usinkhu wa kuzindikira, ndipo iwe ukudziwa chimene chiri cholakwika ndi chokhoza, iwe umayenera kuti utembenuke kuchoka ku cholakwika chako. Chifukwa, iwe unabadwira mu tchimo, kuwumbidwa mu kusaweruzika, kubwera ku dziko ukuyankhula mabodza. Ndiye ndiwe—ndiwe makamaka wobadwa mwa chikhumbo cha kugonana, ndiyeno iwe uyenera kuti ubadwe kachiwiri polinga kuti ulandire kubadwa kwatsopano, kuti ukalowe Kumwamba. Chifukwa mabadwidwe a mtundu uwu amene inu muli nawo kuno. . .

<sup>231</sup> Inu mukuona pamene a Mboni za Yehova akanakhalira olakwitsa motalika kwambiri pamenepo, poganiza kuti kubadwa kwatsopano ndiko chiwukitsiro cha thupi, inu

mukuona. Iko sikukanakhoza kukhala. Mwaona? Iko kuyenera kuti kukhale chinachake. . .

<sup>232</sup> Inu, inu muli mu danga la nthawi, ndipo chinthu chokha chimene chiri Chamuyaya chiri chinachake chimene chinalibe chiyambi kapena chopanda mapeto. Chirichonse Chamuyaya chinalibe konse chiyambi, kapena icho sichidzakhala nawo konse mapeto. Mwaona? Koteri ngati inu muli gawo la Mulungu, Mzimu umene uli mwa inu unalibe konse chiyambi kapena sudzakhala nawo konse mapeto, ndipo ndinu Wamuyaya limodzi ndi Mzimu umene uli mwa inu. Mwaona? Monga chi—chi—chikondi cha agapao, ndiye icho chimabwera pansu ku chikondi cha phileo, ndiyeno kutsika mpaka ku chikondi cha kukhumbira, icho chimangokhala chikupitabe pansu ndikupitabe pansu, kumapotoza mopitirirabe pansu mpaka izo zimabwera ku chisakanizikiro basi cha uve bwanji. Bwanji, njira yokha, Yesu anabwera pansu pa makwerero omwewo pansu pano kuti adzanyamulire mmwamba ndi kuwatengera mmbuyo kachiwiri ku mawonekedwe apamwamba; kuchokera ku mawonekedwe otsikitsitsa, kuchokera ku imfa kupita ku Moyo, kuchoka ku matenda kupita ku thanzi, kuchoka ku kusalungama kupita ku chilungamo. Mukuona? Iye anakhala wochokera ku chapamwamba kufika ku chotsikitsitsa, kuti Iye akakhoze kubweretsa chotsikitsitsa kupita ku chapamwamba. Iye anakhala ine kuti ine ndikakhoze kupyolera mu chisomo Chake kukhala Iye, wolowa mmalo wa Mpandowachifumu mu Ulemerero. Mukuona chimene ine ndikutanthauza, zinthu zimenezo? Tsopano penyani, kutali mmbuyo dziko ili lisanayambe mu ma atomu amenewo mmbuyo kutaliko, pamene Mulungu anawona zimene zinali zoti zikachitike, apo pomwe Iye anakuwonani inu, Iye anandiwona ine, Iye anawona utitiri uliwonse, ntchentche iliyonse, chule aliyense, tongole aliyense, chirichonse chimene chikanati chidzakhalepo pa dziko lapansi, Iye anachiwona icho nthawi yomweyo. Zedi, Iye anatero.

<sup>233</sup> Tsopano, Iye sananene konse, “Ine ndidzamatuma Mwana Wanga wamwamuna pansu ndi kukumulola Iye kuti afe, ndipo mwinamwake winawake angachitire chisoni pa Iye. Ndipo iyo idzakhala nkhani yochititsa chisoni chotero, iwo. . .kapena mwinamwake winawake angakakhoze kukapululumutsidwa.”

<sup>234</sup> Iye anadziwiratu yemwe akanati adzapulumutsidwe! Inde, bwana. Iye anati, “Esau ine ndimamuda, ndipo Yakobo ine ndimamukonda,” nkuti mmodzi aliyenseyo asanakhale nawo konse mwayi woti atsimikizire chimene iwo anali, chifukwa Iye ankadziwa chimene iwo anali. Iye ankadziwa. Iye amadziwa chirichonse. Iye anadziwa chimene inu mukanadzachita, inu musanabadwe, ndi pamene dziko linkayamba.

<sup>235</sup> Tsopano penyani, monga inu mukudziwira, ine—ine—ine ndine munthu wa mfuti. Ine—ine ndimakonda mifuti. Ndipo mkazi wina mu Texas, ine ndikukhulupirira ndi

Texas, anandigulira ine Swift, Swift ya .220. Ine nthawizonse ndinkafuna imodzi, ine ndinkafuna kuyifufuza iyo. Ndi mfuti yaying'ono yowombera mwamphamvu kwambiri. Ndi ya zipolopolo makumi awiri ndi ziwiri, chipolopolo cha machaka makumi anai mphambu zisanu ndi atatu, ndipo iwe ukhoza kuyigwira iyo... Tsopano, fakitare imati, "Musati muchite izo, njowopsya kwambiri." Koma iwe ukhoza kuchigwira chipolopolo chimenecho mpaka pa mapazi zikwi zisanu pa mphindi, ndipo nkukhala atayigwirabe iyo mu malo ake. Mapazi zikwi zisanu pa mphindi, ndi mailo pa mphindi. Mwa kuyankhula kwina, chiombankhanga chitakhala pa mayadi mazana awiri, iwe ukhoza kuchiwombera chiombankhangacho ndi kuwona nthenga zikuwuluka mfutiyo isanakukankhe iwe konse. Mwaona? Iyo, koma iwe ukatenga mbali ya mphwanthimpwanthi ya chotokosera mmano ndi kuyifikitsa iyo mu wonga wako, ndi kutsanulira wochulukuka *choncho* kenanso mmenemo, wokwanira basi umene iwe ungakhoze kuwunyamula iwo pa chotokosera mmano; ndipo iwe ukhoza kuwombera pa nguluwe atakhala pa mapeto a nyumba iyi kuno, ndipo iyo ikanangokhala ndi kumayang'ana pa iwe. Chavuta ndi chiyani? Chipolopolo chimanyenyeka, icho chikupita mwaliwiro kwambiri. Ndipo iwe ukhoza kuyika chipepala pakati pa pano ndi apo, ndipo iwe sudzawona nkome ngakhale kachidutswa kamodzi kakang'ono kakugwa pa chipepalacho. Icho chimangobwerera mmbuyo. Osati ku—ku maphulusa, phulusa laphala; koma icho chimapita kutali kuposa pamenepo. Icho chimapita mmbuyo ku zidulo zapachiyambi zimene zimapanga kopala ndi nkala zimene ziri mmenemo. Icho chimapita mmbuyo monga icho chinali zaka mabilioni zana zapitazo. Tsopano, pano pali chipolopolo chaching'ono, machaka makumi anai mpambu zisanu ndi atatu a chipolopolo, ine ndikuchigwirizira mu dzanja langa, ndipo mphindi yotsatira icho chabwerera ku chimene icho chinali zaka mamilioni zana zapitazo. Ndipo ngati dziko likanadzakhala mwinamwake litayima zaka zina mamilioni zana, icho chikanadzabwereranso kudzakhala chipolopolo kachiwiri, chikhoza kubweretsedwa kumene mmbuyo, pakuti iye anachiwumba mu kopala kumene.

<sup>236</sup> Tsopano penyani chimene Mulungu anachita, ndiyeno inu mumukonda Iye, ndiye inu muzipita kwanu, ndipo mmawa inu mukagona mochedwa pang'ono ndipo—ndipo inu—inukamukonda Iye kuposa konseko. Tsopano, Mulungu ndi Womanga. Ndi angati amadziwa zimenezo? Iye ndi Mmisiri. Chabwino, mvetserani mwatcheru kwenikweni. Tsopano, Mulungu mmbuyo kutaliko, iwo amati... Tsopano ife titenga lingaliro la owerengerazaka pa izo. Mulungu, zaka mabilioni zana zapitazo, pamene Iye ankati kuti apange dziko, chabwino, Iye anangoyamba. Tsopano Iye anali ndi... Iye anali nalo ganizo mu malingaliro Ake.

237 Tsopano inu munena kuti, “Ngati Iye ali wamkulu chotero, M’bale Branham, Iye analolera motani kuti Mdierekezi apange tchimo?” Chabwino, Iye ankadziwa Mdierekezi asanalengedwe konse kuti iye akanadzakhala Mdierekezi. Ulemerero! Tsopano ine ndikumverera mwachipembedzo. O, mai! Iye anadziwa Mdierekezi asanalengedwe kuti iye akanadzakhala Mdierekezi. Tsopano inu mukufunsa, “Nanga bwanji zimenezo?” Inu mukuti, “Chifukwa chiyani Iye anamulola iye kuti akhale Mdierekezi?” Kutu Iye akakhoze kutsimikiziridwa kuti ali Mulungu. Ndicho chifukwa Iye anachitira zimenezo. Chifukwa chiyani kunakhalapo konse kusalungama?

238 Bwanji, nchiyani chinali choyamba, Mpulumutsi kapena wochimwa? Nchiyani chinali choyamba? Mpulumutsi. Nchiyani chinali choyamba, Mchiritsi kapena munthu wodwala? Nchifukwa chiyani kunaloledwa kuti kukhale wochimwa? Chifukwa zikhumbo za Iye ziri Mpulumutsi. Ngati pakanapanda kukhala konse wochimwa, Iye sakanakhoza kudziwika konse ngati Mpulumutsi. Aleluya! Iye akhoza kupanga zinthu zonse kuti zipite mozungulira kwa ulemerero Wake. “Kodi wowumba anganene kwa . . .” Kapena, “Kodi m’phika ungakhoze kunena kwa wowumba, ‘Inu munandipanga ine chotere?’” Ndi ndani yemwe ali pa gudumu? Ndani yemwe ali ndi dongo? Ndi manja a ndani omwe ilo lirimo? Paulo anati, “O, munthu wopusa, kodi Iye sananene kuti Iye anamuwutsa Farao chifukwa cha cholinga chomwechi?” Ndithudi, Iye anadziwa izo dziko lisanakhalepo, Iye anadziwa yemwe akanati adzakhale chiyani. Ndipo Iye analola kukhale tchimo kuti Iye akakhoze kukhala Mpulumutsi. Iye analola kuti kukhale matenda kuti Iye akakhoze kukhala Mchiritsi. Iye analola kuti kukhale kudana kuti Iye akakhoze kukhala chikondi. Zedi, Iye anatero. Iye ndi Mulungu, ndipo izo ndi zikhumbo Zake, ndipo Iye ayenera kuti akhale nacho chinachake kuti awonetsere zikhumbo Zake.

239 Inu mukanadziwa bwanji konse kuti kunali usiku, inu mukanadziwa konse bwanji kuti unalipo konse; ngati iwo unali wonse kuwala kwa usana, inu mukanadziwa bwanji kuti kunali usiku. Ulipo usiku kuti iwo ukhoze kutsimikizira kuwala kwa masana. Zedi, ulipo iwo. Ameni. Inu mukuona chimene Iye anachita?

240 Koma pamene Iye anali mmbuyo kotaliko asanayikidwe maziko a dziko, Iye asanatenge dzuwa lakale ili ndipo Iye analisuntha ilo mozungulira nyenyezi yakale iyi imene ife tikukhalapo tsopano, dziko lapansi ili, ndipo Iye analiwumba ilo pa dzuwa ili, ndipo analiyika ilo lizizungulira dzuwa. Titi, *pano* pali dzuwa. Iye analiwumba ilo ku mbali *iyi* ndi kulilola ilo kupachikika pamenepo kwa zaka mabilioni zana. Kodi Iye anali akupanga chiyani? Mipweya yina. Iye anasunthira mozungulira ku mbali *iyi*, Iye anapanga chinachakenso. Kodi Iye anali akupanga chiyani pamenepo? Mapotashi. Iye anasunthira

mozungulira mbali *iyi*, ndipo kodi Iye anali akuchita chiyani apa? Kupanga makashiamu. Kodi Iye anali akupanga chiyani? Iye anali akupanga inu ndi ine. Kodi Iye anali akuchita chiyani? Monga womanga akuyala zake zonse za thuwu-bayi-foro ndi ma thuwu-bayi-eyiti ake, mikwamba yake, zambali zake, iye ankadziwa basi nyumba zingati zimene iye amati azimange. Ndipo ndife opangidwa kuchokera ku mapulusa khumi asanu ndi limodzi a dziko lapansi, ndipo Iye anali akutipanga ife tonse, ndipo anatiyala ife kunja uko dziko lisanabwereco konse... Ndipo ilo mwina linali lotalika mobulungika pa nthawi imeneyo, ine sindikudziwa chimene ilo linali. Kodi Iye anali kupanga golide, ndi kopala, ndi mkuwa, ndi madzi, ndi zinthu zonse izo za chiyani? Iye ndi Womanga. Iye ali mwina. . . Mmisiri, Iye anali akuyala chirichonse kunja uko, anali atadula chirichonse ndipo chitakonzedwa. Pamene Iye anafika pokonza izo zonse, iko kunali basi kuphulika kwakukulu kwa chiphala chamoto. Iye analola maphala amoto amenewo kuti azizire pamenepo kwa zaka mamilioni zana, kuti apange makashiamu. Ndi chiyani chimenecho? Ndilo gawo la inu.

<sup>241</sup> Ndiyeno, kusanakhale konse chidutswa chimodzi cha moyo pa dziko lapansi ili, matupi athu anali alipo apa. Aleluya. Lisanakhalepo dontho limodzi la chinyezi kuti libwere konse pa dziko lapansi, ife tinali tiripo apa. Pamene Adamu ankayenda chokwera ndi chotsika m'Munda wa Edeni, ine ndinali ndiripo apa. Amen. Inde, bwana. O, ulemerero! Pamene Akerubi, nyenyezi zammawa zinkayimba limodzi, ndipo ana a Mulungu ankafuula mwachisangalalo, ine ndinali ndiripo apa kumangoyembekezera kupuma kwa moyo kuti kubwere. Ine ndinali pano. Iye anandipanga ine pano, ndinali nalo thupi langa liripo apa. Inde, bwana. Ilo silinali kumene inu mumachokerako. Mai, kodi ilo linafika bwanji kuno? Mulungu anali nazo izo ziri kuno. Mulungu analipanga ilo. Ndife opangidwa kuchokera ku maphulusa khumi asanu ndi limodzi, petroleamu, potashi ndi kuwala kwa dziko, ndi zinazonse. Mwaona, ife tinali tiripo kuno.

<sup>242</sup> Ndiye nchiyani chinachitika? Ndiye Mulungu ananena kwa Mzimu Woyera, ife tingo zitenga izo mwa mawonekedwe ophiphiritsa, “Tsopano Iwe upite apo, ndipo Iwe upite uzikapanga chikondi kwa dziko limenelo, chifukwa Ndine Chikondi ndipo Ndiwe chotuluka kwa Ine, kotero tsopano Iwe upite uzikapanga chikondi kwa dziko.” Ndipo Mzimu Woyera waukulu, ife tikuganiza, unabwera kunja uko, mu mawonekedwe chabe a chithunzi tsopano. Izo sizinali mwa njira imeneyo. Ndithudi, Mzimu Woyera ndi Mulungu ali mwini yemweyo, cholinga chomwecho, cholinga chamwiniyemweyo, Munthu. Mundikhululukire ine. Ndipo kungonena kuti Iye anatambasula mapiko Ake mozungulira dziko lapansi, Iye anayamba kufungatira. Kufungatira kumeneko ndi chiyani?

Monga nsoti kwa anapiye ake, kuluku, akupanga chikondi, “kuluku, kuluku, kuluku.” O.

243 “O moyo, tulukira apa!” Iye anafuula. Iye anayang’ana pozungulira. “Ine ndikufuna kukongola pa dziko lapansi ili. Tulukira apa, kuwala!” Mzimu Woyera ukusuntha. Ndipo pamene Iye anatero, ine ndikuyang’ana chikubwera, pali kulira pansi pa phiri kutaliko, kutaliko kukubwera makashiamu akutsanuliridwa pansi, ndipo akusakanizana ndi potashi. Kodi izo zikupiringizikira mu chiyani? “Moyo, tulukira apa!” Duwa laling’ono la Chiwukitsiro linatulutsa mutu wake mmwamba kuchokera pansi pa thanthwe. “Bwerani kuno, Atate, tayang’anani pa ilo.”

244 “Izo zikuwoneka bwino, basi zipitiriza kufungatira.” Iwo unafungatira nutulutsa maluwa, Iwo unabweretsa kunjja zomera zonse, Iwo unabweretsa kunjja moyo wa zinyama, ndipo mbalame zinawuluka kuchokera mu fumbi. Patapita kanthawi, apo panabwera mwamuna ndi mkazi; apo panabwera mwamuna, ndipo mwamuna anali zonse mwamuna ndi mkazi. Osati wa ziwaloziwiri, tsopano; basi—basi mwa iye.

245 Panali mzimu wachikazi. Pamene inu mumutenga mwamuna yemwe ali wachikazi kwambiri, iye akhoza kukhala wabwino, wolunga bwinobwino, koma pali chinachake cholakwika. Ndipo pamene inu mumutenga mkazi, wofuna azidula tsitsi lake ndi kumavala maovololo, ndi kumatuluka kunjja uko, “Ndi kudalitsa Mulungu, ine ndikukuuzani inu,” apo pali chinachake cholakwika. Mkazi ali ndi mzimu wachikazi, ndipo mwamuna ndi wamphongo. Ife timadziwa zimenezo, ndipo inu mumadziwa zimenezo. Kodi mkazi amawoneka bwino yemwe akuyesera kukhala, kumachita monga mwamuna?

246 Bwanji, ine ndinakhala nthawi yina, ine ndinali wosamalira zinyama kuno, ndipo ine ndinakhala mu basi ndipo ndinkapita kumeneko ndipo ndinali kumamumenya mkazi ameneyo pa mwendo, ndi dzanja langa, ndikuyankhula kwa iye, ndipo ine sindinali kudziwa kuti uyo anali mkazi. Iye anali atavala zipewa za owotcherera izi ndi magalasi aakulu monga *choncho*, ndipo ine ndinali nditakhala kumene kumbuyo uko, ndipo iye anali kundiwuza chinachake chimzake za chinachake chimene chinachitika. Iye anati, “Inu mukudziwa,” ndipo iye anati, “ndipo usiku watha,” wowoneka moyipa basi monga iye akanakhoza kukhalira, akusuta ndudu. Iye anati, “Usiku watha, ine ndikukuuzani inu, munthu ameneyo anateleleka pamwamba pa chinthu chimenecho,” ndipo anati, “mai, iye anabwera akuserereka kupyola pamenepo.” Anati, “Ine sindinasekepo mochuluka choncho mu moyo wanga.”

247 Ndipo ine ndinali kuseka, inu mukudziwa, monga choncho. [M’bale Branham akupanga phokoso la kuwomba—Mkonzi.] Ine ndinati, “Mnyamata, uyo anali wina, sichoncho?” Nditakhala



pamenepo ndikuyankhula monga choncho. Ndipo ngati iye akanapanda kuchotsa chinthu chimenecho ndi kugwedeza mutu wake, ndipo iye anali ali ndi chitsitsi pamenepo kuti iye anali mkazi. Ine sindinayambe ndamvererapo mochepa chotero mu moyo wanga. Ine—ine ndinati, “Kodi ndinu mkazi?”

Iye anati, “Bwanji, zedi!”

<sup>248</sup> Ine ndinati, “Mundikhulukire ine.” Ine ndinali ndisanawonepo zoterozi. Tsopano, izo zinali zoono.

<sup>249</sup> Ine ndinawona chikwangwani tsiku lina chimene chinakhala ngati chikanandidolera ine. Iwo anali ndi chikwangwani chachikulu pamwamba, chinati, “Madona okonzeka kuvala zovala.” Ine ndinaganiza, “Mulungu alemekezeke chifukwa cha zimenezo.” Mwaona? Koma, ndinadzapeza kuti, izo zinali chabe mtundu wina wa zovala zimene iwo anali atapanga kale, inu mukudziwa. Ine—ine ndimaganiza kuti iwo anali oti akavale kwenikweni zovala. Ine ndithudi ndinatero. Anati, “Madona ali okonzeka kuvala zovala.” Ine ndinati, “Mulungu alemekezeke chifukwa cha iwo. Ndizo zabwino. Ndiko kulondola, ine zedi ndikuthokoza Ambuye chifukwa cha izo.” Koma, onani, izo zinali chabe mtundu wina wa zovala zimene iwo anali atazipanga kale, chinachake. Icho chikanakhoza kukhala chinachake choseketsa, sichingakhale icho, mu dziko ili? Chabwino.

<sup>250</sup> Ndiye pamene Adamu anabwera apo. Ndiyeno Adamu ankawoneka wosungulumwa, kotero Iye anatenga nthiti kuchokera ku mbali yake ndi kumupanga Eva, chotuluka kuchokera kwa iye. Ndipo Iye anapanga, Iye anatenga mzimu wachikazi kuchokera mwa Adamu ndipo anawuyika iwo mwa mkazi, mzimu wa chikondi, wachikazi, wachifundo, waulemu. Ndipo Iye anawusiya mzimu waumphongo mwa Adamu. Tsopano, ngati pali chirichonse chosiyana, apo pali kupotoza penapake. Tsopano, ndiyeno iwo awiri anali mmodzi.

<sup>251</sup> Ndipo kotero tiyeni tingotenga sewero pang’ono ndiye ife tisanati titseke. Apa pakubwera, apa pali Adamu akumutenga Eva pa mkono ndipo iwo akuyendera kunja. Ine ndimangoyikonda nkhani iyi. Ndipo iwo akuyendera kunja, inu mukudziwa, ndipo Eva anati, “O, wokonedwa, inu mukutanthauza kuti inu muli nazo?”

“Inde, ine ndinachitcha icho.”

“Chabwino, munachitcha chiyani *icho*?”

“Chimenecho chimatchedwa kavalo.”

“A-nhu. Nchiyani *icho*?”

“Imeneyo ndi ng’ombe.”

“Inu munachitcha chimenecho?”

“Eya. A-nhu.”

252 “Munachitcha chiyani *icho*, *izo* ziwiri zimenezo zakhala apo zo mitu yawo limodzi?”

“Izo ndi mbalamezachikondi.”

253 “O, chabwino, chabwino.” Ndipo iwo amapitirizabe monga choncho. “Ndi chiyani ichi chiri *apachi*?”

“Iyo ndinachitcha icho *icho*, ndi *ichi* apa.”

254 Ndipo, “O, chabwino. A-nhu, izo ndi zokongola.” Ndipo mkango ukubangula. “Mumachitcha chiyani *chimenecho*?”

“Umenewo ndi mkango.”

“Ndi chiyani *ichi*?”

“Kambuku.”

255 Ndi zonse monga . . . “O, chabwino.” Monga ngati amphaka, inu mukudziwa, ndipo akumalira akuzungulira.

256 Kotero patapita kanthawi iye akuyang’ana pozungulira, iye anati, “Wokonedwa, tayang’anani apo, dzuwa likupita pansu, ndi nthawi yopita ku tchalitchi.” Inu mukudziwa, pali chinachake basi pamene dzuwa likulowa, iwe umafuna kupembeza. Ngati iwe supita ku tchalitchi usiku umenewo, iwe umangofuna kuti ulowe kulowa mu chipinda ndi kuwerenga Baibulo. Ndi angati amene amakonda kuchita zimenezo, kudzipatula kwa wekha? Mukuona? Izo ziri basi mwa munthu kuti azichita zimenezo. Inu muyenera kumachita zimenezo. “Nthawi yopita ku tchalitchi.”

257 Tsopano, iwo sananene konse, “Tsopano, dikirani miniti tsopano, tsopano, Yonasi ndi wa Assemblies, ndipo ife ndife a . . .” Ayi, panalibe kanthu konga zimenezo apo, kotero iwo anangopita uko. Iwo analibe tchalitchi, pokhala pabwino poti azikhalapo monga choncho. Iwo anangopita uko pansu pa tchalitchi chachikulu kwambiri cha nkhalango, ndipo anagwada pansu.

258 Ndipo Kuwala kuja kunali kutapachikika kumeneko pa thengo, mwaona. Ine ndikukhoza kumva Liwu likuyankhula pansu ndi kunena, “Kodi ana Anga adzisangalalira okha pa dziko lapansu, tsiku limene Ambuye Mulungu wanu wakupatsani inu?”

259 “Eya, Ambuye, ife tadzisangalalira tokha lero.” “Sichoncho ife, wokonedwa?”

260 “Inde, inde, wokonedwa, ife tatero.” “Ambuye, ife zedi tikukuyamikirani Inu. Tsopano ine ndikudzigoneka pansu kuti ndigone.” Mwaona? Ndipo iye akugoneka mkono wake wawukulu mowutambasula, ndipo mkaziyo akugona pansu pa mkono wake, ndipo iye akumugoneka kambuku pansu, ndi mkango pansu, ndi chirichonse pansu kuti zigone, mwamtendere chotero.

261 Kotero Mulungu akubwera pansi ndipo Iye akubweretsa pansi, o, gulu la Angelo, Gabrielo, chirengedwe Chake cha Kumwamba. Kotero iwo akubwera pansi ndipo iwo akuyenda chonyang'ama mosamala kwenikweni kulowa mu chipinda chogona, mukuona, akuyang'ana pozungulira. Gabrielo anati, “Bwerani kuno, Atate. Bwerani kuno, taonani apa. Ndi uyu apa. Apa, apa agona ana Anu agona apa.”

262 Ndi angati muno amene anayamba apitako ku mbali ya bedi, ena a inu amayi, inu ndi adadi limodzi, ndi kuyang'ana pa mnyamata wamng'ono ndi msungwana wamng'ono, ndipo inu nkungokumbutsana wina ndi mzake, “Kodi—kodi iye sakuwoneka ngati inu, motere ndi motero?” Kodi inu munayamba mwachitapo zimenezo? Bwanji, nthawi zambiri ine ndimapita ndi kunena kwa Meda, kunena zokhudza Joseph. Iye nkuti, “Bill, iye ali ndi chipumi chachitali monga iwe.”

263 “Eya. Koma, Meda, iye ali ndi maso aakulu monga iwe.” Chifukwa chiyani? Iye ndi gawo la chotuluka chathu, iye ndi chotuluka pa—pa chilumikizano chathu.

264 Tsopano, ndipo Atate anati, akhoza kunena izi zokhudza izi, anati, “Inu mukudziwa. . .” Ndipo Gabrielo anati, “Inu mukudziwa, iye akungowoneka basi monga Inu.” Ndimomomwe Mulungu amawonekera, dziyang'aneni pa inueni. Ndimomomwe Mulungu amawonekera, Iye amawoneka monga inu. Ndinu mphukira Zake. Ndi angati amadziwa zimenezo? Mukuona?

265 Tsopano penyani. Ndi chiyani mawonekedwe otsikitsitsa a moyo amene ife tiri nawo? Chule. Ndi chiyani mawonekedwe apamwamba kwambiri a moyo? Munthu. Ndithudi. Ndipo mawonekedwe apamwamba kwambiri ndi chiyani? Izo zinkangopitirira kubwera kuchokera ku chotsikitsitsa kupitirira kukwera, kuchokera kwa chule kupita kwa *ichi* kwa *icho*, ndi kwa mbalame, ndi kwa. . .o, zina zotero, mawonekedwe basi apamwamba kwambiri a moyo, mpakana izo zitafika ku mawonekedwe apamwamba kwambiri amene izo zikanakhoza kufikapo, ndiye izo zinapangidwa mwa chifanizo cha Mulungu. Apo inu muli. Ndipo mkazi sanapangidwe mwa chifaniziro cha Mulungu, koma mwa chifaniziro cha mwamuna. Mwaona? Tsopano, tsopano, apo iwo ali. Ndipo Mulungu akuyang'ana pa iwo, anati, “Inde, iwo akuwoneka—iwo akuwoneka okondeka.”

266 Kodi icho chinali chiyani, m'bale? Iwo sankasowa kuti adzafe konse. Uyo anali kokha kashiamu woyamba wodzaza dzanja, potashi woyamba, ndipo chirichonse chinayambikira apo monga choncho. Kodi izo sindizo zokongola? Koma tchimo linabwera motsatira ndipo linawononga chithunzicho. Tsopano, ali Mulungu. . . Kodi Mulungu analilola ilo kuti lichite chiyani? Nchifukwa chiyani Iye anazilola izo kuti zikhale monga ife timayankhulira kanthawi kapitako? Iye analolera izo kotero

kuti Iye akanakhoza kutsimikizira kuti Iye anali Mpulumutsi. Iye anazichita izo. Iye analola matenda kuti azichitika kotero kuti Iye akanakhoza kutsimikizira kuti Iye anali Mchiritsi. Iye analola imfa izichitika kuti atsimikizire kuti Iye anali moyo. Mwaona? Iye analola zinthu zonse zoyipa izi zizichitika kuti akatsimikizire kuti Iye anali wabwino, chimene Iye anali. Ife ti . . .

<sup>267</sup> Inu mukunena za kuyimba za nkhani ya chiwombolo! Bwanji, m'bale, pamene Yesu abwera, uwu—mpingo uwu udzayima kutsidya m'mpheapete mwa dziko lapansi ili ndi kuyimba nkhani za chiwombolo, pamene Angelo ati adzaweramtise mitu yawo, osadziwa za chomwe ife tikuchikamba. Chabwino, iwo sanayambe atayikapo. Iwo sakudziwa zimene ife tadutsamo. Ife tikudziwa chimene chimatanthauza kuti ukhale wotayika ndi kukhala utapezeka. O, kodi ife sitingakhoze kufuulira matamando Ake? Iye sali Mpulumutsi kwa iwo. Iwo sankasowa konse kupulumutsa kulikonse. Iye sanali Mchiritsi kwa iwo. Ayi. Ulemerero! Iye sali—Iye sali Moyo kwa iwo, ndithudi ayi, iwo sanafe konse mu tchimo ndi kulakwitsa. Ife tinali, koma tapangidwa kukhala amoyo. Pamenepo ife tiri. Kodi ife tidzanena chiyani titavula nduwira zathu, “Ndinu abusa *Akuti-ndi-akuti?*” O, ayi, ayi, ayi, ayi. Ulemerero wonse kwa Iye! Koma zimenezo. Apo inu muli. Ndiye ife tidzanena nkhani ya momwe ife tinagonjetsera, ife tidzamvetsa izo pang'ono ndi pang'ono.

<sup>268</sup> Ndiye, kumeneko mkati umo ndiye, ndiye nchiyani chinachitika? Kodi Mulungu ndiye anangoti, “Chabwino, Ine kulibwino mwina ndingowononga potashi Wanga yense ndi kashiamu, iye yense wawonongedwa?” Ayi, ayi, Iye ankadziwa kuti izo zikanadzakhala mwa njira imeneyo. Tsopano, tsopano, ngati Mzimu Woyera unandipanga ine chimene ine ndiri, ndipo ine ndimadya chakudya ndi kuchibwezeretsanso icho mu thupi langa ndi kumawumba ku chimene ine ndiri tsopano, tsopano, komabe, ine ndinapangidwa mwa mawonekedwe. Chithunzi chirichonse chimene Mulungu anachiwona, asanakhalepo maziko a dziko, chikukhwima, chikuwonekera. Mwaona? Icho chinabwera kuno kuchokera mwa mkazi, monga Iye anati icho chikanatero. Nthawi yotsatira icho chikubwera kuno kuchokera kwa Mulungu. Icho chinabwera nthawi imeneyo mwa mkazi; icho chikubwera nthawi iyi mwa Mwamuna. Mwaona? Chinabwera nthawi imeneyo mwa chikhumbo cha kugonana; icho chikubwera nthawi iyi mwa Mawu oyankhulidwa a Mulungu? Mwaona?

<sup>269</sup> Ndipo pamenepo, tsopano, kodi chirichonse sichingakhoze kundivulaza ine. Ayi, bwana. Palibe chinthu chimene chingakhoze kutivulaza ife. Monga Paulo ananena, “Palibe ngakhale zinthu zimene ziripo, zinthu zakudza, matenda, imfa, palibe kanthu kangakhoze kutilekanitsa ife kuti tichoke ku

chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu.” Palibe kanthu kangakhoze kutilekanitsa ife.

<sup>270</sup> Monga ine ndanenapo kankhani kakang’ono. Ine ndangotsala pafupi tsitsi lisanu kuti ndikhale wadazi, kwathunthu. Ndipo ine ndinali kulipesa lingapo ilo kuno nthawiyina kale, mkazi wanga anati, “Billy, ndiwe pafupifupi wa mutu wa dazi.”

Ine ndinati, “Koma ine sindinataye limodzi la ilo.”

Iye anati, “Liri kuti ilo?”

<sup>271</sup> Ine ndinati, “Kodi ilo linali kuti ine ndisanakhale nalo ilo? Mukuona, kulikonse kumene ilo linali ine ndisanakhale nalo ilo.” Tsopano, panali nthawi imodzi, zaka zana zapitazo, tsitsi ili panalibe apa nkomwe, koma ilo linali kunja kuno mu fumbi. Ndi kulondola uko? Ndiye pafupi zaka makumi asanu zapitazo, ilo linayamba kubwera pa mutu wanga. Ilo linkabwera kuchokera kuti? Kuchokera mu fumbi. Ndipo tsopano ilo likubwerera mmbuyo kumene ilo linali. Ndiko kulondola uko? Ilo panalibe, ndiye ilo linalipo, ndipo tsopano ilo palibe. Ndi chiyani icho? Ndi chiyani chimene chinalipanga ilo chimene ilo liri? Mulungu! Ndi Uyo apo. Iye anajambula chithunzi, ndipo umo ndi momwe ine ndikumufunira Iye.

<sup>272</sup> “O imfa, ili kuti mbola yako? Manda, chiri kuti chigonjetso chako?” Inu mukhoza kundikwilira ine limodzi la masiku awa nkuchoka kuno, ine sindikudziwa. Koma, m’bale, ine sindidzakhala wakufa. Ine ndikukuuzani inu zimenezo. Ayi, bwana. O, ife tidzauka, aleluya, ife tidzauka! Pa mmawa wa chiwukitsiro umenewo pamene zotchingira za imfa ziti zidzathyoke, ife tidzauka, aleluya, ife tidzauka. Palibe kanthu kangakhoze kundiletsa ine kuti ndiwuke. Palibe adierekezi okwanira mu gehena yonse amene angakhoze kundilepheretsa ine kuti ndiwuke. Palibe kanthu kokwanira kalikonse koti kandiletse ine kuwuka. Ine ndiri nalo lonjezo la Mulungu, ine ndiri nawo Mzimu Woyera. Ine ndiri naye Zoe, Moyo Wamuyaya wa Mulungu, ukupumula mkati umu. Chimtembo chakale ichi chinachokera kumeneko, ndipo Mulungu anandifungatira ine kuchokera mu nthaka.

<sup>273</sup> Ndipo ngati Iye Amene anandifungatira ine kuchokera mu nthaka, pamene ine ndakhala wa usinkhu tsopano, nthawi iliyonse ine ndinamva belu la mpingo, chinachake chimayankhula kwa ine, Liwu laling’ono ng’ono. Mngelo anayankhula kuchokera mu thengo, anati, “Usati udzamwe konse kapena kusuta, ine ndiri nayo ntchito yoti iwe udzayichite. Usati uwononge thupi lako kapena kuthamanga thamanga ndi akazi ndi zinthu, iwe, ine ndiri nacho chinachake kuti iwe udzachite pamene iwe udzafika pokulirapo.”

Ndinu Yani? Ndinu Yani?”

274 “Iwe udzadziwa zochuluka za izo patsogolo.” Patapita kanthawi, apa Iye akubwera, Iye akupachikika kutsidyako pa ubatizo. Iye akudziwonetsera Iyemwini. Iye akudzifotokoza Iyemwini. Iye akuyankha. Ine ndikumuwona Iye akuyima kutsidyako paliponse, pa dzanja lililonse.

275 Inu muchita motani, ngati Iye anandipanga ine chimene ine ndiri popanda kukhala nako kusankha kulikonse nkomwe? Ine sindinapite konse kumbuyo uko ndi kukanena, “Tsopano, Charlie Branham, inu mukakwatire Ella Harvey, ndi kundibala ine pa dziko lapansi.” Ayi, bwana. Ine sindinali nako konse kusankha kwa zimenezo. Mulungu anachita zimenezo. Ndipo ngati Iye anandipanga ine chimene ine ndiri, popanda kusankha, mochuluka bwanji pamene Mzimu Woyera umenewo uti upite kukafungatira pa ine ndipo ine ndinena, “Eya, Ambuye, Ndinu Mlengi wanga, ndipo ine ndimakukondani Inu ndipo ine ndikukuvomerani Inu ngati Mpulumutsi wanga.”

276 Inu mukanandigwirira ine chotani mu fumbi? Simungakhoze basi kuchita zimenezo, m’bale, simungakhoze basi kuchita zimenezo. Mulungu sanawumbe konse chidutswa chimodzi cha kashiamu uyu kapena potashi, kapena china chirichonse, chimene chikanadzakhala konse—kuti chitayidwe. “Onse amene Atate andipatsa Ine, maziko a dziko asanayikidwe, adzadza kwa Ine.” Whuuu! Ine ndikumverera ngati ndifuule pakali pano. “Onse amene Atate anandipatsa Ine adzadza kwa Ine, ndipo palibe mmodzi wa iwo ati adzatayike, koma Ine ndidzawawukitsa iwo kachiwiri mu chiwukitsiro. Ine ndinamumva Iye akuyitana, ndipo ine ndinabwera kwa Iye. Iwo angandisunge bwanji ine mu fumbi la dziko lapansi? Palibe oyika maliro okwanira mu dziko akanati andilayishire ine mu nkhope ndi fosholo, akanakhoza konse kundisunga ine mu fumbi la dziko lapansi. Ine ndidzawuka tsiku lina ndi kuyima mwa kufanana Naye, wotsukidwa mu Magazi Ake, wobadwa wa Mzimu Wake! Aleluya! Khalani nazoni zipembedzo zonse zimene inu mukuzifuna; ine nditenga Yesu. Amen!

277 Munthu wa inshuranse anabwera kwa ine, Wilbur Snyder, mzanga wabwino wa ine. Iye anati, “Billy, ine ndikufuna ndikugulitse iwe dongosolo la inshuranse.”

278 Ine ndinati, “Ine ndiri nayo kale iyo.” (Mkazi wanga anayang’ana pozungulira ngati kuti ati, “Ukunamira chiyani, mnyamata?”)

Anati, “Iwe uli nayo inshuranse?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Anati, “Ndi kampane yanji imeneyo? Ndi chiyani iyoyo?”

279 Ine ndinati, “Chitsimikizo chodala, Yesu ndi wanga, o, nkulawiratu bwanji kwa ulemerero Wauzimu! Wolowa wa chipulumutso, wogulidwa ndi Mulungu, wobadwa ndi Mzimu Wake, wotsukidwa mu Magazi Ake.”

280 Iye anati, “Izo ndi zabwino, Billy, koma iyo siyidzakuyika iwe kumanda.”

281 Koma ine ndinati, “Iyo idzanditurutsa ine kunjja.” Aleluya! Ine sindikudandaula za kulowa mkati umo; ndi kutuluka kunjja.

282 Kotero, ine ndiri nayo inshuranse imene imandiuza ine, “Ine ndidzabweretsa zonse zimene Atate andipatsa Ine, ndi Zanga.” Ine sindikusamala chimene adadi anga anachita, chimene amayi anga anachita, chimene chirichonse chinali. “Zonse zimene Atate andipatsa Ine zidzadza kwa Ine, ndipo palibe munthu angakhoze kubwera kupatula ngati Atate Anga amukoka iye.” Aleluya! Iye anawadziwiranji iwo? “Ine ndinawadziwiratu iwo maziko a dziko asanayikidwe. Pamene Ine ndinapha Mwanawankhosa, Ine ndinamupha iye limodzi ndi Iye.” Amen. “Ine ndinawukonzeratu Mpingo.” Nchiyani chimene chinakonzedweratu? Mpingo. Inu mumalowa bwanji mu Mpingo? “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwira kulowa mu Thupi limodzi.” Iye anadziwa maziko a dziko asanayikidwe kuti ife tikanadzakhala tiripo. Ndipo iwo amene Iye anawadziwiratu, Iye anawayitana. Iwo amene Iye wawayitana, Iye wawalungamitsa. Iwo amene Iye wawalungamitsa, Iye wawapatsa kale ulemerero.

283 Mu Mabuku a Mulungu Iye wanena kale kuti Iye adzakomana nane ine kumeneko komwe. Palibepo adierekezi onse ochokera ku gehena angakhoze konse kumuletsa iye pena paliponse koma kumuletsa iye kuti abwere kumeneko komwe, chifukwa Mulungu wanena kale chomwecho, ndipo izo zikukhazikitsa icho. Ngati zaka mabilioni zana dziko lisanawumbidwe nkomwe, nyenyezi za mmawa zinayimba limodzi ndipo ana aamuna a Mulungu anafuula mwa chisangalalo, nkuti kusanakhale maziko a dziko, onani, nkuti kusanakhale maziko. Ndipo Angelo amenewo ndi chirichonse chinali chokondwa, chikufuula za izo, nkuti kusanakhale maziko a dziko, Mdierekezi akanandisunga motani ine mu fumbi la dziko lapansi? Sangakhoze basi kuchita izo. Inu mukulondola.

284 Tiyeni tiwone, tsopano, ino ndi nthawi ya chidemokarase imene ine ndiri nayo mpaka pano. Iyi ili maminiti makumi awiri kuti ikwane ileveni, iyo ili maminiti makumi awiri okha kuti ikwane teni. Ndi kulondola uko, M’bale Wood? Ndiko kulondola, maminiti makumi awiri kuti ikwane teni. Aliyense akukondwa?

O, ine ndikumverera ngati ndiziyendabe,  
Ine ndikumverera ngati ndiziyendabe;  
Kwathu kwa mmwamba ndi kowala ndi  
kwabwino,  
Ndipo ndikumverera ngati ndiziyendabe.

O, ndikumverera ngati ndiziyendabe,  
 Ine ndikumverera ngati ndiziyendabe,  
 Kwathu kwa mmwamba ndi kowala ndi  
 kwabwino,  
 Ndipo ndikumverera ngati ndiziyendabe.

<sup>285</sup> Inu mumazikonda nyimbo zachikale izo monga imeneyo? Inalipo kalelo imodzi yachikale imene ife tinkakonda kuyiyimba, ya chinachake, yokhudza “*Chisomo ndi chifundo zinandipeza ine, pamenepo Nyenyezi ya Mmawa inawala*. Ndi iti imeneyo, Mlongo Gertie? Tiyeni tiwone. Momwe, ndi yotani imeneyo, M’bale Neville? Onani, inayake, “Chisomo ndi chifundo zinandipeza ine, pamenepo Nyenyezi Yowala ya mmawa Inawonetsa kokhalako kwake pozungulira ine.” U-nhu, eya. *Mu Mtanda*. Tipatseni ife poyambira pa iyo, mlongo. Ndiyo *Pafupi Ndi Mtanda*. Bwerani kuno. O, ine ndimakonda izi. Ndi angati amakonda nyimbo zakale zodzozedwa izo? Inu mukhoza kukhala nazo zanu zonse zodumphammmwamba-ndipansi kwasa-kwasa zimene inu mukuzifuna. Ndipatseni ine iyi, apa ndi pamene chisomo ndi chifundo zinandipeza ine. Ndi imeneyo. Chabwino, iyimbeni iyo tsopano.

Yesu, mundisunge pafupi ndi mtanda,  
 Pamenepo kasupe wofunika,  
 Waulere kwa onse, mtsinje wochiza,  
 Wochokera ku phiri la Kalvare.

Mu mtanda, mu mtanda,  
 Pakhale ulemerero wanga nthawizonse;  
 Mpaka moyo wanga wokwatulidwa udzapeze  
 Mpumulo kuseri kwa mtsinje.

<sup>286</sup> [M’bale Branham akuyamba kung’ung’uza *Pafupi Ndi Mtanda—Mkonzi*.] O, ndi zokongola bwanji! Taganizani za zimenezo! Bwanji ngati kukanati kukhale kopanda Mpulumutsi? Bwanji ngati ife tikanati tikhale opanda Mawu awa? Bwanji ngati Iye akanakhala asanakuyitaneni inu? Bwanji ngati Iye akanakhala asanakudziwirenitu inu, ndipo inu makanakhala kunja kuno mu dziko lonse ili usikuuno? Kodi inu mukumukonda Iye? O, mai! Musati muyiwale misonkhano mmawa, tsopano, pa hafu pasiti naini.

Mu mtanda, mu mtanda,  
 Mukhale ulemerero wanga nthawizonse;  
 Mpaka moyo wanga wokwatulidwa udzapeze  
 Mpumulo kuseri kwa mtsinje.

<sup>287</sup> Tsopano tipatseni ife poyambira pa *Malo Pa Kasupe*. Nyimbo yabwino yakale iyi, *Pali Malo Pa Kasupe*. Ndi angati amayidziwa iyo? “Malo, malo, inde, alipo malo, malo pa Kasupe.” Ndipo pamene inu muzichita izo tsopano, mwakachetechete kwenikweni, ingofikirani ku mbali ya inu, gwiranani chanza ndi mbale ameneyo. Inu mukudziwa, alipo



malo tsopano a Amethodisti onse, alipo malo a Abaptisti, alipo malo a Apentekoste. Alipo malo a onse ife tsopano, pa Kasupe. Ndi angati akuyidziwa nyimbo yakaleyo? O, zedi inu mukutero. Ena a inu a nthawi zakale tsopano, iyi ndi nyimbo yabwino yakale ya chi Kentucky tsopano.

Malo, malo, (tiyeni tigwirane chanza), inde,  
pali malo,  
Pali malo pa Kasupe a inu;  
Malo, malo, inde, pali malo,  
Pali malo pa Kasupe a inu.

O, malo, malo, pali malo ambiri,  
Pali malo pa Kasupe a inu;  
O, malo, malo, inde, pali malo,  
Pali malo pa Kasupe a inu.

<sup>288</sup> Tsopano, ine ndiri nacho chodzidzimutsa pang'ono kwa inu. Maulaliki onse aposachedwapa ndi mabuku ndi chirichonse zidzakhala pa malonda pa mapeto enawo a tchalitchi, sabata lamawa, pa misonkhano. Matepi ndi chirichonse, ndipo zonse mwa mawonekedwe abwino a zowerenga. Apo padzakhala tebulu kumbuyo uko kumbuyo mu chimodzi cha zipinda, ndi zowerenga, maulaliki aposachedwapa, ndi zina za zolembedwa zabwino zimene zinachitika mwapachiyambi mu mabuku atsopano, kulemba kwatsopano, zonse zidzayikidwa mu—mu kumapeto a nyumbayi Lachitatu likubwera ili usiku. Ndipo ife tikuyembekezera n—nthawi yabwino mwa Ambuye. Dzabwereni mukupemphera, tsopano. Tsopano, ayitaneni odwala anu ndi osautsika, alembereni iwo kalata ndipo afikitseni iwo muno, ndipo ife basi. . . Mulungu adzangosuntha mwamphamvu. Ife tiri pano ndipo tikudziwa kuti Iye adzachita izo tsopano.

<sup>289</sup> Ndipo tsopano ine ndapita kwa aliyense yemwe ine ndimamudziwa, kuti ali ndi kenakake kakang'ono. Ngati pali chinachake chasiya msewu tsopano, inu kumbukirani, ine ndinakuuzani inu kale nthawi yapitayo, kuti ife tipita kuti tikaziwongole izo. Ndipo ine ndikudziwa kuti inu mukudziwa kuti pali mzimu wosiyana pano kuposa umene unalipo. Mwaona? Mwaona? Mwaona? Ndiko kulondola. Tsopano, musati mulole kuti iwo uchokenso. Ine ndikukulumulirani inu pamaso pa Yesu Khristu, musati muwulole iwo kuti uchoke. Khalani pomwe pano ndi iwo, onani, ingosungani chirichonse chowongoledwa mpaka pansu ndi kumasuntha mopitirira basi. Inu muli abale. Si m'bale wanu konse kapena mlongo amene amachita chirichonse cholakwika, ndi mzimu wa Mdierekezi uwo umene umalowa mkati mmenemo. Onani, iye amapita mozungulira. Ndipo ingomumverani chisoni m'baleyo kapena mlongo, ndi kudziwa kuti ndi Satana yemwe akubwera pakati. Ndipo ngati inu muli nako kumverera kwina za izo, inu mukuchotse iko kuchoke mwa inu mwamsanga ndithu, inu mukuona, chifukwa iko

kudzakuwumitsani inu. Inde, iko kudzatero, koteru khalani kutali ndi izo. Ingokumbukirani.

Pali malo, malo, malo ambiri,  
Pali malo a Amethodisti, malo a Abaptisti,  
malo a Apresbateria, pali malo a onse;  
Malo, malo, inde, pali malo,  
Pali malo pa Kasupe a inu.

<sup>290</sup> Ndi angati akuyikumbukira nyimbo yathu yakale yobalalitsira, ija, “Tenga Dzina la Yesu ndi iwe, mwana wosawuka ndi wa tsoka; Ilo lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza iwe, ulitenge Ilo kulikonse kumene iwe upita?” Tikukhumba inu mukanakhala ndi ife, M’bale Jeffreys, inu ndi Mlongo Jeffreys, ndi anyamata kumeneko, ndi onse a iwo. Ndipo—ndiyeno, “Pa Dzina la Yesu kuwerama, kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake.” O, mai! “Mfumu ya mafumu Kumwamba ife tidzamuveka Iye korona, pamene ulendo wathu watsirizidwa. Tengani Dzina la Yesu ndi inu, litengeni Ilo ngati Chishango lero. O, pamene mayesero ayandikira pafupi, pumani Dzina Loyera ilo mu pemphero.” O, ine ndimakonda imeneyo, Dzina lodabwitsa limenelo la Yesu. Tsopano, tiyeni tiyime tsonga tsopano, pamene ife tikuyimba tsopano. Chabwino.

Tenga Dzina la Yesu ndi iwe,  
Mwana wosawuka ndi wa tsoka;  
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza iwe,  
Ulitenge ilo, ndiye, kulikonse kumene upita.


Dzina lofunika, O ndi lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha dziko ndi chisangalalo cha  
Kumwamba;  
Dzina lofunika, (O Dzina lofunika) O ndi  
lokoma bwanji!  
Chiyembekezo cha dziko ndi chisangalalo cha  
Kumwamba.

<sup>291</sup> Izi ndi zosiyana pang’ono tsopano. Tiyeni tingoweramitsa mitu yathu tsopano, ndipo mwakachetechete kwenikweni tiyeni tikweze dzanja limodzi, kumati:

Pa Dzina la Yesu kuwerama,  
Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,  
Mfumu ya mafumu Kumwamba, tidzamuveka  
Iye korona,  
Pamene ulendo wathu watsirizidwa.

Dzina lofunika (Dzina lofunika),  
O ndi lokoma bwanji! (O ndi lokoma bwanji!)  
Chiyembekezo cha dziko ndi chisangalalo cha  
Kumwamba;

Dzina lofunika (inde, Dzina lofunika),  
O ndi lokoma bwanji! (O ndi lokoma bwanji!)  
Chiyembekezo cha dziko ndi chisangalalo cha  
Kumwamba.

<sup>292</sup> Ndi mitu yathu yoweramitsidwa mopitirira, ife tikuti,  
[M'bale Branham akung'ung'uza, *Tenga Dzina la Yesu ndi iwe—*  
Mkonzi.] 

*NCHIFUKWA CHIYANI IFE SITIRI CHIPEMBEDZO?* CHA58-0927  
(Why Are We Not A Denomination?)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham woperekedwa mu Chingerezi Loweruka usika, Seputmbala 27, 1958, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©1996 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)